# DZIKO LOGARUKIRA MULUNGU

## Satana Akakamira Ulamuliro Wake

- Mngelo wakugwa aikidwa poyera ndi
- mlembi wa chikazi mu mbiri ya dziko
- yemwe mouziridwa ndi Mzimu analemba mabuku 50
- nachitiridwa umboni ndi
- masomphenya 2000 omwe onse akwanitsidwa molondora...
- osati ndi 50 koma ndi 100%

- Wanalemba za moyo wa thanzi
- pa za machiritso, maphunziro
- Asayansi zikuchitira umboni zonse
- Zinalembedwa zaka 125 zapitazo
- pomwe za sayansi/za machiritso
- zinali zongopenekera




### CHOMWE KABUKHU AKA KALEMBEDWERA

Bukhu la *Mkangano Waukuru (Great Controversy),* lolembedwa ndi Ellen G. White, lomwe kabukhu aka kali chifupikitso chake, liri kumasulira komveka bwino kwa mitu 12, 13, ndi 14 ya Bukhu la chibvumbulutso. Kuliwerenga bukhu'li momvetsetsa, zapezeka kuti maulosi omwe ali m'mitu itatuyo akukwaniritsidwa mogwirizana ndi momwe zinthu zakhala zikuchitikira pa dziko lapansi: Kabukhu'ka ndi chifupikitso cha zonse zimene Bukhu'li lazifotokoza komanso kupitiriza kuzilosera.

### *1. Momwe Uchimo Unalowera M'dziko Lapansi*

Ndi kobvuta kufotokoza za magwero enieni a tchimo monganso nkosatheka kufotokoza chifukwa chomwe linachitidwira. Bukhu Lopatulika likuphunzitsa momveka bwino ndi motsimikiza kuti Mulungu sanalenge kapena kutengapo gawo m'njira iri yonse za kulowa kwa tchimo m'dziko lapansi; kunalibe chosowa kapena kulephera kwa chilungamo ndi chiyero cha Mulungu pa kayendetsedwe ka boma lakumwamba, zomwe zikanapatsa mpata wa kuukira kwa mtundu uli wonse. Tchimo linadza monga chinthu chodzidzimutsa chimene malo ake panalibe pakati pa chilengedwe chonse, ndipo palibe chomwe chinaliyenereza kuti lipezeke kapena kukhalako; chikanapezeka chifukwacho, tchimo likanaleka kukhala chinthu choopsya ndi cha chinsinsi. Tanthauzo la tchimo ndi lomwe likupezeka m'Mau a Mulungu; "tchimo ndilo kusayeruzika." Lisanachitike tchimo panali mtendere ndi chimwemwe pakati pa chilengedwe chonse. Zinthu zonse zinamangika pamodzi mwa ngwiro monga mwa chifuniro cha Mlengi. Lamulo la chikondi linali maziko a boma la Mulungu, pomwe panakhazikikapo chimwemwe cha zolengedwa zonse. Mulungu sanaumirize chinthu chiri chonse kum'mvera Iye. Koma anapatsa ufulu wakusankha kumtumikira Iye kwa angelo ndi anthu koma osati mokakamiza.

Koma mngelo wina anagwiritsa ntchito ufulu unaperekedwawo molakwika. Tchimo linadza ndi ameneyo, yemwe anali wotsatira kwa Khristu pa ulamuliro, nabvekedwa ulemelero ndi ulemu waukuru ndi Mulungu, ndiponso kupatsidwa mphamvu zochuruka kuposa khamu lonse la za Kumwamba. Asanachimwe, Lusifara anali wamkuru wa a kerubi akuphimba, woyera ndi wopanda chirema. Akanapanda kuchimwa, Lusifara mwenzi ali chikhalire bwenzi la Mulungu, wokondedwa ndi kulemekezedwa ndi khamu lonse la angelo, nakhala chitsanzo cha kulemekeza Mlengi ndi mdalitso kwa angelo onse. Koma m'malo molimbikitsa zolengedwa zonse kukonda ndi kutumikira Mulungu, Lusifara anafuna kuti zimtumikire iye. Mtima wakuukira womwe unali mkati mwake unadzetsa chisokonekero m'mabwalo a Kumwamba. Uphungu wa Mulungu unayesetsa kumlangiza Lusifara. Mwana wa Mulungu anayesetsa kumuonetsera iye za ukuru, ubwino, ndi chilungamo cha Mlengi ndiponso kupatulika, kwa lamulo lake losasinthika. Koma kunyada ndi kudzifunira ukuru zinaudzadza mtima wa mngelo wa mkuruyo. "Chifukwa chiyani" anadzifunsa iye, "Khristu ali wamkuru? Chifukwa chiyani Iye akulemekezedwa kuposa Lusifara?"

Pomwepo Lusifara ananyamuka kuchoka pamaso pa Mulungu, kunka akusokoneza ndi kubweretsa mzimu wakuukira pakati pa angelo onse. Iye anayesetsa kudzutsa mwa angelo enawo mtima wakusakhutitsidwa ndi malamulo a Mulungu omwe anagwirizanitsa khamu lonse la Kumwamba, nafotokoza kuti malamulo a Mulunguyo anali ankhanza. Ndipo anakutchinjiriza kulakwa komwe anakuchitako kuti sikunali kuti iye anadzifunira ulamuliro, ukuru ndi ulemu, koma kuti amamenyera ufulu khamu ndi chilengedwe chonse cha za Kumwamba.

Modzala ndi chifundo chochuruka, Mulungu anamchitira chisoni Lusifara kwa nthawi yaitali. Moleza Iye anampatsabe Lusifarayo mpata wakuti alape ndi kubvomereza kulakwa kwakeko kuti Mulunguyo amkhululukire. Ndipo atafotokozedwa bwino kuti kusakhutitsidwa kwake kunalibe choonadi mkati mwake, Lusifara anabvomereza za tchimo lake, nalonjeza kukalifotokozera khamu la Kumwamba lonse za ili, ndi kuti walilapa. Koma kunyada ndi kudzikuza kunaumitsabe mtima wake nalephera iye kukwaniritsa lonjezano lake'lo pamaso pa Mulungu.

Kuyambira pamenepo mphamvu ndi nzeru zake zonse zinadetsedwa ndi bodza pakufuna kuti achitiridwe chisoni ndi angelo amene anawanamiza ndi kuwaika pansi pa ulamuliro wake. Iye ananka akulalikira kuti angelo onse amene anakana kupotozedwa ndi kukhala kumbali yake, ndiwo anali oukira Mulungu. Anakuyeretsa kulakwa kwake komwe anakuchitako pakunena kuti ndiko kunali chifuniro cha Mulungu. Kuyambira pomwepo iye anakhala akuyambitsa mikangano yosapindulitsa pakati pa angelo onse yopereka chikaiko za ungwiro wa chikhalidwe cha Mulungu.

Moleza mtima, Mulungu analora Satana kupitiriza kuukira kwakeko, kufikira kuipa kwake kufike poonekera ndi kutsimikizika ndi onse m'ntchito zooneka ndi maso. Mulungu analora ichi pofuna kuti nzeru zoipa za Lusifara zikule ndi kukhwima kuti kuipa kwake kuonekere ku chilengdwe chonse. Koma ngakhale anali ndi mphamvu yaikuru yosokeretsa, Lusifara anaichita iyi pobisalira m'bodza.

Lusifara anali kulemekezedwa ndi kuopedwa ndi angelo onse, kotero kuti palibe mngelo ndi m'modzi yemwe anayerekeza kufufuza za chinsinsi chomwe chinali m'mtima mwa mgelo wamkuruyo monganso kunali kobvuta kwa iye mwini, kuwafotokozera iwo za chomwe chinali cholinga cha kuukira kwake. Kufikira uchimo unakula msinkhu ndi kukhwima, palibe mngelo anamvetsetsa chenicheni chomwe unali. Angelo sanathe kuzindikira za kuopsya ndi chotsatira cha chakuukira lamulo la Mulungu. Iye anawanamiza iwo kuti cholinga chake pa zonse anachitazo chinali kufuna kulemekeza dzina la Mulungu, kubweretsa mtendere ndi kufunira ubwino boma ndiponso khamu lonse la Kumwamba.

Mulungu anagwiritsa ntchito chilungamo ndi choonadi kulimbana ndi tchimo linachitikalo. Koma Satana anagwiritsa ntchito zinthu zimene kunali kosatheka kuti Mulungu nkuzigwiritsa ntchito – chinyengo

ndi mau a utambwali. Mulungu anagwiritsa ntchito chilungamo pofuna kuonetsera ku miyamba ndi khamu lonse la Kumwamba kuti ulamuliro wake unali wa chiyero, ndi lamulo lake langwiro. Iye anamsiya dala Satana kuti kuipa kwake kukhale poyera.

Satana anaunamizira ulamuliro ndi lamulo la Mulungu kuti zinali za nkhanza, ndi kuti ndizo zinadzetsa chisokonekero Kumwamba. Koma kufikira lero, zotsatira za ntchito zake zikumdzudzula mwini yekha. Kuyambira pachiyambi iye wanakanitsitsa kuti cholinga chake sichinali kuukira. Koma pano chilengedwe chonse chikuchitira umboni kuti anaukira podzifunira mwini yekha ulemu ndi ukuru.

Ngakhale zinatsimikizika kuti Satana athamangitsidwe kuchoka Kumwamba, Mulungu sanamuononge iye. Ngati Mulungu akanatero nthawi yomweyo, chilengedwe chonse chikanamtumikira Iye chifukwa cha mantha osati kuchokera m'chikondi. Kuipa kwa wonyengayo sikunaonongedwe, kapena mzimu wakuukira kuthetsedwa. Tchimo linaloledwa kuti lifike pakuti silingathe kubisika.

Ntchito za Satana, ndi zotsatira zake pa munthu ndi angelo, zinasiyidwa kuti zionetsere kuipa kwa kunyalanyaza ndi kusasunga lamulo la Mulungu. Zinasiyidwa kuti zichitire umboni kuti ndi pakuchita chifuniro cha Mulungu momwe muli ubwino ndi umodzi



wa zinthu zonse zimene Mulunguyo anazilenga.

Pamene kunalengezedwa kuti Satana pamodzi ndi angelo ake achotsedwe kumwamba, iye anapsya mtima nalumbira kulimbana ndi lamulo la Mulungu kwa myaya. Pamenepo iye ananka akulengeza ndi kutenga ngati kuthamangitsidwa kwakeko unali umboni wokwanira kuti lamulo la Mulungu si la ufulu, ndipo nchifukwa anamenyera ufulu kuti alithetse. Mngelo wa mdimayu ndi onse amene anamtsatira anachotsedwa kumwamba ndi kuponyedwa pansi pano.

Mzimu womwewo unayambitsa kuukira kumwamba ukulimbikitsabe kupandukira Mulungu pa dziko lapansi lero. Monga anachitira Kumwamba, Satana ndi angelo ake akunka akuwafotokozera anthu kuti ali ndi ufulu wachibadwidwe choncho adzinka akuswa malamulo oletsa tchimo a Mulungu. M'malo mobvomereza ndi kulapa, angelo a mdimawo, akunka akulimbikitsa anthu kuukira Mulungu, kuzunza atumiki ake ndi kulalikira kuti Mulungu ndi amene analenga tchimo ndi kupangitsa Satanayo ndi angelo ake kuti alowe m'kulakwa ndi m'kumva zowawa zomwe ndi zotsatira za kusayeruzika kwaoko. Ndi mtima wake woukira Satana akunka akuliipitsa khalidwe la Mulungu monga anachitira Kumwamba ponena kuti Mulunguyo ndi wankhanza ndi wopanda chisoni, nalimbikitsa anthu kunka akuchimwirachimwira.

Chifukwa chimene Satana anachotsedwera m'mabwalo a Kumwamba, nchakuti Mulungu anafuna kuonetsa kupidwa kwake ndi kusayeruzika komanso kuonetsa chiyero ndi chilungamo ndi ungwiro wa ulamuliro wake. Ichi chinatsimikizika tsono pamene munthu anachimwa, kuti Mulungu anaonetsa chilungamo cha chikondi chake pakupatsa Mwana wake wobadwa yekha kudzafera mtundu wa anthu.

Kulimbana komwe kunachitika pakati pa Satana ndi Khristu, pa nthawi ya utumiki wa Mpulumutsiyo pa dziko lapansi pano, kunaliika poyera khalidwe loipitsitsa la wonyenga wamkuruyo.

Ndi Satana amene analitsogolera dziko lapansi kumkana Khristu. Ndi mphamvu zake zonse ndi machenjerero a ulamuliro wake wa mdima iye anafunitsitsa kumuononga Yesu. Wodzala ndi nsanje ndi udani wokhala ngati ng'anjo yotentha mu mphamvu yake, kuipidwa ndi mtima wa kufuna kubwezera, iye analitsogolera khamu lonse linasonkhana pa Gologotha kupfuula motsutsana ndi Mwana wa Mulungu pamene Kumwamba kunachitira umboni choopsya chimachitikacho mwakachetechete ndi modzazidwa ndi chisoni chachikuru. Yesu analibe banga liri lonse la uchimo lomwe likanampangitsa kumva zowawa. Kuzunzika kwake kunafika poipa kwambiri pa mtanda paja, pamene kudzipereka nsembe kwake kunakwaniritsa chomwe chinali cholinga chake; chifukwa chake Iye anapatsidwa dzina loposa maina onse.

Chokhacho kuti anafika pomkhomera Yesu pa mtanda, tchimo la Satana linafika pakuti silingakhululukidwenso. Khalidwe lake lokhala wabodza ndi wakupha linaonekera poyera. Iye ananka akufotokozera onse kuti kuukira lamulo la Mulungu kudzadzetsa ufulu ndi moyo wachipambano; koma tsopano zinaonekera kuti kuukirako kunadzetsa undende ndi kunyozedwa kwa moyo wa uzimu wa choonadi. Bodza la Satana ndi zoipa zonse zimene anazinena motsutsana ndi khalidwe ndiponso boma la Mulungu zinakhala poyera. Koma chilungamo cha Mulungu chinaonekera pakupulumutsa mtundu wa anthu kuti Mfumu mwini zonseyi inaikiratu nsembe yaikuru imene ndi chikondi chokha chomwe chikanatha kuipatsa. Khristu anadzichepetsa nakhala womvera kufikira imfa, nauononga uchimo pakutero.

Kumwamba konse kunachitira umboni za bvumbulutso la chilungamo chake, chomwe chinaonetsedwa pakupirira kunyozedwa ndi Satana ndiponso pa kupatsa chipulumutso kwa munthu. Chilango cha kuchimwira lamulo la Mulungu chanamgwera Iye amene anali wofanana ndi Mulungu. Pakutero munthu anapatsidwa ufulu wakuchilandira chilungamo cha Khristu kuti kudzera pakulapa ndi kudzichepetsa, iyenso agonjetse ndi kuilaka mphamvu ya Satana monga analakikira Mwana wa Mulungu.

Si kunali kufuna kudzaonetsera ku za moyo za pa dziko lapansi kokha za kufunikira kwa lamulo la Mulungu; koma kutsimikiziranso ku miyamba yonse kuti lamulo'lo ndi la myaya ndi losasinthika. Kukanakhala kuti zimene lamulo'lo linazinena zinali zoti nkusinthika, panalibe chifukwa chakuti Mwana wa Mulungu akanapereka moyo wake dipo la kusayeruzika komwe kunachitika motsutsana ndi lamulo'lo. Chilungamo ndi chifundo ndiwo maziko a lamulo pomwenso pakhazikikapo boma la Mulungu.

Pachiweruzo chotsiriza chinthu chiri chonse choyambitsa uchimo chidzaononongedwa. Pamene imfa ya Yesu pa mtanda pa Gologotha, ikulalikira umyaya ndi kusasinthika ndi kupatsa moyo kwa lamulo, iyi ikulalikiranso kuti mphotho yake ya uchimo ndi imfa. Choncho m'mau a Mpulumutsi akuti, "kwatha," pamene amapereka moyo wake, analinso kulalikira za kuonongedwa kwa myaya kwa Satana.

Chilengedwe chonse chidzachitira umboni za kuipa ndi chotsatira chake cha uchimo. Ndipo kuonongedwa kwa uchimo, womwe pachiyambi unachititsa mantha angelo ndi kudzetsa chitonzo pa Mulungu, kudzakhala chipambano cha chikondi cha Mulunguyo ndi maziko a ulemelero wake pamaso pa a moyo onse okhala m'miyamba yonse amene akukondwera kuchita chifuniro chake, ndipo lamulo lidzakhala chikhalire m'mitima mwao. Lamulo la Mulungu limene Satana anati ndi lopatsa ukapolo lidzalemekezedwa kuti ndi lamulo la ufulu.

## 2. Khristu Ananenera za Mtsogolo

"Pakuti masiku adzakudzera, ndipo adani ako adzakuzingira linga, nadzakuzungulira iwe kwete, nadzakutsekereza ponsepo; ndipo adzakupasula iwe, ndi ana ako mwa iwe; ndipo sadzasiya mwa iwe mwala wina pa mwala unzake; …." Luka 19:43-44.

Ophunzira anadzala ndi mantha nanthunthumira za ulosi wa kuonongedwa kwa kachisi, ndipo anafunitsitsa atamvetsa bwino za chimene Yesu anatanthauza m'mau ake'wo. "Mutiuze ife zija zidzaoneka liti? Ndipo chizindikiro cha kufika kwanu nchiyani, ndi cha mathedwe a nthawi ya pansi pano?"Mat. 24:23.

Khristu anaifotokoza momveka ndondomeko ya zochitika zikuruzikuru zomwe zidzachitike kumapeto a nthawi. Ulosi umene anaulankhula unali ndi matanthauzo m'magawo awiri: unanenera zakuonongedwa kwa Yerusalemu komwe kunachitika m'chaka cha A.D. 70, komanso za zoopsya zomwe zidzachitike pa tsiku lalikuru ndi lotsiriza. Kudzera pa zomwe zinali nkuchitika m'Yerusalemu, Khristu anakuona kuuma mtima ndi kupandukira Mulungu komanso kudza kwa msanga kwa chiweruzo ndi mkwiyo wa Mulungu. Poyang'ana kutsogolo za m'badwo unali nkudza, Iye analiona dziko lapansi liri m'kusayeruzika kosaneneka monga komwe pa nthawiyo kunatsogolera Yerusalemu ku chionongeko. Tchimo lalikuru la Ayuda linali lomkana Khristu; pamene tchimo lalikuru la akhristu a dziko lonse lapansi lero ndilo kukana Mau ndi Malamulo a Mulungu. Kudzera m'phunziro la chionongeko cha mzinda wosankhidwa'wo ife tingathe kuonamo chionongeko chachikuru chomwe chiri nkudza pa mizinda yonse ya dziko lapansi chifukwa chokana chifundo cha Mulungu ndi kulipondereza lamulo lake. Ndi chinthu choopsya kukana ndi kutsutsana ndi ulamuliro wa Kumwamba.

Tifune tisafune, tsiku la Mulungu liri nkudza koma modzidzimutsa kwa iwo osakhulupirira. Kuchokera pa phiri la Azitona Mpulumutsi anaona masauko omwe anali pafupi kuugwera mpingo wa nthawi ya atumwi: ndipo, kuposera apo diso lake linapyola kufikira ku za mtsogolo kwambiri, Iye anaona nthawi zowawitsa, za anamondwe oopsya a mabvuto omwe anali nkudza pa anthu onse omtsatira m'zaka za mdima komanso za chizunzo chachikuru chotsiriza.

Mphamvu za dziko lapansi ndi za mdima zinaturuka kulimbana ndi Khristu pakuzunza anthu omtsatira. Chizunzo chachikuru chinadza. Pansi pakuzunzidwa koopsyetsetsa, mboni za Yesu zinasunga chikhulupiriro osagwedezeka. Koma mphamvu za Satana zinalephera kuugonjetsa mpingo wa Khristu pogwiritsa ntchito machitidwe a nkhanza.

Anthu zikwizikwi anaponyedwa m'ndende ndi kuphedwa; koma ena anatengabe malo a ophedwa'wo. Chitsanzo cha moyo wao wachikhristu komanso imfa yao monga mboni zinali umboni wokwanira wa choonadi chimene chinali mwa iwo.

Kenaka Satana wanafuna njira zina zomenyera nkhondo yake yolimbana ndi boma la Mulungu mwachipambano; wanakhazikitsa mbendera yake mu mpingo wa Chikhristu.


Mdani wa miyoyo wamkuruyu wanagwiritsa ntchito njira ya mtendere koma yodzala ndi chinyengo mkati mwake m'malo mwa machitidwe a nkhanza amene anawagwiritsa ntchito pa chiyambi. Kuzunza oyera mtima kunalekeka, m'malo mwake machitidwe okhala ngati a mtendere koma ali a upandu kwambiri omwenso mkati mwake munali ulemelero ndi maulemu a dziko lapansi zinagwiritsidwa ntchito. Iye anauza okhulupirira kuti popeza mbali yake inasiya kuwachitira nkhanza, iwonso afewetsenso mbendera zina za choonadi chao.

Mpingo unalowa m'choopsya. Koma akhristu ena anaimabe pa choonadi, nakana kubvomereza cholakwika cha mtundu uli wonse ndi cholinga chakuti apeze ufulu m'njira ya uchimo. Koma ena anabvomereza kusinthanitsa choonadi ndiponso chikhulupiriro chao ndi chisalungamo.

Kenaka m'kupita kwa nthawi akhristu ambiri anagonjera natsitsako mbendera za chikhulipiriro chao ndi kulowa mu mgwirizano wapakati pa Chikhristu ndi chikunja. Utumiki wa Satana'wu unakakamira chipembedzo cha mafano pakuchotsa zinthunzithunzi za mafano a chikunja ndi kuika za anthu oyera

mtima a kale. Ziphunzitso zosamveka, kupembedza mizimu ya akufa, ndi zikondwerero za chikunja zinalowa kudzera mu mgwirizano wabodza'wo. Bukhu Lopatulika lomwe ndi muyeso woona wa Mau a Mulungu linakanidwa. Chiphunzitso cha mau ndi lamulo la Mulungu chinanenedwa kuti nkupandukira.

Pambuyo pa kulimbana koopsya, kwa nthawi yaitali, okhulupirira owerengeka anaganiza zothetsa mgwirizano wao ndi mpingo unapandukira Mulungu'wo. Iwo anaona kuti ngati cholinga chao chinalidi kuti atsatire Mau a Mulungu moyenera, kunali kofunika kupatukana ndi chipembedzo cha mafano'cho. Iwo anakanitsitsa kubvomereza



chosalungama chiri chonse.

Mtumwi Paulo, m'kalata wake wachiwiri ku Atesalonika, analosera za kupandukira Mulungu komwe kunachitikaku ndipo m'nthawi yake kunali mtsogolo ndipo chotsatira chake chinakhala kukhazikitsidwa kwa ulamuliro wophatikiza za ndale ndi zachipembedzo (upapa). Iye anafotokoza kuti lisanafike tsiku la kudza kwa Khristu, "chiyambe chifike chipatukocho, nabvumbulutsidwe munthu wosayeruzika, mwana wachionongeko." *2 Ates. 2:3.*

Pang'ono ndi pang'ono, mwakachetechete ndi monyengerera, kenaka modzionetsera, miyambo ya chikunja inalowa mu mpingo wa Chikhristu. Kuzunza oyera mtima kunalekeka, ndipo chikhristu chinakhala chipembedzo chobvomerezeka m'mabwalo a milandu ndi m'nyumba za chifumu, ndipo mpingo unayamba kusiya machitidwe ake akudzichepetsa monga mwa khalidwe la Khristu ndi atumwi ake, nuyamba kudzitukumula ndi kunyada komanso kutengera makhalidwe a ansembe ndi a olamulira a chikunja; ndipo m'malo mwa malamulo a Mulungu, unaika maphunzitso ndi miyambo ya anthu. Kuyambira pomwepo makhalidwe achikunja ananka akukulirakulira. M'malo mwakuti chikhristu chigonjetse chikunja, ndi chikunja chomwe chinagonjetsa chikhristu.

Kulolerana kwa pakati pa chikunja ndi Chikhristu kunabala mchitidwe wotchedwa "munhtu wakusayeruzika" monga zinanenedwera mu ulosi.

Ulosi unanenera kuti machitidwe a upapa adzayesetsa, "kusintha nthawizo ndi chilamulo." Kupembedza mafano ndi anthu akufa zinalowa pang'ono ndi pang'ono m'chipembedzo cha Chikhristu. Komanso mpingo wa Aroma unayesetsanso kuchotsa lamulo lachiwiri la malamulo khumi lomwe likuletsa kupembedza mafano, ndi kuligawa lamulo la khumi pawiri pofuna kukwaniritsabe chiwerengero cha malamulo khumi monga chiri m'Bukhu Lopatulika.

Satana wanayesetsanso kulifafaniza lamulo la chinai, nafunitsitsa kulichotsa Sabata la chilengedwe ndi kuika m'malo mwake tsiku lomwe anthu achikunja anapembedza dzuwa, - "tsiku lolemekezeka lopembedza dzuwa." Pakufuna kuonetsetsa kuti akhristu ambiri alibvomereza ndi kulilemekeza tsiku la dzuwa'li, iye anadzetsa chiphunzitso cha bodza chakuti tsiku loyamba la pa mlungu'li linakhala la sabata chifukwa chakuti ndi lomwe Khristu anauka kwa akufa. Ndipo Sabata loona la chilengedwe analiipitsa kuti ndi la Sabata la Chiyuda.

M'zaka za pakati pa 300 mpaka 400 [A.D. 321], mfumu Konstantini inalamulira kuti Sunday lidzikhala tsiku lakupumula kwa anthu onse okhala mu ufumu wa Aroma. Chinali cholakalaka cha mfumuyi kuti ilunzanitse anthu achikunja ndi akhristu. Iye anachita ichi polangizidwa ndi aepisikopi a mpingo. Koma ngakhale pang'ono ndi pang'ono akhristu anapotozedwa kuti adziliona Sunday ngati loyera, ambiri a iwo anasungabe Sabata loona la tsiku la chisanu ndi chiwiri monga lopatulika la Ambuye, napitiriza kulilemekeza monga mwa lamulo la chinai la malamulo khumi.

Misonkhano yambiri inakhala ikuchitika momwe atsogoleri a mpingo kuchokera ku dziko lonse lapansi anakomana. Mu msonkhano uli wonse, Sabata la Mulungu woona linakhala likuponderezedwa, pamene Sunday linanka likukwezedwa.

Munthu wakusayeruzikayu wayesetsadi kusintha lamulo lokhalo lomwe likulozera mtundu wonse wa anthu kwa Mulungu wamoyo. Mu lamulo lachinai la malamulo khumi [Eksodo 20:8-11], Mulungu akudzifotokozedwa kuti ali Mlengi. Koma Satana akuyesetsa kuwapotoza anthu kuti asalemekeze Mulungu pakulisunga lamulo lake'li, choncho ndi mphamvu zake zonse wakuwapangitsa iwo kunyansidwa ndi lamulo lomwe likufotokoza momveka bwino kuti Mulungu ali Mlengi'li. Pano ngakhale a mipingo ya Mpanduko akumaphunzitsanso kuti chifukwa chakuti Khristu anauka kwa akufa pa tsiku la Sunday, Iye analipanga ili kukhala sabata la Chikhristu. Koma palibe umboni uli wonse m'Bukhu Lopatulika wotsimikizira kuti Khristu ndiponso ophunzira ake anayamba alilemekeza Sunday kuti ndi la sabata. M'zaka zapakati pa 500 ndi 600 [A.D. 538] mchitidwe wa upapa unali utakhazikika ndithu. Ulamuliro wa chikunja wa ufumu wa Aroma unapatsa mphamvu ku mchitidwe wa upapa. Chizunzo cha anthu oyera mtima chinachitidwa mwa nkhanza yaikuru ndiponso mu mkwiyo umene sunachitikepo kuyambira kale; dziko lapansi linakhala bwalo lalikuru lochitirako nkhondo. Kwa zaka mazana anai mpingo wa Khristu unakhala wothawathawa ndi wobisalabisala.

Kukhala pa ulamuliro wophatikitiza ndale ndi za chipembedzo kwa mpingo wa Aroma kunali chiyambi cha zaka za mdima wa uzimu. Chikhulupiriro chinachotsedwa pakudalira Khristu yemwe ndi maziko a choonadi ndi kuikidwa pa papa. M'malo modalira pa Mwana wa Mulungu kuti ndiye ali ndi mphamvu yakukhululukira machimo ndiponso ya kupulumutsa kuloza ku moyo wosatha, anthu anayang'ana kwa papa ndiponso ansembe ndi gulu lao. Umu ndimo malingaliro a anthu anapotozedwera kuchoka kwa Mulungu ndi kupititsidwa kwa munthu amene ndi wakugwa, wokhala ndi ufooko komanso woipa mtima; ndiponso kwa kalonga wa ulamuliro wa za mdima (Satana), amene papayo pamodzi ndi ansembe ake akumtumikira. Uchimo waphimbidwa m'machitidwe ngati a chipembedzo choona. Paliponse pamene Mau a Mulungu amaponderezedwa, ndipo munthu amadzikweza pamwamba pa awa, chisalungamo, chinyengo ndi mdima wa bi wa uchimo zimatsatira.

Chimodzi cha zifukwa zimene zinapangitsa kuti mpingo wa choonadi udzilekanitse ndi mpingo wa Aroma chinali udani ndi upandu umene mpingo wa Aromawo uli nawo pa Sabata la m'Bukhu Lopatulika. Lamulo la Mulungu linaponderezedwa m'matope, pamene lamulo la miyambo ndi maphunzitso a anthu linakwezedwa. Ndi pambuyo podzilekanitsa ndi mphamvu ya ulamuliro wa mpingo wa Aroma kuti anthu anayambanso kusunga lamulo la Mulungu mwa ufulu.

## *3. A Waldense, Wycliffe ndi Huss*

Mkati mwa mdima wa uzimu umene unaliphimba dziko lapansi kwa nthawi yaitali ya ulamuliro wa utsogoleri wa mpingo wa Aroma, kuunika kwa choonadi sikunazimiretu. Mu m'badwo uli wonse mumakhala mboni zokhulupirika za Mulungu, - amuna oona mtima amene samagwedera chikhulupiriro chao pa Khristu amene ndi Nkhoswe yokhayo ya pakati pa Mulungu ndi munthu; anthu omwe amalitenga Bukhu Lopatulika kukhala lamulo lokhalo la moyo wao, ndi kulilemekeza Sabata loona.

M'maiko a m'katikati ku Ulaya omwe anali kunja kwa ulamuliro wa Aroma, kwa zaka zambiri munakhala magulu a akhristu amene sanalumikizanepo konse ndi machitidwe achikunja a utsogoleri wa mpingo wa Aroma. Anthu a mtundu wa chi - Waldanse anali amodzi a magulu amenewo. Ngakhale asilikari ankhondo anatumizidwa kulimbana nao, komanso ambiri kuphedwa mopanda chisoni, anthu'wo anapitiriza kutumiza anthu ogwira ntchito ya kunka akufalitsa uthenga wa choonadi. Iwo anali maziko a ntchito ya Kukonzanso imene inaonekera poyera mu nthawi ya Wycliffe, ndi kukula komanso kumera mizu m'masiku a Luther, ndipo idzakhala ikupitabe chitsogolo kufikira nthawi yachimaliziro.

Isanafike nthawi ya Kukonzanso Bukhu Lopatulika limapezeka mwa apo ndi apo ndipo sikunali kwapafupi kuti munthu alipeze; koma Mulungu sanalore kuti Mau ake aonongedwe ndi kusoweratu.. Choonadi chake sichinali chakuti chibisidwe kwa myaya. M'maiko osiyanasiyana a ku Ulaya, anthu ena anachifufuza choonadi monga chimafufuzidwira chuma chobisika. Motsogozedwa ndi mphamvu ya Mulungu anawapeza Malembo oyera'wo, nawawerenga tsamba liri lonse moikapo mtima.

Kupatula kwa anthu a mtundu wa chi-Waldanse, kwa zaka zambiri Mau a Mulungu anakhala obisika kwa anthu amitundu ina chifukwa analembedwa m'chilankhulo chodziwika ndi anthu ophunzira okha; koma pano nthawi inakwana yakuti Mau'wo amasuliridwe ndi kupatsidwa kwa anthu a m'maiko osiyana m'zilankhulo zao.

M'zaka za pakati pa 1300 ndi 1400 munauka m'dziko la Angelezi, "Nthanda, Nyenyezi ya Mbandakucha ya Kukonzanso." Yohane Wycliffe anali mkupamame wa ntchito ya kukonzanso, osati wa Angelezi okha, koma wa chipembedzo chonse cha Chikhristu.

Pamene Wycliffe anali ku sukulu ya ukachenjede, anayamba kuwerenga Mau a Mulungu ndi chidwi chachikuru. Pamene chidziwitso chake chinafika pozikika, iye anayamba kufufuza mwakuya za Mau'wo monga akanachitira munthu ali yense wa maphunziro a pamwamba.

Monga anthu okonzanso amene anadza pambuyo pake, Wycliffe sanazindikire kumene ntchito anaichitayo imamtsogolera. Sichinali cholinga chake kuti akazindikira atsutsane ndi atsogoleri a mpingo wa Aroma. Koma chikondi chake cha choonadi ndicho chinamkakamiza kuti alimbane ndi ziphunzitso zabodza zomwe mpingo'wo unadzibweretsa. Iye anakhala ndi moyo ndi cholinga chakuti apatse m'manja mwa anthu a mtundu wake chida cha mphamvu choposa zida zonse chomwe anthuwo achigwiritse ntchito kutsutsana ndi mpingo wa Aroma; anafuna kuwapatsa iwo Bukhu Lopatulika. Potsirizira - Bukhu Lopatulika loyamba kumasulidwa m'Chingelezi linatsirizidwa. Mau a Mulungu anatseguka m' England.

Makina osindikiza mabuku asanaturukiridwe, mabuku amalembedwa pa manja, ntchito yomwe inali yotopetsa ndi kutenga nthawi yaitali kuti ichitike ndipo ichi chinachedwetsa kuti Bukhu Lopatulika lifalikire kwa anthu ambiri. Pomwepo Wycliffe anayamba kuphunzitsa ziphunzitso zomwe pambuyo pake zinatchedwa za Mpanduko (Protestantism), - zakuti chipulumutso chidalira pa kukhulupirira Khristu ndi Mau osasinthika a Mulungu. Mulungu anaipereka ntchito yake kwa Wycliffe. Iye anaika Mau ake'wo mkamwa mwa Wycliffe, ndi kumtsogolera ndi Mzimu wake kuti afalitse Mau'wo kwa anthu onse.

Wycliffe anawalandira Malemba Oyera ndi mtima wake wonse kuti anali Mau ouziridwa ndi Mzimu wa Mulungu, ndi kuti ndi Mzimu Woyerayo yemwe anali ndi mphamvu yowamasulira kuti munthu wowerenga ziphunzitso zochokera m'menemo azindikire za undindo wa utumiki wake.

Kunali kudzera m'zolembera za Wycliffe kuti Yohane Huss, wa ku Bohemiya, anatseguka maso nayamba kuzikana ziphunzitso za chikunja za mpingo wa Aroma. Ndi kudzera m'maiko awiriwa omwe analekanitsidwa ndi machitidwe a mpingo wa Aroma kuti mbeu ya choonadi inabzalidwa.

Kuchokera ku Bohemiya ntchitoyi inafalikira ku maiko ena. Dzanja la Mulungu linali kukonzetsera ntchito Yaikuru ya Kukonzanso yomwe inali patsogolo.

Uthenga Wabwino unabzalidwa m'Bohemiya m'zaka zoyambirira za pakati pa 1300 ndi 1400. Bukhu Lopatulika linamasuliridwa, ndipo mapemphero anachitidwa m'chilankhulo cha anthu a m'dziko'lo. Huss anakwezedwa pa udindo wa mphunzitsi wamkuru ndi mkuru woyang'anira pa sukulu ya za Ukachenjede ya dziko'lo.

Chifukwa cha udindo umene analandira, maganizo a Huss anagawika ndi kulimbana kwakuru mkati mwake. Ngakhale mpingo wa Aroma unafuna kumchotsa ndi kumzunza, iye anakhalabe chiwalo chake, nalemekezabe ulamuliro wa mpingowo. Ichi chinadzetsa kulimbana kwakuru pakati pa choonadi chimene iye anachizindikira chomwenso chinali cholakalaka cha chikumbumtima chake. Ngati utsogoleri wa mpingo wa Aroma unali wosachimwa monga iye anakhala akukhulupirira, nanga ndi chifukwa ninji iye anakakamizidwa kusaumvera? Ichi chinamtsogolera iye kuwatenga Malembo Oyera kukhala nyali ya kumapazi ake ndi muuni wa pa njira yake ndipo anawalalikira Mau'wo kwa anthu ena kuti akhalenso chowaunikira, ndi kulamulira mitima yao; kuti azindikire kuti Mulungu amene analankhula m'Bukhu Lopatulika, osati kudzera mu mpingo ndi ansembe ndi Iye yekhayo anali Wolungama ndi Mtsogozi.

## *4. Luther ndi Kukonzanso Uzimu Woyenera ku Germany*

Mwa onse ndi Martin Luther anaitanidwa kuutsogolera mpingo kuturuka mu mdima wa chikunja cha ziphunzitso za Aroma ndi kulowanso m'kuunika kwa choonadi cha Bukhu Lopatulika. Modzara ndi changu, kulimbika mtima ndi kudzipereka nsembe, komanso kusachita mantha ndi munthu aliyense koma kuopa Mulungu yekha, ndipo mosakhulupiriranso maziko ena a chikhulupiriro koma Malembo Oyera, Luther anakhala ngwazi ya choonadi ya m'nthawi yake. Tsiku lina iye anali kusanthura mabuku m'nyumba yowerengeramo mabuku ya sukulu ya za ukachenjede, pamene anaturukira Bukhu Lopatulika lolembedwa m'chi - Latini.

Nthawi iri yonse yakupumulira pa ntchito zake za tsiku ndi tsiku iye anadzipereka kwatunthu kuliwerenga Bukhu Lopatulika'lo. Iye sanataye nthawi kuwerenga mabuku wamba koma anaika mtima wake wonse pa kuwerenga Mau a Mulungu'wo.

Monga njira imodzi yopezera ndalama zomangira nyumba yopemphereramo ya Petro Woyera ku Vatikani, dzikalata za chikhululukiro cha machimo, zinalembedwa ndi kugulitsidwa kwa anthu onse mobvomerezedwa ndi Papa. Munthu amene anapatsidwa ntchito yogulitsa dzikalata'zi m' dziko la Germany amatchedwa Tetzel. Koma kunafunikira kuti izi zisanayambe kugulitsidwa zifotokozedwe kwa anthu anasonkhana'wo m'nyumba yopemphereramo; ndipo Tetzel, atakwera pa gome analalikira, moyamikira dzikalata za uchimo'zo kuti zinali mphatso yamtengo wapatali yochokera kwa Mulungu. Iye anapitiriza kufotokoza kuti dzikalata zimenezi zinali zakuti munthu akazigula, ndiye kuti iye pamodzi ndi abale ake amene anafa kale machimo ao amakhululukidwa komanso kuti machimo omwe munthu wa moyo'yo adzawachita mtsogolo adzakhala akukhululukidwabe. Panalibe wansembe ndi m'modzi yemwe amene anaturutsa liu kutsutsa chinthu cha uchimo chinanenedwa'cho. Koma ngakhale zinthu zinakhala choncho, mitima ya anthu inabvutika ndi kukhala yosakhutitsidwa, ndipo ambiri anagwada maondo ao pansi kupempha Mulungu kuti achitepo kanthu kuti mpingo wake uyeretsedwenso.

Pamenepo Luther monga ngwazi ya choonadi anailowa ntchito yake molimba mtima. Nalalikira kuchokera pa guwa la ulaliki mau akutsutsa ndi kuchenjeza za tchimo'li. Iye anafotokoza kuti palibe njira ina koma kulapa ndi kubwerera kwa Mulungu ndi kukhala ndi chikhulupiriro mwa Khristu ndi machitidwe okhawo munthu wochimwa angampulumutsidwe nao. Chisomo cha Yesu sichinali chakuti munthu nkuchigula ndi ndalama; ndi mphatso ya ulere.

Pamene Tetzel anapitiriza kulalikira ndi kuchita ntchito yake ya chinyengoyo, Luther anapitiriza kutsutsa mwamphamvu maulaliki achikunjawo. Pa [October 31, 1517], Luther analowerera m'kati mwa magulu a anthu omwe amapita ku nyumba yopemphererako, nakhoma pa chitseko cha nyumbayo chikalata pomwe analembapo mpfundo makumi asanu ndi anai mphambu zisanu zotsutsa chiphunzitso cha dzikalata za chikhululukiro cha machimozo. Mpfundo zomwe iye anazilembazo zinagwira mtima anthu ambiri. Kuchokera pamenepo anthu ambiri anayamba kuzindikira kuti mphamvu yakukhululukira machimo sinapatsidwa kwa Papa kapena munthu wina ali yense.

Chiphunzitso cha Luther'chi chinakopa chidwi cha anthu ambiri olingirira zinthu mwakuya m'dziko lonse la Germany. Chikhulupiriro cha moyo chinayamba kutenga malo a chipembedzo chakufa ndi chochitidwa mwa miyambo chimene mpingo unachilandira ndi kuchigwiritsa ntchito kwa nthawi yaitali. Anthu ambiri anasiya kukhulupirira ziphunzitso za chikunja za Chiroma.

Luther anachita mantha podziona kuti anali yekha; munthu m'modzi, iye anatsutsana ndi mphamvu ndi maukuru za dziko lapansi. Pamene anayamba kufooka chifukwa cha manthawo, iye anayang'ana kwa Mulungu, nadalira pa chitchinjirizo cha ngwiro cha dzanja la Mwini mphamvu zonse.

Panali choonadi cha nthawi zonse mu nthawi ya Luther, - choonadi cha mtengo wapatali cha nthawi yoikika; palinso choonadi cha nthawi zonse ku mpingo lero lino. Mulungu amene anachita zinthu zonse molingana ndi chifuniro chake wakhala akulora anthu ake kudutsa mayesero osiyanasiyana, ndi kuwazindikiritsa iwo za ntchito imene anawaitanira kuti aichite mwachipambano. Monga zinachitikira kale, nkutheka anthu kutsatira maphunzitso ndi miyambo ya umunthu m'malo mwa Mau a Mulungu.

Kukonzanso kwa uzimu wabwino mu za Kumwamba sikunathere pa Luther monga amaganizira anthu ambiri. Uku kukupitirirabe ndipo kudzafikira ku chimaliziro cha dziko lapansi. Kuyambira nthawiyo kufikira lero, kuunika kwatsopano kwakhala kukuwala mosalekeza pa Mau a Mulungu ndipo ziphunzitso za choonadi zakhala zikubvumbulutsidwa tsiku ndi tsiku.

## *5. Wokonzanso Uzimu Woyenera wa ku Swirtzerland*

Pa kasankhidwe ka antchito ochita ntchito yakukonzanso mpingo, mphamvu yotsogolera ya umulungu inaonekera monga zinachitikira mu nthawi yakukhazikitsa mpingo'wo mu nthawi ya atumwi. Khristu anasiya osasankha anthu otchuka ndi odziwika a dziko lapansi, amaudindo ndi olemera, iwo amene anazolowera kuyamikiridwa ndi kugwadiridwa pokhala iwo atsogoleri a anthu. Zinachitikanso chomwecho mu thawi ya kukonzanso.

Atangobadwa Luther, panadutsa milungu yowerengeka, nabadwanso Ulric Zwingli, m'banja la mbusa wina m'kachipinda komwenso kanali nyumba yokhalamo, m' Saxony, mkati mwa mapiri a Alps. Mnyamatayu sanakhalitse nthawi yaitali m'chigwa chomwe anthu a mtundu wake anakhalako. Iye anadza ku Basil [1502-1506] kumene anayamba maphunziro ake. Kunali ku Basil komwe Zwingli kwa nthawi yoyamba anamva uthenga wabwino wa chisomo choperekedwa mwa ulere cha Mulungu. Posakhalitsa iye anaitanidwa kuchoka ku Basil, ndi kukayamba kugwira ntchito ya moyo wake wonse. Malo oyambira ntchito yake anali chigawo china chake cha mpingo chomwe chimatchedwa Alpine. Pamene iye anapitiriza kuzama m'Mau a Mulungu, anapitirizanso kuturukira za kusiyana komwe kunalipo pakati pa choonadi cha m'Mau'wo ndi ziphunzitso zosokeretsa za mpingo wa Aroma. Iye anadzipereka ndi mtima wake wonse kuliwerenga Bukhu Lopatulika lomwe anatsimikizika kotheratu kuti liri Mau a Mulungu ndi lamulo langwiro ndi losasinthika. Pakutero anaturukiranso kuti Bukhu Lopatulika'lo limadzitanthauzira lokha. Kuyambira pomwepo iye sanaligwiritse ntchito Bukhu Lopatulika pofuna kutchinjiriza chiphunzitso chiri chonse cha umunthu, koma anatenga nthawi yake yaitali kuliphunzira kuti alimvetsetse bwino.

"Pamene ndinayamba kudzipereka kwatunthu ku Mau a Mulungu, chikondi cha nzeru za dziko lapansi ndi kumfunamfuna Mulungu pogwiritsa ntchito nzeru za umunthu zinakhala zikulimbana mkati mwanga. Kumapeto kwake, ndinafika pakuganiza, 'Uyenera kutaya bodza liri lonse, ndi kuphunzira tanthauzo la chiyero chenicheni cha Mulungu kudzera m'Mau ake osabvuta kuwamvetsawo.'"

Chiphunzitso chimene Zwingli anachilalikira sichinachokere kwa Luther. Chinali cha Khristu.

Chidwi cha anthu chinadzutsidwa ndi choonadi chimene Zwingli anachiphunzitsa; ndipo anthu anakhamukira kukamvetsera ku ulaliki wake. Ambiri a iwo amene anasiya kale osapitanso kukapembedza ku nyumba zopemphererako anali pakati pa anthu amene anapita kukamvetsera mlalikiyo. Monga anachitira ku Einsiedeln, Zwingli analalikira kuti ndi Mau a Mulungu okhawo anali ndi mphamvu yosasinthika, ndi kuti imfa ya Khristu inali nsembe yokhayo yangwiro. Iye sanangolalikira za chipulumutso chaulere chimene chinapatsidwa ku mtundu wa anthu, komanso mopanda mantha anadzudzula machimo amene anachitidwa pa nthawiyo. Ngakhale poyambirira uthenga wake unalandiridwa ndi chimwemwe, kumapeto kwake unapezana ndi chitsutso chachikuru.

Kukanitsitsa kulolera ziphunzitso zolakwika kwa ku Spires [April 19, 1525] ndi kusabvomerezanso izi kwa ku Augsburg [June 25, 1530], ndi chipambano chakukonzanso m'dziko la Germany, zinatsatidwa ndi zaka za mkangano ndi mdima. Anthu olimbana ndi mphamvu yomwe inatsogolera ntchito ya kukonzanso anaoneka ngati akupambana. Koma mwadzidzidzi ndi mosayembekezeka zinthu zinasintha, mfumu ya dziko'lo inagonjetsedwa. Iye anaona anthu analimbana nawo'wo akumasuka kuchoka m'manja mwake, ndipo iye anakakamizidwa kubvomereza ziphunzitso zomwe cholakalaka chake chinali kuzipondereza. Charles V analimbana ndikusutsana ndi mphamvu ya Wosaonekayo.



M'dziko la Switzerland monganso zinachitikira m'Germany kunadzanso masiku a mdima kumbali ya magulu a Kukonzanso. Pamene ambiri a ansembe anabvomereza za chikhulupiriro chakukonzanso, ena anakakamira mosadziwa ku ziphunzitso zosokonekera za mpingo. Kuzunzidwa kwa anthu amene anasankha kutsatira choonadi kunadzetsa nkhondo ya pachiweniweni. Ndipo mpingo wa Aroma unagonjetsa nukhalanso wa mphamvu m'malo ambiri omwe anthu anaupandukira. Koma Mulungu amene maweruzo ake ndi ochokera ku nthawi za myaya anapitiriza kukhala kumbali ya anthu ake.

## *6. Okonzanso a Chingelezi*

Pamene Luther anali nkutsegula Bukhu Lopatulika linatsekedwa'lo kwa anthu a ku Germany, [William] Tyndale motumidwa ndi Mzimu wa Mulungu anachitanso chimodzimodzi ku dziko la England.

Pakuyankhapo pa bodza la anthu onse amene amatsatira ziphunzitso za papa kuti mpingo wa Aroma ndiwo unali ndi mphamvu pa Bukhu Lopatulika, choncho ndi wokhawo

womwe unali ndi mphamvu ya kulimasulira, Tyndale anati, "Mungandiuze za Iye amene anaphunzitsa mphungu kugudukira chakudya chake? Mulungu ndi amene amaphunzitsa ana ake akumva njara ndi ludzu lakumfuna Iye kuti ampeze Atate wao kudzera m'Mau ake. Maulaliki a Tyndale anadzutsa chilakolako chachikuru cha uzimu; anthu ambiri anachilandira choonadi. Koma ansembe anakhala tcheru kotero kuti pongotsiriza iye kulalikira, iwo anayesetsa kukhotetsa ndi kuinongeratu ntchito yake. Ha! Ngati akhristu akanakhala ndi Bukhu Lopatulika lomasulidwa m'zilankhulo zao, akanatha kudziwerengera okha ndi kulimbana ndi ziphunzitso zosayenera'zo. Popanda Bukhu Lopatulika kunali kobvuta kuwakhazikitsa okhulupirira omwe sanali ansembe m'choonadi." Kuwala kwa tsopano kunaudzadza mtima wa Tyndale.

Sipanapite nthawi yaitali kuchokera pamenepo, m'modzi wa anthu ophunzira kwambiri wa mpingo wa Chikatolika anaimirira kutsutsana ndi Tyndale pakunena, "Kuli bwino kukhala wopanda lamulo la Mulungu kuposa kukhala opanda papa." Ndipo ku mau awa Tyndale anayankha, "Ndikumkana papa ndi malamulo ake onse; ndipo ngati Mulungu angausunge moyo wanga kwa zaka zochurukirapo kuchokera pano, ndidzaonetsetsa kuti ngakhale mnyamata wolima ku munda azindikire choonadi kuposa inu." Anthu ambiri m'dziko la Angelezi anamuukira Tyndale ndipo iye anathawa kukabisara m'dziko la Germany. Ndi m'Germany momwe Tyndale anachitira ntchito yake yasindikiza Chipangano Chatsopano m'Chingelezi.

Koma iye anaperekedwa m'manja mwa adani ake, ndipo anaponyedwa m'ndende momwe anakhalamo miyezi ingapo. Kenaka anachitira umboni uthenga anaulalikirawo pophedwa monga mboni.

[Hugh] Latimer anapitiriza kulalikira zakuti Bukhu Lopatulika liwerengedwe m'chilankhulo cha anthu. "Kodi mukumdziwa," iye anafunsa, "m'episkopi wotangwanika kwambiri m'Engaland? Ndikukuonani mukundicheukira kuti ndimtchule. Ndidzakufotokozerani za iye. Ndi mdierekezi amene samatopa pa ntchito yake m'dziko lapansi'li; simudzampeza atangokhala mtambasale."

Chiphunzitso chomwe Okonzanso oyambirira'wa anafunitsitsa kuchipambanitsa – ndi chomwenso chinakwezedwa ndi akhristu a chi-Waldanse, Wycliffe, Yohane Huss, Luther, Zwingli, ndi onse amene anawatsatira awa, – chakuti Bukhu Lopatulika liri la myaya ndiponso maziko a chikhulupiriro choonetsedwa mwa ntchito. Iwo anakanitsitsa zakuti apapa, mabungwe ao, ansembe ndi mafumu ndiwo anali ndi ulamuliro mu zinthu za chipembedzo.

Ngakhale kukhazikikitsidwa kwa Mpanduko kukhala mchitidwe wa chipembedzo kunachitika m' England, sikunathetse chizunzo ndi kuphedwa kwa okhulupirira choonadi. Ngakhale zikhulupiriro ndi ziphunzitso zabodza zambiri za Aroma zinakanidwa, koma za pang'ono zinatsalira. Inde ulamuliro wa papa unakanidwa m'dziko'lo, koma m'malo mwa papa utsogoleri wa za chipembedzo unatengedwa ndi ufumu wa za dziko. Kusamvetsetsa za kufunika kwa ufulu wa chipembedzo kunapitirirabe.

M'zaka za pakati pa 1600 ndi 1700 zikwizikwi za abusa ambiri anachotsedwa ntchito. Anthu analetsedwa ndi kuopsyetsedwa kuti adzaponyedwa m'ndende, kulipiritsidwa ndalama zochuruka, ndi kuthamangitsidwa m'dziko'mo ngati angapezeke pa misonkhano iri yonse ya mipingo ina kupatula yokhayo yomwe iri ziwalo za mpingo wa Anglican. Koma Mulungu anakhalabe ndi anthu ake, ndipo chizunzo sichinagonjetse umboni wao. Ambiri anathamangitsidwa kuoloka nyanja za zikuru kuthawira ku Amerika, chinthu chomwe chinali maziko a ufulu wachipembedzo womwe unakhazikitsidwa m'dziko'lo.

Zaka zana limodzi pambuyo pake, mu nthawi inanso ya mdima wa uzimu, Whitefield ndi a Wesley anaturukira monga atumiki achoonadi a Mulungu.

Atangokhazikika iwo eni m'chikhulupiriro cha Khristu moyo wao wonse unamva changu chakufunitsitsa kufalitsa chidziwitso cha uthenga wa choonadi chopambana cha chisomo chaulere cha Mulungu'chi kuli konse ku dziko lapansi.Whitefield anakhala moyo wakudzikana mwini yekha, osati chifukwa chakudzikonda koma chifukwa cha chikhulupiriro chomwe chinali mwa iye; osati monga chiyambi koma monga chipatso cha moyo wake wa chiyero. Chisomo cha Mulungu mwa Khristu chiri maziko a chiyembekezo cha m'khristu ali yense, ndipo chimaonekera kudzera pa kumvera.

Poyankhapo pa chiphunzitso chakuti pa imfa ya Khristu malamulo khumi anathera pa mtanda pamodzi ndi malamulo a zinsembe, [Yohane] Wesley anati, "Lamulo la ufulu, lopezeka m'malamulo khumi, lomwenso linaphunzitsidwa ndi aneneri, silinathetsedwe ndi Yesu. Ndipo sichinali cholinga chake kuti pamene anadza adzathetse mbali iri yonse ya chilamulo. Ili ndi lamulo limene zibvute zitani silidzachotsedwa, ndipo ndi lachikhalire monga mboni yokhulupirika Kumwamba. Mbali iri yonse ya chilamulo inali yoti idzakhala ikugwira ntchito pa mtundu wonse wa anthu ku midabwo yonse; siidzasintha chifukwa chakuti mwina nthawi yatalika chikhazikitsidwire, koma chifukwa malamulo ali chikhalidwe chenicheni cha Mulungu, monga akuyeneranso kukhala chikhalidwe cha munthu, ndiponso ali kusasinthika kwa ubale wa mbali ziwiri'zi.

Wesley anafotokozanso za m'gwirizano wa ngwiro wa pakati pa malamulo ndi uthenga wabwino. Kumbali ina, lamulo limationetsera njira ndi kutilozera ku uthenga wabwino; pamene kumbali inanso uthenga wabwino umatitsogolera kuchilunjiko cha momwe tingakwaniritsire lamulo.



Kwa iwo amene amati, "kulalikira uthenga wabwino kukukwaniritsa zinthu zonse kuphatikiza cholinga cha lamulo," Wesley anati, "Chiphunzitso ichi tikutsutsana nacho kotheratu, chifukwa sichikufotokoza bwino za ntchito ya lamulo kuti ndi kuwaonetsera anthu za tchimo ndi kuwadzidzimutsa iwo amene akanagonabe pamphepete pa dzenje la manda."

Choncho ponka iye akulalikira za uthenga wabwino wa chisomo cha Mulungu, Wesley monga Ambuye wake, anafunitsitsa, "kukuza chilamulo ndi kuchilemekeza." Ndipo mokhulupirika anaigwira ntchito imene Mulungu anampatsa, ndipo zipatso zake zinali zopambana zomwe mwini yekha anachitiranso umboni ndi maso ake.

## *7. Bukhu Lopatulika ndi Kuukira kwa ku France*

M' zaka za pakati pa 1500 ndi 1600 chotsatira cha Kukonzanso chinali chakuti Bukhu Lopatulika linaperekedwa m'manja mwa anthu ndipo linafalikira ku maiko onse a ku Ulaya. Koma mu limodzi la maiko'wo ngakhale kuwala kunalifikira, kunakhala kopanda tanthauzo chifukwa cha mdima wa tchimo. Kwa nthawi yaitali kulimbana pakati pa choonadi ndi chisalungamo kunakhala kukuchitika. Potsirizira chisalungamo chinapambana ndipo choonadi cha Kumwamba chinaponyedwa kunja. Ndipo Mzimu wa Mulungu anachotsedwa pa anthu amene anakhala akuchinyoza chisomo chake. Kuipa kunaloledwa kuti kukule msinkhu kufika pa kukhwima. Ndipo dziko lonse lapansi linachiona chipatso chakusankha kwa kukukana kuunika.

Nkhondo yakulimbana ndi Bukhu Lopatulika, inapita chitsogolo kwa zaka mazanamazana m'dziko la France yomwe chotsatira chake chinakhala kuukira ulamuliro wa dziko'lo. Kuukira koopsyako kunachitika monga chotsatira cha ulamuliro wankhanza wa mpingo wa Aroma wolimbananso ndi kupondereza Bukhu Lopatulika.

Palibe dziko linakhala ndi udani pa Khristu monga umene unaonetsedwa ndi dziko la France. Panalibe dziko ndi limodzi lomwe momwe choonadi chinapezana ndi mabvuto wonyansitsitsa. Pa chizunzo chimene dziko la France linachitira pa abvomerezi a uthenga wabwino, kunali kumpachika Khristu kwachiwiri kudzera mwa ophunzira ake, ma-Albigenses [a Mpanduko] a ku France. Anthu olimba mtima a chi - Heguenot, [a Mpanduko enanso a ku France], pakumenyera ufulu wakuti munthu akhale ndi ufulu wakupembedza momasuka, anakhetsa mwazi wao m'mabwalo ambiri ankhondo.

Koma kuphedwa kwa anthu kochititsa mantha ndi chisoni kwambiri, koipitsitsa komwe kunali kusanachitikepo m'zaka zambuyo, kunali kwa ku St. Bartholomew Massacre [August 24, 1572].

Mzimu woipa womwe unakhetsetsa mwazi kosaneneka ku St. Bartholomew Massacre ndi womwenso unatsogolera zochitika za Kuukirana komwe kunachitika ku France.

Ulamuliro wokana Mulungu komanso woopsya womwe unali nkulamulira m'dziko la France, mu nthawi ya Kuukirako unachita nkhondo ndi Bukhu Lopatulika yomwe dziko lapansi silinayambe laionapo. Mau a Mulungu analetsedwa ndi nyumba ya malamulo. Malamulo a Mulungu anaponderezedwa kumapazi. Machitidwe a mtundu wina ali wonse achipembedzo analetsedwa kupatula ufulu wa chibadwidwe ndiponso kupembedza Mai Dziko.

Dziko la France litakana kupembedza Mulungu wa moyo, "Iye amene akwezedwa ndi woposa zonse, Iye amene ali wa ku nthawi zonse," pang'onopang'ono linayamba kupembedza mafano, nilikweza Malingaliro a Umunthu, ndi kujambula chithunzi cha mkazi wamaliseche amene anthu anampembedza.

Unali ulamuliro wa chikunja wa utsogoleri wa mpingo wa Aroma umene unayambitsa machitidwe a chikunja omwe ulamuliro wa dziko wokana Mulungu unayesetsa kuwakwaniritsa. Malamulo a mpingo wa Aroma ndiwo anapangitsa kuti machitidwe a chikhalidwe cha anthu, ndale ndiponso za chipembedzo zilifulumizitse dziko'lo ku chionongeko.

Mzimu wakupembedza mwa ufulu ndi momasuka unayendera limodzi ndi Bukhu Lopatulika. Kuli konse kumene uthenga wabwino unalalikidwa anthu anaulandira, ndipo nzeru zao zimatseguka. Iwo amatha kuchita zinthu mwaluntha ndi molingirira bwino. Mafumu anachiona ichi nachita mantha chifukwa cha chinthu choipitsitsa chimene anachitira Mau a Mulungu. Koma mpingo wa Aroma sunachedwetse kuwasokoneza kuti achite nsanje kuphatikiza pa mantha ao'wo.

Mafumu'wo sanathe kulingirira konse za chotsatira choipitsitsa chomwe chinadza chifukwa cha lamulo analikhazikitsa'lo. Bukhu Lopatulika limene analichotsa likanaidzadza m'mitima ya anthu ndi malamulo a chilungamo, kudzipatula, choonadi, kusasankhana, ndiponso kuchitirana ubwino pakati pa anthu onse zomwe ndi maziko achipambano a mtundu uli wonse. Iye amene aopa Mulungu adzalemekeza wolamulira wa anthu a mtundu wake pozindikira kuti ulamuliro uli wonse umaikidwa ndi Mulungu. Koma dziko lomvetsa chisoni la France linaletsa Bukhu Lopatulika ndi kuthamangitsa alaliki onse a uthenga wabwino. Alaliki ankhaninkhani anathawa; ndipo izi zinachitika kwa zaka mazana awiri mphambu makumi asanu pambuyo kukonzanso kutachitika kale.

Panalibe munthu ndi m'modzi yemwe m'France m'zaka zimenezi amene sanachitire umboni za kuthamangitsidwa ndi kuthawa kwa alialiki a uthenga wabwino. Pamene alaliki'wa ananka akulowa ndi

kulalikira m'maiko ena anthu aku France anadzichotsera eni okha madalitso.

Ndi kuthawa kwa anthu a chi-Huguenot, zinthu zambiri zinabwerera m'mbuyo m'France. Ntchito zopanga katundu ndi za malonda zinaima.

Uthenga wabwino ukanathandiza kuthetsa mabvuto a zandale ndiponso a chikhalidwe cha anthu omwe anabvutitsa kwambiri ansembe, mfumu, aphungu a nyumba ya malamulo, zomwe zinapangitsa kuti dziko'lo ligwe m'masautso, nkhanza ndi chisokonekero. Chifukwa chakusowa uphungu wochokera m'Mau a Mulungu, anthu anapatukira ku ziphunzitso za chikunja ndi ku makhalidwe odzikonda, nakhala mu umbuli ndi kukhulupirira ziwanda.

Koma motsutsana ndi m'mene Mpingo wa Romu unafunira kukwaniritsa chifuniro chake, zinthu zinasokonekera koposera muyeso. Powatsekera anthu mu mdima wa ziphunzitso zake za bodza kuti asadziwe Mulungu, chifukwa cha umbuli anthu'wo anakhala oukira ndiponso opandukira ndi a dzipolowe.



Mpingo wa Romu unanyozetsa khalidwe la Mulungu, ndi kupotoza malemba ake, ndipo chotsatira chake chinakhala chakuti anthu anaukira Bukhu Lopatulika ndi kumkana Iye amene analipereka.

Koyambirira kwa Kuukira, kudzera m'chilolezo cha mfumu, anthu anapatsidwa ulamuliro woposa wa iwo amene anawalamulira komanso wa ansembe kuuphatikiza pamodzi. Choncho mphamvu zinali m'manja mwao, koma sanali okhwima m'malingaliro kuti nkuzigwiritsa ntchito izi moyenera ndiponso mwa luntha. Iwo amene anazunzidwa anatengerapo mwai wakubwezera pa zimene owazunza anawachitira kale.

France wodzala ndi chisoni anakolora zimene anabzala pakukhetsa mwazi wochuruka. Kuopsya kwa kumvera ulamuliro wa mpingo wa Aroma kunabala chipatso chowawitsa. Kulimbana ndi Bukhu Lopatulika kunadzetsa nthawi imene mpaka lero imatchedwa, "Ulamuliro Wochititsa Mantha ." Mtendere ndi chimwemwe zinachoka m'mabanja ndi m'mitima ya anthu. Palibe anali ndi ufulu m'moyo wake.

Mfumu, ansembe ndi anthu otchuka a dziko'lo anakakamizidwa kugonjera ku nkhanza za anthu osadziwa chomwe amachita koma mtima wakuononga. Chilakolako chao chakufuna kubwezera nkhanza zomwe anachitiridwa chinafika poipa kwambiri pamene anafika pakuipha mfumu; komanso anthu amene analamula za imfa ya mfumuyo, mosakhalitsa naonso anapehedwa ponyongedwa. Mizinda yonse ya dziko'lo inasanduka malo ochititsa mantha komanso chisoni. Kuphatikiza pakuphana kwa chisawawa, magulu amene anatsogolera dzipolowe'zi naonso anaukirananso okhaokha kotero kuti France linasandulika chigwa cha chisokonekero komwe magulu osiyanasiyana anakanganiranako mokakamizidwa ndi mkwiyo komanso chilakolako choononga. Komanso kuonjezera pa chisoni chomwe chinalipo kale, pfuko la France linalowanso mu nkhondo yoononga koopsya yomwe inatenga zaka zambiri yolimbana ndi mapfuko ena a mphamvu kwambiri a ku Ulaya.

Bvuto lalikuru kwambiri limene linadzetsa zowawa zonsezi pa anthu a ku France linali chifukwa chakukana choonadi chomwe ndi chinthu chofunikira kwambiri; choonadi chakuti ufulu weniweni wa munthu uli m'Mau ndi Malamulo a Mulungu. "Mwenzi utamvera malamulo anga, mtendere wako ukanakhala ngati mtsinje ndi chilungamo chako monga mafunde a nyanja."

Anthu okana Mulungu, oukira ndi opandukira anatsutsa ndi kunyoza malamulo a Mulungu; koma zotsatira za kuipa kwa machitidwe ao'wa zinatsimikizira kuti chimwemwe ndi chisangalalo cha munthu zimapezeka pakumvera Malamulo a Mulungu. Iwo amene sangathe kuphunzira kuchokera m'Mau a Mulungu angatsimikizire za zotsatira za kunyozera chomwe Mau a Mulungu akunena powerenga mbiri za amitundu. Mu nthawi ya Kuukira kwa ku France bungwe lalikuru loyendetsa ulamuliro wa Kuukirawo mwakachetechete linachotsa ndi kuika pambali lamulo la Mulungu, koma ulamuliro womvetsa chisoni ndi wochititsa mantha umene unatsatira chinthu chochitika ndi choipa ichi ndi zotsatira za kutero zinaonedwa ndi onse – France pakufuna atakhala ufumu womasuka kuchoka m'malamulo a Mulungu analowa m'chisautso chachikuru. Kusamvera ndi kuswa malamulo a chilungamo a Mulungu kunadzetsa chisoni ndi chionongeko. France anagwedezeka ngati ndi chibvomezi. "Bukhu Lopatulika ndi chida chimene chagonjetsa adani ambiri." "Mau a Mulungu wathu adzakhala nthawi za chikhalire." "Malamulo ake onse ndiwo okhulupirika, Achirikizika ku nthawi za nthawi, achitika m'choonadi ndi chilunjiko." Yesaya 40:8; Masalmo 111:7,8. Chinthu chiri chonse chimene chingamangike pa ulamuliro wa munthu chidzagonjetsedwa; koma icho chomwe chakhazikika pa thanthwe la lamulo lamyaya la Mulungu chidzakhala ku nthawi za nthawi.

## *8. Atate Ogwiritsitsa Chikhristu ndi Ufulu wa Chipembedzo*

Ngakhale Okonzanso a Chingelezi, anakana ziphunzitso za mpingo wa Aroma, koma si zonse, anasungabe zina zambiri. Choncho ngakhale anakana ulamuliro ndi zolembedwa monga mwa mwambo za Aroma anasunganso zambiri za maphunzitso ndi miyambo yao zomwe anazilowetsa m'kapembedzedwe ka mpingo wa England (Anglican).


Pachifukwa chakuti ziphunzitso zao zinafananako pang'ono ndi za mpingo wa Aroma, iwo anaona kuti nkokwanira kuzisunga. Kuyambira pa chiyambi kupandukira Mulungu kwakukuru kunachitika pamene mpingo unafuna kuonjezerapo maganizo ake a umunthu pa ulamuliro wa Mulungu.

Mpingo wa Anglican, pokhala pansi ndi kuthangatidwa ndi ulamuliro wa dziko sunalora kusintha kuli konse pa zimene unazikhazikitsa. Kulowa mu mpingowo kunachitika potsatira malamulo opangidwa ku nyumba ya malamulo. Machitidwe ali onse osabvomerezeka ndi mpingo'wu analetsedwa, ndipo owachita amalandira chilango cha kumangidwa, kuthamangitsidwa m'dziko la England, kapena kuphedwa. Mfumu [James 1] atangokwezedwa pa mpando wa chifumu wa dziko la England analumbira kuthana ndi opembedza a chi-Puritan pokhapokha "ngati atabvomereza malamulo, koma ngati sanatero anathamangitsidwa m'dzikomo kapena kuonetsedwa nkhanza zoipitsitsa." Ena a anthu'wa anathawa kukabisala m'dziko la Holland. Chizunzo, kuonongedwa kwa chuma ndi miyoyo, ndiponso kuponyedwa m'ndende zinawachitikira. Zolinga zao zinasokonezedwa, naperekedwa iwo m'manja mwa adani ao. Koma potsirizira kupirira ndi kulimba mtima zinawachitira iwo chipambano, napeza mpumulo ndi chitchinjirizo m'dziko la a Dutch.

Ngakhale iwo anali aumphawi wosaneneka koma anayamika Mulungu chifukwa cha madalitso amene Iye anapitiriza kuwachitira, nadzala ndi chimwemwe chifukwa cha mtendere wa chiyanjano chao m'moyo wosaopsyezedwa. Ndipo pamene dzanja la Mulungu linawaonetsera njira yakuti aoleke nyanja yaikuru, kupita ku dziko limene likakhale laolao ndi kuwasiyira ana ao chuma cha mtengo wapatali cha ufulu wa chipembedzo, iwo anapita chitsogolo, osakaika za njira imene Mulungu anawatsogolera. (1620).

Atate a chikhulupiriro chozamawa ananyamuka m'dziko la Holland kunka akudzifunira malo okhalamo atsopano m'Dziko Latsopano. Yohane Robinson, yemwe anali mbusa wao, amenenso anakanizidwa kuti asapite nao, polawirana nao anati, "Ndiri ndi chikhulupiriro kuti Ambuye ali nacho choonadi ndi kuunika komwe adzapitiriza kukuonetsera kudzera m'Mau ake Oyera. Koma kumbali yanga sindingathe kudandaulira mokwanira za machitidwe amene mipingo yakukonzanso irimo, imene yafika pa nthawi ya chifooko ya chipembedzo iyi, ndipo sidzatha kupita chitsogolo kuposa pamene inathera ntchito ya Kukonzanso. Kumbukirani pangano lanu ndi Mulungu ndiponso wina ndi mnzake, kuti mudzakulandira kuwala kuli konse angakuonetseni kuchokera m'Mau ake olembedwawa."

Akhristu odzala ndi chikhulupiriro'wa ananyamuka ulendo wao napirira zoopsya zonse za ulendo wao wautali wa pa nyanja zazikuru. Koma ngakhale iwo anali oona mtima ndi oopa Mulungu, Atate a chikhulupiriro'wa anakhalabe akhungu osazindikira za chomwe ufulu wa chipembedzo unali ndiponso umatanthauza. Ufulu umene iwo anaubvutikira ndi kudzipereka nsembe kuti aupeze, sanali okonzeka iwo eni kuupatsa kwa anthu ena. Wina wa abusa otchuka wa gulu'lo ku chigawo cha dooko la Masaasachusetts potchinjiriza kulephera kwao kupatsa ufulu'wo kwa ena anati, " Kunali kulolerana pa chipembedzo komwe kunalipangitsa dziko lapansi kusokonekera pa chikhristu chake; ndipo mpingo sunalakwe powalanga anthu oukira." Pamene izi zimalankhulidwa nkuti ulamuliro wa za dziko uli m'manja mwa mpingo. Sipanatenge nthawi yaitali kuchokera pamene mau'wa analankhulidwa – chizunzo cha okhulupirira chinayambikanso.



Zaka khumi ndi chimodzi kuchokera pamene boma loyamba linakhazikitsidwa, Roger Williams anafika ku Dziko Latsopano. Iye anadza kuti adzakhale mosangalala mu ufulu wachipembedzo; koma mosiyana ndi anzake onse, iye anaona chinthu china chomwe ndi anthu ochepetsetsa kwambiri anachiganizira – chakuti ufulu umene anaupeza'wo unali wa anthu onse mosasankha mtundu osati wa anthu owerengeka okha. Iye anafotokoza kuti unali udindo wa oweruza milandu kuchepetsa kuswa malamulo, ndi kuti asalamulire chikumbumtima cha munthu. Pa nthawi imene Rogers amalankhula mau awa, nkuti munthu akuti akangokhala nawo pa nthawi ya mapemphero a mpingo wokhazikika womwe iye sanali chiwalo chake amalandira chilango cha kulipira kapena kuponyedwa m'ndende, ndiponso kuti mabwalo a milandu anali ndi ulamuliro pa mipingo, ndiponso kuti iye atapempha kuti pakhale ufulu wakupembedza zomwe anzake sanagwirizane nazo. Kenaka iye analamulidwa kuti athamangitsidwe kuchoka ku zigawo zonse za maboma anakhazikitsidwa'wo; ndipo poopa iye kumangidwa, anaumirizika kuthawa, ndipo mkati mwakuzizira ndiponso anamondwe za nthawi ya dzinja, analowa iye m'nkhalango ya mdima bi. Ndipo atayenda kwa miyezi yochuruka m'nyengo zobvutazo, osadziwa kumene amapita anaturukira m'mphete mwa Dooko la Narragansett, kumeneko anaika maziko a boma loyambirira lokhala ngati momwe ali malamulo oyendetsera maboma ambiri momwe muli ufulu wachipembedzo lero lino. Kaboma kakang'ono kamene Rogers anakakhazikitsa pa Chisumbu cha Rhode, kanakhala pothawirapo ndi kupulumukira anthu onse opsyinjika ndi ozunzidwa; ndipo kanapitirira kukhala kotchuka ndi kopambana kufikira pamene malamulo enieni – a dziko akayendetsedwe kabwino ndi olekanitsa ntchito za boma ndi za chipembedzo anakhazikitsidwa – nakhala maziko a Malamulo oyendetsera dziko la ufulu wodzilamulira la Amerika wa

Mgwirizano.

Malamulo'wo amafotokoza momveka bwino za kusafunikira kwakuti ntchito za chipembedzo zidzilamulidwa ndi boma m'mau akuti, "Pasakhale machitidwe a mtundu wina uli wonse wa chipembedzo adzitengedwa kukhala chomyenereza munthu kukhala pa udindo wina uli wonse wotumikira m'boma m'dziko la Amerika." "Nyumba ya Malamulo isadzapange lamulo liri lonse lokhuzana ndi kukhazikitsidwa kwa chipembedzo, kapena kuletsa ufulu wakutero."



Pamene uthengawu unafalikira ku maiko a ku Ulaya, za dziko limene munthu aliyense anali ndi ufulu wakudyerera thukuta lake ndiponso kukhala ndi chikumbumtima chomasuka, anthu zikwizikwi anakhamukira ku mbali za nyanja ya Dziko Latsopano'lo. Bukhu Lopatulika linatengedwa kukhala maziko a chikhulupiriro, chiyambi cha nzeru, ndi lamulo la ufulu. Mau ndi malamulo a Mulungu anaphunzitsidwa mwakuya m'mabanja, m'masukulu, ndi mu mpingo; ndipo chotsatira chake chinaonekera pa ntchito zakusamalirana ndiponso chikondi pakati pa anthu ndi pakagwiritsidwe ntchito kabwino ka ndalama, luntha, chilungamo ndiponso kudzipatula kwa anthu a dzikolo. Zinatsimikizikanso kuti malamulo a m'Bukhu Lopatulika anali njira yokhayo yodalirika ndi yachipambano ku pfuko liri lonse.

Ili linali dziko limene linadabwitsa anthu ndi mtendere ndiponso chipambano cha "mpingo umene sunasoweke utsogoleri wa upapa ndiponso dziko lokhala ndi boma limene silinasoweke mfumu." Lamulo limene linakhazikitsidwa ndi atsogoleri oyambirira, longolora anthu amene anali ziwalo za mpingo okha kukhala ndi ufulu wakutengako mbali pa chinthu chiri chonse kapena kugwira ntchito yotumikira m'boma, linadzetsa chisokonekero chosaneneka. Pakutenga chipembedzo kukhala muyeso womlolera munthu ntchito m'boma, zinapangitsa kuti anthu osatembenuka alowe m'chipembedzo pongotsatira malamulo a dziko kuti aloredwe ntchito koma osati chifukwa chakutembenuka mtima.

Ichitu, mosakaika konse, ndi chimodzi cha zifukwa zakuti m'mipingo yambiri muyambe kupezeka anthu osatembenuka. Mgwirizano wa mpingo ndi Boma ngakhale unaoneka ngati chinthu chofunika, chifukwa unakhala ngati njira yolibweretsa dziko ku mpingo, koma mosabisa mau unagwira ntchito yaikuru youbweretsa mpingo ku za dziko lapansi. Chotsatira chake ndi chakuti mipingo ya Mpanduko ya ku Amerika – ndi ya ku Ulaya yomwe – ngakhale inakondwera polandira madalitso amene anadza ndi Kukonzanso, koma inalephera kuipitiriza m'ntchito yao ya kukonzansoko. Chifukwa cha ichi chipembedzo chinayamba kulowa pansi ndi kukhala monga mwa mwambo; ndipo kusayeruzika ndi chisokonekero cha uzimu zomwe zikanatha kutaidwa kunja kukanakhala kuti mpingo unapitiriza kuyenda m'kuunika kwa Mau a Mulungu, zinasungidwa ndi kukuzidwa.

Umu ndimo ntchito imene inayambitsidwa ndi Kukonzanso inanka ikuloweralowera pansi pang'ono ndi pang'ono kenaka niferatu, ndipo Satana anatsogolera anthu ambiri kusachitapo kanthu ngakhale anadziwa za kufunikira koipitiriza ntchitoyo pochipangitsa chikumbumtima chao kuiona ngati yosafunikira kwenikweni. Anthu anasiya kufufuza ndi kuwerenga Mau a Mulungu. Ataona kuti kuzunza mpingo ndi kutsutsana mwa chindunji ndi choonadi sikunampindulire, Satana anaganiza zongobweretsa machitidwe akulolerana omwenso ndi amene kale anadzetsa kupandukira Mulungu kwakukuru komwe kunatsogolera kukukhazikitsidwa kwa Mpingo wa Aroma. Iye anawatsogolera akhristu kupanga migwirizano, osati ndi anthu achikunja okha, koma ndi anthu ooneka ngati opembedza m'choonadi, koma chikhalirecho machitidwe ao ali a dziko lapansi, ndipo pakutero akhristuwo anatembenuzidwa kukhala opembedza mafano ndi zithunzi zosema. Mpingo wakhala ukuphunzitsa ndi kutchinjiriza miyambo ya umunthu,



m'malo molimbikitsa za "chikhulupiriro chomwe chinapatsidwanso kwa oyera mtima akale."

### *9. Choonadi Cha Kubwera Kwachiwiri Kwa Khristu*

Chimodzi cha ziphunzitso komanso choonadi chopambana chomwe Bukhu Lopatulika lachionetsera poyera ndi chija cha kubwera kwachiwiri kwa Khristu, kudzaitsiriza ntchito yaikuru ya chipulumuntso. Chiphunzitso ichi cha kubweranso kwachiwiri ndicho cholinga chenicheni cha Bukhu Lopatulika.

Kubwera kwa Ambuye kwakhala kuli chiyembekezo cha otsatira enieni a Khristu ku mibadwo yonse. Pamenepo akufa mwa Khristu adzauka, ndipo pamodzi ndi a moyo otsala'fe adzakwatulidwa kukakomana ndi Ambuye mu mlengalenga. "Ndipo potero," Paulo anatero, "tidzakhala ndi Ambuye nthawi zonse." 1 Atesalonika 4:17. Oyera mtima akale anakhala akumyembekezera "Ambuye alinkudza pa mitambo ya kumwamba, ndi mphamvu ndi ulemelero wa Atate wake."

Luther ananena, "Ndiri ndithu ndi chitsimikizo mwini ndekha, kuti tsiku la chiweruzo silingakhale liri kutali kuposa zaka mazana atatu kuchokera pano. Mulungu sadzalora ndipo sakulora kuti dziko loipali lipitirire kukhalako." "Dziko lakalekale'li si liri patali ndi chimaliziro," anatero Melancthon.

Ridley analemba, "Dziko lapansi mosakaika – ichi ndakhulupirira ndithu, ndipo ndikuchinena – layandikitsitsa chimaliziro." Pamene mzimu wakudzichepetsa ndi kudzipereka ukunka ukucheperachepera mu mpingo ukupatsa mpata wa kunyada ndi kupembedza monga mwa miyambo, ndipo chikondi pa Khristu ndi chikhulupiriro za kudza kwake kwachiwiri zikunka zikuzilara. Pa nthawi imene Mpulumutsi mwini wake ankaowafotokozera ophunzira ake za zizindikilo za kubwera kwake, analoseranso za kubwerera m'mbuyo kwa moyo wa uzimu kwa anthu ambiri komwe kudzachitike pafupi penipeni pakubwera kwake kwa chiwiri. "Koma inu dikirani nyengo zonse, ndi kupemphera, kuti mukalimbike kupulumuka zonse zimene zidzachitika, ndi kuimirira pamaso pa Mwana wa munthu." *Luka 21:36.*

Chinali chinthu choyenera kuti anthu achenjezedwe za choopsya chomwe alimo; kuti agalamuke ndi kukonzekera za zizindikilo zokhuzana ndi kutsekedwa kwa chitetezo. "taonani tsiku la Yehova lidza, la nkhanza, ndi mkwiyo ndi kukalipira kwaukali; kupasula dziko, ndi kudzaonongamo akuchimwa psiti." Yesaya 13:9. "Muombe lipenga m' Ziyoni nimupfuulitse m'phiri langa lopatulika; onse okhala m'dziko anjenjemere; pakuti tsiku la Yehova lirinkudza pakuti liyandikira." "Munditembenukire Ine ndi mtima wanu wonse, ndi kusala, ndi kulira, ndi kuchita maliro; ndipo ng'ambani mitima yanu, si zobvala zanu ai." *Yoweli 2:1, 12-13.*

Pofuna kuwakonzetsera anthu kuti adzaime m'tsiku la Mulungu, pamafunika ichitike ntchito yaikuru yakukonzanso. Tsono Poona kuti anthu ambiri amene amadzitcha ndi dzina lake ndi osakonzeka konse kukhala m'chilungamo chake, ndiponso kuti nthawi yatsala pang'ono, Mulungu anatumiza uthenga wakuchenjeza kuti ugalamutse iwo akugona tulo ndi kuwatsogolera kukonzekera za kubwera kwa Ambuye wao.

Chenjezo ili linaperekedwa kwa anthu onse pa Chibvumbulutso 14. Chenjezo'li linachitika kudzera mu uthenga wa angelo atatu. Woyamba wa angelo amene'wa akulalikira za kuyandikitsitsa kwa Chiweruzo. "Opani Mulungu, mpatseni ulemelero; pakuti yafika nthawi ya chiweruziro chake; ndipo mlambireni Iye amene analenga m'mwamba ndi mtunda ndi nyanja ndi akasupe amadzi." *Chibvumbulutso 14:7.* Anthu okhulupirika omwe anamvera zomwe Mzimu wa Mulungu anawalamulira m'ziphunzitso za m'Mau ake'wa, anauzidwa kulalikira chenjezo ili ku dziko lapansi.

Mpingo umene unapandukira Mulungu unatseka maso a anthu kuti asamvetsetse za zizindikilo za nthawi. Koma Mulungu sanafune kapena kulora kuti anthu omwe akumkhulupirira Iye akhale mu mdima; ngakhale iwo anadzilekanitsa ndi chikondi chake. Pena pali ponse pamene anthu amakana kumva malamulo ake, Iyenso samakwaniritsa malonjezano ake pa iwo. Mulungu amafuna anthu ake akhale ndi chikhulupiriro chakuchita mwa ntchito ndiponso akumvera molingana ndi madalitso



ndiponso chisomo chimene chapatsidwa kwa iwo. Kumvera kumadalira pa kudzipereka nsembe ndiponso kulora kumva zowawa; ndipo ichi nchifukwa chake anthu ambiri omwe anadzitcha kuti ali otsatira a Khristu analephera kukulandira kuwala kochokera Kumwambaku, ndipo, monga Ayuda a kale, sanathe kuzindikira ngakhale za makwaniridwe a nthawi.

### *10. Kuunika Kwatsopano Kwa m'Bukhu Lopatulika Kuturukiridwa*

Mlimi wachilungamo, wodzichepetsa kuchokera pansi pa mtima, amene wanakhala akutsutsana nacho choonadi cha Bukhu Lopatulika, koma pambuyo pake anafunitsitsa atachizindikira anasankhidwa mwapadera ndi Mulungu kutsogolera pa ntchito yakulalikira za kudza kwachiwiri kwa Khristu. Ali wa zaka makumi awiri mphambu zinai Mzimu Woyera anautsimikizira mtima wake za kukhala kwake munthu wochimwa [1816]. "Ndapeza kuti Bukhu Lopatulika landionetsera za Mpulunutsi amene moyo wanga wakhala ukumfunitsitsa." Pa nthawi'yi iye anayamba kukhulupirira za chipembedzo chomwe anakhala akuchinyoza. Koma abwenzi ake amene anakhala akunyoza nao limodzi, sanachedwe kuyamba kutsutsana naye pogwiritsa ntchito mau amene iye anawagwiritsa ntchito pa nthawi imene ankatsutsana ndi Choonadi cha Bukhu Lopatulika.

Moyesetsa ndi pofunitsitsa kupewa malingaliro komanso ndemanga za maganizo a umunthu, iye anayerekeza lemba ndi lemba linzake mothandizidwa ndi ndemanga zomwe zimalembedwa m'munsi mwa tsamba liri lonse komanso nkhokwe ya ndime za Bukhu Lopatulika. Moikapo mtima kwambiri iye anawerenga mabuku a Danieli ndi Chibvumbulutso, nagwiritsa ntchito lamulo lija lakuti Bukhu Lopatulika limadzimasulira lokha poyerekeza lemba ndi lemba lina, ndipo pamene anatero anapeza chimwemwe chachikuru poturukira kuti ziphiphiritso za m'maulosi zinayamba kumveka bwino.

Iye anafika pokhutitsidwa kuti chiphunzitso chakuti Khristu adzayamba wakhazikitsa ufumu wa uzimu...padziko lapansi kwa zaka chikwi chisanafike chimaliziro...sichinali chochokera m'Bukhu Lopatulika. Komanso kuti chiphunzitso'chi sichinayambe chaphunzitsidwapo mu mpingo wa atumwi. Ndipo chiphunzitso'chi chinakhala chikukanidwa ndi akhristu kufikira pafupifupi koyambirira kwa zaka za pakati pa 1700 ndi 1800. Miller anapeza kuti kubwera kwa Khristu kunali kwenikweni monga kwafotokozedwa momveka bwino m'Bukhu Lopatulika. Ndipo pakubwera kwake akufa olungama adzaukitsidwa, ndipo

olungama omwe adzakhale ali moyo adzasinthidwa. "Pakuti lipenga lidzalira, ndipo akufa adzaukitsidwa osabvunda, ndipo ife tidzasandulika. Pakuti chobvunda ichi chiyenera kubvala chisabvundi, ndi cha imfa ichi chidzabvala chosafa." *1 Akorinto 15:12-13.* "Ndipo akufa mwa Ambuye adzayanba kuuka; pamenepo ife okhala ndi moyo, otsalafe, tidzakwatulidwa nao pamodzi m'mitambo kukakomana ndi Ambuye mu mlengalenga, ndipo potero tidzakhala ndi Ambuye nthawi zonse." *1 Atesalonika 4:16, 17.*

Taona kuchokera m'malemba apatsidwa'wa kuti pamene Mwana wa munthu adzadza, akufa adzaukitsidwa osabvunda ndipo amoyo adzasinthidwa. Ndi kusinthidwa kwakuru kumeneku iwo adzakonzetsedwa kulandira ufumu'wo. Kuonjezera apo taonanso kuti zizindikiro ndiponso zochitika zonse za dziko lapansi zikugwirizana ndi zomwe maulosi akufotokoza za masiku otsiriza. Kuchokera apo Miller anapitirira nafika potsimikizitsa kuchokera pakuwerenga Bukhu Lopatulika lokha, kuti momwe zinthu ziliri nthawi ya mathedwe a dziko lapansi inangotsala pang'ono.

"Chitsimikizo china chomwe chinakhuza maganizo anga kwambiri," anapitiriza kufotokoza, "chinali ndondomeko yokhazikika bwino ya momwe lalembedwera Bukhu Lopatulika. Ndinaturukira kuti zochitika zonse zimene zinakwaniritsidwa kale, zinachitika molingana ndi nthawi zake zoikika." "Zinsinsi nza Yehova Mulungu wathu," anatero Mose, ""koma zobvumbuluka nza ife ndi ana athu kosatha." *Deuteronomo 29:29.* Choncho ophunzira a Mau a Mulungu ayenera ndi chikhulupiriro chonse kuyembekezera ndi kuonetsetsa kuti pafupifupi zinthu zonse zomwe zikuchitika mu mbiri ya mtundu wa anthu zikugwirizana kotheratu ndi choonadi cha Bukhu Lopatulika.

Ulosi umene ukufotokoza mwatchutchutchu za kubwera kwachiwiri ndi wa pa Danieli 8:14; "Mpaka masiku zikwi ziwiri mphambu mazana atatu usana ndi usiku; pamenepo malo opatulika adzayeretsedwa." Miller anapeza kuti tsiku limodzi m'ulosi likuimira chaka chimodzi. (Numeri 14:34; Ezikieli 14:6). Kuchokera apa iye anakutenga kuyeretsedwa kwa malo opatulika komwe kunaloseredwa pa Danieli 8:14, kuti kumaimira kuyeretsedwa ndi moto kwa dziko lapansi pakubwera kwachiwiri kwa Khristu. Iye analingalira kuti nthawi yakuyamba kuwerenga masiku 2300'wa ikanadziwika, pomwepo tsiku la kubwera kwachiwiri lidzadziwika mosabvuta.

Miller sanathe kumvetsetsa chenicheni chomwe chimafotokozedwa pa mutu wachisanu ndi chitatu wa Danieli, makamaka za pomwe pamayambira masiku 2300. Danieli nayenso "anakomoka ndi kudwala masiku ena." "Ndipo ndinadabwa nao masomphenyawo," iye anatero, "koma panalibe wakundizindikiritsa." *Danieli 8:27.* Kenaka Mulungu anatumiza wamithenga wake, "Zindikiritsa munthuyo masomphenyawo." *Ndime 16.*

Panali chinthu chimodzi chokha m'masomphenya a mutu wachisanu ndi chitatu'wu chomwe chinali chosafotokozedwa, kutalika kwa nthawi, -masiku 2300; choncho popitiriza kumasulira kwake, mngelo anakhazikika kwambiri pa nthawiyo: "Masabata makumi asanu ndi awiri alamulidwira anthu a mtundu wako ndi mudzi wako wopatulika ... Dziwa tsono, nuzindikire, kuti kuyambira kuturuka kwa lamulo lakukonzanso, ndi kumanga Yerusalemu, kufikira wodzozedwayo, ndiye kalonga, kudzakhala masabata asanu ndi awiri; ndi masabata makumi asanu ndi limodzi mphambu awiri makwalala ndi chemba zidzamangidwanso, koma mu nthawi za mabvuto. Ndipo atapita masabata makumi asanu ndi limodzi mphambu awiri wodzozedwayo adzalikhidwa, nadzakhala wopanda kanthu...Ndipo iye adzapangana chipangano cholimba ndi ambiri sabata limodzi; ndi pakati pa sabata adzaleketsa nsembe yophera ndi nsembe ya ufa." *Danieli 9:24-27.*

Mngelo anatumizidwa kuti akamfotokozere Danieli pomwe sanamvetsetse za masomphenya a mutu wa chisanu ndi chitatu, okhuza za nthawi inatchulidwayo. Liu loti, "cholembedweratu" likungopiriza ganizo lakuti "adzalamulidwa." Masabata makumi asanu ndi awiri, omwe akuimira zaka 490, akufotokozedwa ndi mngelo kuti adzalamulidwa makamaka ponena za Ayuda. Koma kuchokera ku chiyani komwe adzalamulidwa? Masabata makumi asanu ndi awiri ayenera kukhala mbali imodzi ya masiku 2300 ndipo nthawi'zi ziyenera kuyambira chaka chimodzi.

Pa Ezara 7:12-26 lamulo linaperekedwa mu mphamvu yake. Linaperekedwa ndi Aritasasta mfumu ya Aperezi m'chaka cha 457 B.C. Pakutenga 457 B.C. nthawi yomwe lamulo linaperekedwa mu mphamvu yake, chiri chonse chimene chinaloseredwa mu ulosi chokhuza masabata makumi asanu ndi awiri chinaoneka kuti chakwaniritsidwa. Lamulo la Aritasasta linayamba kugwira ntchito mu nthawi ya chirimwe m'chaka cha 457 B.C. Kuchokera pa chaka ichi zaka 483 zinapitirira ndi kuthera mu nthawi ya chirimwe m'chaka cha A.D. 27. Pa nthawi imeneyi Khristu anabatizidwa ndi Yohane, nadzozedwa Iye ndi Mzimu Woyera. "Ndipo Iye adzapangana chipangano cholimba ndi ambiri sabata limodzi."

Sabata limodzi lomwe likunenedwa apa'li ndi lotsirizira la masabata makumi asanu ndi awiri. Mu nthawi imeneyi kuyambira pa A.D. 27 mpaka pa A.D. 34, Khristu, poyamba Mwini yekha, ndipo pambuyo pake kudzera mwa ophunzira ake, anapitiriza kulalikira uthenga wabwino kwa Ayuda okhaokha. "Ndi pakati pa sabata adzaleketsa nsembe yophera ndi nsembe ya ufa."

Mu chaka cha A.D. 31, zaka zitatu ndi theka kuchokera pamene anabatizidwa, Ambuye wathu anapachikidwa, Nsembe yeniyeni kukwaniritsa zonse zimene machitidwe a zinsembe analozera, ndipo pomwepo zinsembe zonse zophera ndi za ufa za m'chilamulo cha zinsembe zinalekeka. Masabata makumi asanu ndi awiri kapena kuti zaka 490, zomwe zinaperekedwa kwa Ayuda okhaokha zinatha monga tikuonera m'chaka cha A.D. 34.

Kuchokera m'chaka chimenechi palibenso bvuto pofuna kupeza pothera pa masiku 2300. Masabata asanu – masiku – atachotsedwa pa 2300, panakhala masiku 1810. Kuyambira chaka cha A.D. 34, zaka 1810 zinathera m'chaka cha 1844.

Ngakhale anawerenga Bukhu Lopatulika monga anachitira, ndi kupitiriza pakufuna kutsimikizira kuti izi zinaperekedwa mwa bvumbulutso lochokera kwa Mulungu, Miller sanaganizire konse kuti adzafikira yankho monga anachitiramu. Zinamtengera nthawi ya zaka ziwiri akuliwerenga Bukhu Lopatulika motsimikizika mtima; pamene m'chaka cha 1818, anatsimikiza mu mtima mwake kuti kuchokera pamenepo kufika zaka makumi awiri ndi zisanu kutsogolo Khristu adzakhala atadza kudzapulumutsa anthu ake. Ngakhale iye anazindikira kuti atsutsidwa ndi anthu ambiri osakhulupirira, koma anakhalabe ndi chikhulupiriro kuti akhristu enieni adzakondwera m'chiyembekezo chakuti adzapezana ndi Mpulumutsi wao amene anamkondetsetsa posachedwa.

Koma mantha amene anali nao anali okhawo akuti nkutheka kuti anthu ambiri adzachilandira chiphunzitso'chi mwa umunthu osati podziwerengera okha kuchokera m'Bukhu Lopatulika. Iye anatenganso nthawi yake nayesetsa kupeza maumboni otsimikizira za choonadi anachipezacho, ndikulingirira mwakuya za bvuto limene anthu ena anati apezane nalo pofuna kumvetsetsa za ichi. Zinamtengera zaka zisanu akulingirira za chiphunzitso'chi napitirira iye kutsimikizika kuti anaturukiracho chinali choonadi chotsimikizika ndithu. Kuchokera pamenepo anamva chikakamizo mu mtima mwake chakuti anke akudziwitsa anthu ena za choonadi chatsopano cha m'Bukhu Lopataulika'cho. Anamva mau omuuza kuti apite ndi kulichenjeza dziko lapansi za choopsya chomwe linalimo.

Iye anayamba kuchipereka choonadi'cho poyamba kwa anthu owerengeka okha mwai wakutero ukapezeka, napempheranso kuti enanso athe kuchimvetsetsa kuti athandizane naye kuchifalitsa. Kwa zaka zisanu ndi zinai iye anadikira, koma mtima wake ukumva chikakamizo chakuichita ntchito anapatsidwayo, kufikira m'chaka cha 1831 pamene kwa nthawi yoyamba iye anachilalikira chikhulupiriro chake'chi kwa anthu onse. Modzazidwa ndi mantha iye anailowa ntchitoyi, ndi kuwafotokozera anthu omwe anadza kudzamvetsera mosamalitsa kuti nawonso amvetsetse za ulosi wakufotokoza za nthawi ndi kubwera kwachiwiri kwa Khristu. Iye analimbikitsidwa mtima kwambiri pamene anaona anthu ambiri akuchita chidwi ndi maulaliki ake. Iye



anali wa zaka makumi asanu zakubadwa, wa manyazi kulankhula pagulu komanso wodzazidwa ndi mantha za ntchito imene inapatsidwa kwa iye. Koma kuyambira pamene anayamba, ntchitoyo inadalitsidwa mwapadera ndidzetsa chipulumutso ku miyoyo yochuruka.

Pafupifupi mu mzinda uli wonse munapezeka anthu, mwina mumapezeka mazana angapo otembenuka kudzera m'maulaliki ake. M'malo mwina mumapezeka kuti mipingo ya Mpanduko imangomtsegulira zitseko zao kuti alalikiremo; nthawi zina anaitanidwa iye ndi abusa amipingo ingapo kuti akalalikire kumeneko. M'mizinda ina ikuruikuru ntchito yake inabala chipatso chochuruka kuposa m'mene anayembekezera. Misonkhano ya mapemphero inakhazikitsidwa m'mipingo yosiyanasiyana, ndi m'madera osiyanasiyana.

Iye anayenda ndi kulalikira osatopa, ngakhale kwambiri anachititsa ntchito yake m'chigawo cha New England ndiponso madera amene anayandikana ndi chigawo'cho. Sikuti Miller'yu anachita ntchito'yi osapezana ndi otsutsana naye. Mau a Mulungu anawalalikira'wo anali umboni womwe unalandiridwa ndi alaliki omwe anakonzetsedwa kuchilandira chiphunzitso cha choonadi cha kudza kwa chiwiri okha'wo. Kwa awa, "Bukhu Lopatulika, ndipo Bukhu Lopatulika lokha," ndilo linali liu lakuwalimbikitsa. Chifukwa cha kusadziwa malembo kwa iwo amene anatsutsana ndi atumiki a choonadi, adani'wo amangothamangira kunyoza ndi kunyogodola.

Adani a choonadi'wo anayesetsa ndi mphamvu zao zonse kupotoza maganizo a anthu kuti asamvetsere za chiphunzitso cha kubweranso kwachiwiricho. Iwo anauza anthu amakamvetsera maulaliki a Miller'wo kuti pakutero amachita tchimo. Koma ngakhale kutsutsako kunafika pokura msinkhu kwambiri gulu lakulalikira za kubweranso kwachiwiri'lo linanka likukulirakulira. Kuchoka pa makumi linafika pa mazana kenaka mipingo yomwe chiwerengero chao chinafika pa zikwi. Kenaka mipingo inayamba kumachotsa anthu onse amene anakhulupirira m'ziphunzitso za Miller.

Pamene kunapezeka kuti matsutsano okhuza za nthawi za maulosi sanatheke, adani otsutsa'wo anayesetsa kukhumudwitsa anthu amene amafufuza moona mtima za maulosi'wo pophunzitsa kuti maulosi onse anali otsekedwa. Mipingo ya Mpanduko inalalikira kuti Mau a Mulungu ndiwo anali ofunikira kwambiri osati maulosi ndi nthawi – zomwe ndi zobvuta kuzimvetsetsa, komwe kunali kutsutsana ndi mau akuti, "Iye amene awerenga m'kalata *azindikire*." *Mateyu 24:15.* "*Wodala* iye amene *awerenga,* ndi iwo amene *akumva*

mau a chinenerocho, *nasunga* zolembedwa momwemo." *Chibvumbulutso 1:3.*

Ndi chifukwa ninji, nanga, kuti khungu lakusamvetsetsa Mau Oyera linafalikira chomwechi? Miller nayenso chifukwa cha kusamvetsetsa komweko analalikira kuti dziko lapansi linali kachisi, nakhulupirira kuti kuyeretsedwa kwa kachisi komwe anakufotokoza Danieli kunaimira kuyeretsedwa kwa dziko lapansi ndi moto pakubwera kwachiwiri kwa Ambuye. Kulakwitsaku anakuchita potsatira ziphunzitso zotchuka ndi zolakwika za mipingo ya Mpanduko pa nkhani'yi. Kuyeretsedwa kwa kachisi kunali utumiki wotsirizira wa pa chaka womwe akuru ansembe anauchita. Umakhala chitseka kukhomo cha ntchito yonse ya chitetezero. Utumiki umene'wu mkati mwake mumakhala ntchito yakufufuza za mkati mwa mtima, chiweruzo; ndipo weniweni'wo udzachitika pafupi penipeni pakubwera kwachiwiri kwa Khristu m'mitambo yakumwamba mu mphamvu ndi ulemelero waukuru; chifukwa pamene Iye adzakhale akubwera, mlandu uli wonse udzakhala utaweruzidwa. Ndi ntchito ya chiweruzo cha mtundu umene'wu, cha pafupi penipeni pa kubwera kwachiwiri yomwe ikufotokozedwa mu uthenga wa mngelo woyamba wa *Chibvumbulutso 14:7:* "Opanai Mulungu, mpatseni ulemelero; pakuti yafika nthawi ya chiweruzo chake."

Monga mu nthawi ya Kukonzanso kwakukuru kwa m'zaka zapakati pa 1500 ndi 1600, gulu la kulalikira Kudza Kwachiwiri linaturukira kunka likulalikira m'maiko osiyanasiyana a Chikhristu nthawi imodzimodzi yomweyo. Konse ku Ulaya ndi ku Amerika, anthu a chikhulupiriro ndi pemphero anatsogolera pa ntchito yakufufuza maulosi.

M' chaka aha 1821, zaka zitatu kuyambira pamene Miller anayamba kumasulira maulosi a za chiweruzo mwakuya, a Joseph Wolff, munthu wophunzira kwambiri, "mtumwi wa ku dziko lonse lapansi" anayamba kulalikira za kubwera kwa msanga kwa Ambuye. M'nthawi ya zaka makumi awiri mphambu zinai kuyambira 1821 mpaka 1845, Wolff anayenda kunka akulalikira m'maiko ambiri: m'Africa anafika ku Aigupto ndi maiko ena akumpoto kwa dziko'lo. M'Asia anadutsa m'Palestine, Syria, Persia, Bokhara, ndi India. Iye analalikiranso m'dziko la United States of America.

M'zaka zoyambirira makamaka 1826 uthenga wa gulu lakulalikira kudza kwachiwiri'li unafika ku dziko la England. Mourant Brock, yemwe anali mlembi wa Chingelezi, akufotokoza za abusa pafupifupi mazana atatu a mpingo wa England amene anatangwanikanso ndi ntchito yakulalikira "uthenga uwu wa ufumu." Uthenga wonena kuti kubwera kwachiwiri kwa Ambuye kuchitika m'chaka cha 1844 unalalikidwanso m' Great Britain. M'chaka cha 1842, a Robert Winter amene anali mbadwa ya Chingelezi, ndipo anaulandira uthenga wakubwera kwachiwiri'wu ku dziko la America, anabwerera ku dziko la kwao kunka akulalikira za kudza kwa Ambuyeko. Anthu ambiri analumikizana naye m'ntchitoyi.

M'maiko a America wa kumwera, mu nthawi ya mdima wa chikunja chosaneneka, Lacunza, wa mtundu wa chi-Spanish yemwenso anali m'Jesuit, anawerenga Mau a Mulungu, napeza chidziwitso cha choonadi za kubwera kwa msanga kwa Khristu. M'Germany chiphunzitsochi chinali chitalalikidwa kale m'zaka za pakati pa 1700 ndi 1800 ndi Bengel yemwe anali mbusa wa mpingo wa Lutheran ndiponso wotchuka pa za chidziwitso ndiponso zofufuzafufuza mwakuya za Mau a Mulungu. Kuwala kunaturukiranso m'maiko a France ndi Switzerland. Ku Geneva Farel ndi Calvin anafalitsa choonadi cha Kukonzanso, Gaussen analalikira uthenga wa kubweranso kwachiwiri. M'Scandinavia uthenga wakubwera kwachiwiriwu unalalikidwa ndi kudzutsa chidwi cha anthu ambiri.

Anthu ambiri anatsitsimutsidwa kuchoka ku chiyero cha umunthu, nalapa ndi kusiya machimo ao. Mulungu anachiona chofunikira kufalitsa uthenga wake'wu kudzera mwa ana ang'ono. Pokhala iwo a zaka zochepa kwambiri, lamulo la dziko'lo silinathe kuwaletsa; ndipo analalikira uthengawo mosasokonezedwa.

Kwa William Miller ndi anthu onse amene analumikizana naye pa ntchitoyi kunapatsidwa ntchito yolichenjeza dziko la America. Choncho dziko'lo linakhala likuru la gulu lolalikira uthenga wakubwera kwachiwiri'wo. Umu ndimo unakwanitsidwira mwachindunji uthenga wa mngelo woyamba. Zolembera za Miller ndi anzake zinafalitsidwa ku maiko akutali. Umu ndimo unafalikira pafupi ndi kutari uthenga uwu wabwino wosatha, "Opani Mulungu, mpatseni ulemelero; pakuti yafika nthawi ya chiweruzo chake" [Uthenga wa Mngelo Woyamba. Chibvumbulutso 14:7]. [Lero lino Harvestime Books ndi Cornerstone Publishing, USA omwenso ndi alembi a kabuku mukuwerenga'ka akhala akutumiza ku maiko osiyanasiyana myandamyanda ya mabukhu ndiponso mapepala osindikizidwa a mau a Mulungu akuchenjeza a mauthenga a angelo 1, 2, 3, ndi 4 a Chibvumbulutso 14:6-12; 18:1-4 ku mbali iri yonse ya dziko lapansi omwe akunka akulalikira mu unyinji wao za chochitika chachikuru chomwe changotsala pang'ono kuchitika, kubwera kwachiwiri kwa Khristu Ambuye wathu ndi momwe anthu angakonzekere kukomana Naye ali mkhalidwe la chiyero obvekedwa ndi Miinjiro ya Chilungamo Chake. Kodi inu simungathe kukonzekera kuti tidzakomane kumeneko? [Pitirizani kuwerenga!].

Anthu ambiri anakhulupirira kuti zolembera zonse zonena nthawi za maulosi zinali zolondora. Ndipo anadzipereka nsembe mwa chimwemwe ndi kuchotsa kudzikudzika kwa m'mitima mwao nakulandira mu mphamvu yake kuwala kwa choonadi. Koma ora limene anayembekezera kuti Ambuye aturukira litafika, Khristu sanabwere kudzatenga anthu ake. Ndipo iwo amene ndi mtima wao wonse ndi modzichepetsa amayambekezera za kudza kwa Mpulumutsiyo anakhumudwa kwambiri. Panalinso ena pakati pao omwe kusinthika kwao sikunali kochokera pansi pa mtima koma chifukwa cha mantha. Awa sanakhumudwe konse ndi kusabwewra kwa Khristu'ko. Ndipo pamene kunalephereka iwo anati anadziwa kuti sikuchitika choncho sanakhumudwe chifukwa anazindikira kuti Khristu sabwera. Awa ndiwo anatsogolera pakunyoza anthu amene anakhulupirira kuchokera pansi pa mtima.

## *11. Kodi Kachisi ndi Chiyani?*

Mau a Mulungu omwe, kuposa zolembera zina zonse ali maziko ndi chikatikati cha chikhulupiriro cha chiphunzitso cha kubweranso kwachiwiri ndi awa akuti, "Mpaka masiku zikwi ziwiri mphambu mazana atatu usana ndi usiku, pamenepo malo opatulika adzayesedwa olungama." *Danieli 8:14.* Masiku a ulosi awa anaonetsedwa kuti adzathera m'nthawi ya chirimwe m'chaka cha 1844. Mogwirizana ndi momwe anaphunzitsira okhulupirira ena onse a mipingo ya Chikhristu dziko lonse lapansi, anthu oyambirira okhulupirira kubwera kwa Ambuye kwachiwiri naonso, anakhulupiriranso kuti dziko lapansi ndilo kachisi; koma pakufufuzitsa iwo m'Bukhu Lopatulika anapeza kuti ilo likumfotokoza kachisi, ku malo komwe ali, chikhalidwe chake ndi mautumiki ake m'mau akuti, "Ndipo chingakhale chipangano choyambachi chinali nazo zoikika za kulambira, ndi malo opatulika a pa dziko lapansi." *Ahebri 9:1.* Kachisi amene anamangidwa ndi Mose polamulidwa ndi Mulungu, anali malo okhalamo Mulungu Wam'mwambamwamba pa dziko lapansi. Pambuyo polowa ndi kukhazikika kwa Ahebri m'Kanani, Kachisi wa Solomo analowa m'malo mwa kachisi wa Chihemayo. Uyu ndi kachisi yekhayo yemwe wakhala aliko pa dziko lapansi amene Bukhu Lopatulika linakhala likufotokoza za iye. Paulo anamfotokozanso uyu kuti anali kachisi wa pangano loyamba.

Kodi ndiye kuti pangano latsopano liribe kachisi? "Koma mutu wa izi tanenazi ndi uwu: Tiri naye Mkuruwansembe wotere, amene anakhala pa dzanja lamanja la mpando wachifumu wa Ukuru m'Kumwamba, Mtumiki wa malo opatulika ndi wa chihema choona, chimene Ambuye anachimanga, si munthu ai." *Ahebri 8:1, 2.*

Chithunzithunzi chenicheni cha kachisi wa pangano latsopano chikuonetsedwa apa; uyu ndi womangidwa ndi Mulungu osati ndi munthu. Kachisi wina anali wa pansi pano; wina ali Kumwamba. Kachisi amene anamangidwa ndi Mose anapangidwa poonera pa chifanizo china chake. Kachisi wa Kumwambayu yemwe Yesu akutumikiramo pakali pano m'malo mwathu, ndi wamkuru ndi weniweniyo, amene kachisi anamangidwa ndi Mose anali chifanizo chake.

Ulemelero wosayerekezeka wa kachisi wa pansi pano unaonetsera ulemelero woposa wa kachisi wakumwamba komwe Khrsistu Mtsogoleri wathu akutumikira m'malo mwathu pamaso pa mpandowachifumu



wa Mulungu. Komatu choonadi chopambana chokhuza kachisi wakumwamba ndi ntchito yaikuru yomwe ikuchitika kumeneko yokhuza chipulumutso cha munthu, zinaphunzitsidwa kudzera m'mautumiki a kachisi wa pansi pano. Malo opatulika a kachisi wakumwamba anaimiridwa ndi zipinda ziwiri za kachisi wa pansi pano.

Choncho anthu amene anali kuwerenga za chiphunzitso ichi anapeza tanthauzo lenileni la chifukwa chimene kumwamba kunapezekera kachisi. M'chipinda chopatulikitsa muli lamulo la Mulungu, lamulo lomwe ndi lalikuru ndipo mtundu wonse wa anthu umaweruzidwa nalo. Bokosi lomwe mumakhalamo magome a miyala, limabvundikiridwa ndi mpando wa chifundo, pomwe Khristu amachitirapo chotetezera m'malo mwa munthu wochimwa pogwiritsa ntchito mwazi wake. Umu ndimo zikugwirizanira chilungamo ndi chifundo za Mulungu mu nzeru ya chipulumutso cha munthu.

Choncho funso lakuti, Kodi kachisi ndi chiyani? Likuyamkhidwa kudzera m'Mau a Mulungu. Liu kachisi, monga momwe limagwiritsidwira ntchito m'Bukhu Lopatulika, poyamba limatanthauza kachisi amene anamangidwa ndi Mose, amene anali chifanizo cha zinthu za kumwamba; ndipo kachiwiri limatanthauza "kachisi woona" Kumwamba amene kachisi wa pansi pano anali kulozera za iye. Pa imfa ya Khristu mautumiki a zinsembe [pa dziko lapansi] anathetsedwa. Kumapeto kwa nthawi ya masiku 2300, m'chaka cha 1844, panali palibe kachisi pa dziko lapansi kwa zaka mazanamazana.

Koma pali funso lina lofunikira kwambiri lakuti liyankhidwe: Nanga kuyeretsedwa kwa kachisi ndi chiyani? Kodi kumwamba kuli chinthu chodetsedwa chofunika kuyeretsedwa? M'Ahebri 9, kuyeretsedwa kwa akachisi onse awiri, wa pa dziko lapansi ndi wakumwamba kukufotokozedwa momveka bwino. Kuyenera uku kuchitika kudzera mu utumiki wa zinsembe ndi wa mwazi wobvomerezeka. Kuchotsedwa kapena kulifufuta tchimo ndi ntchito yomwe iyenera kuchitidwa moyenera. Nanga pali kulumikizana kotani pakati pa tchimo ndi kachisi? Utumiki wa kachisi wa dziko lapansi unali ndi magawo awiri; wansembe amatumikira tsiku ndi tsiku m'chipinda chopatulika, komanso mkuruwansembe amachita utumiki wapadera wachitetezero wakuyeretsa kachisiyo kamodzi pa chaka m'chipinda chopatukitsitsa. Tsiku ndi tsiku munthu amene walapa machimo ake amabweretsa chopereka chake cha nyama pakhomo la chihema, naika manja ake pamutu pa nyamayo, ndi kutchula machimo

ake. Kenaka nyamayo imaphedwa. Wansembe amatenga mwazi wa nyamayo kulowa nao ndi kuuwaza m'chipinda chopatulika. Pakutero zimaimira kuti tchimo limatengedwa kulowa m'kachisi kudzera m'mwazi. Umu ndimo ntchito ya kukhululukidwa kwa tchimo imachitidwira tsiku ndi tsiku kwa chaka cha tunthu. Umunso ndimo machimo a Aisrayeli amatengedwera kulowa nao m'kachisi ndipo kumapeto a chaka ntchito ya padera ya tsiku la chitetezero, yakuyeretsa kapena yakufufuta machimo m'kachisiyo imachitika.

Kamodzi pa chaka, pa tsiku lalikuru la chitetezero, wansembe amalowa m'chipinda chopatulikitsa kukagwira ntchito yoyeretsa kachisi. Mkuru wansembe m'malo mwa khamu lonse amatenga chopereka, nalowa m'chipinda chopatulikitsa ndi mwazi wa nyama yoperekedwa nsembe ndi kuwaza uwu pa mpando wachifundo, ndi pa malamulo kuchita chotetezera monga momwe zinayenera kukhalira. Ichi chomwe chinachitidwa kuimira chenichenicho, m'kachisi wa dziko lapansi, chikuchitikabe pano mu utumiki wa kachisi wakumwamba.

Utumiki wa wansembe wa chaka chonse m'chipinda chopatulika umaimira utumiki umene Khristu akupitiriza kuuchita pamene anakwera kumwamba. Iye panopa akutetezerabe m'malo mwa ochimwa ndi mwazi wake pamaso pa Atate ndipo chikhulupiriro cha ophunzira ake chinamtsatira komweko Iye amene anakwera kuchoka pamaso pao. Ndi chikhulupiriro chao'chi mu izi, chikhazikika chiyembekezo chao.



Kwa zaka mazana khumi ndi asanu mphambu atatu ntchito yotumikira inakhala ikuchitika m'chipinda chopatulika cha kachisi. Monga momwe zinachitikira ndi mautumiki a kachisi wa dziko lapansi kuti pamakhala tsiku la utumiki wapadera wa chitetezero kumapeto kwa chaka, kudzachitika kuti isanatsekedwe ntchito ya Khristu yakukhala Nkhoswe ya chipulumutso cha anthu, padzakhala ntchito ya kuyeretsa ndi kuchotsa uchimo m'kachisi. Uwu ndi utumiki umene unayamba pamene panathera masiku 2300. M'pangano latsopano machimo a munthu wochimwa amaikidwa pa Khristu mwa chikhulupiriro ndi kutengedwera ku kachisi wakumwamba. Kuyeretsa kotsiriza kwa kachisi wa kumwamba kudzachitika pakudzachotsa kapena kufufuta machimo amene analembedwa. Koma ichi chisanachitike, padzayamba pakhala kufufuza m'mabukhu momwe machimo analembedwamo kuti ndi anthu ati amene kudzera m'kubvomereza, analapa, ndipo mwa chikhulupiriro mwa Khristu, ayenera kulandira chilungamo chake.

Choncho kulungamitsidwa kwa kachisi kukuphatikiza mkati mwake ntchito yakufufuza, - ntchito ya chiweruzo. Ntchito iyi iyenera kuchitika patsogolo kubwera kwa Khristu kwachiwiri kusanachitike. Umu ndimo anthu amene anatsatira bwino kuunika kwa mau a ulosi'wu anachimverera chiphunzitso ichi kuti m'malo mobwera pa dziko lapansi pa kutha kwa nthawi ya masiku 2300 m'chaka cha 1844, Khristu anakalowa m'chipinda chopatulikitsa cha kachisi wa Kumwamba, komwe akuchita ntchito yotsiriza ya kutetezera, kukonzekera kubwera kwake.

## *12. Chiweruzo Chakufufuza*

Chiphunzitso cha kachisi chili pfungulo amene anatsegula chinsinsi cha kukhumudwitsidwa kwa 1844. Chinathandizira kuchiika poyera chinsinsi chonse cha choonadi, ndi kulumikizana kwa kuti dzanja la Mulungu ndilo linatsogolera kukhazikitsidwa kwa gulu la anthu limene linayamba kulalikira mwamphamvu za Kubweranso kwa Khristu ndi kuphunzitsa chimene chinayenera kuchitika nthawi ino, popeza chiphunzitsochi chinapereka kuwala ndi momwe anthu a Mulungu anayenera kuigwirira ntchitoyo. Uthenga uwu wakuchenjeza ndi kuphunzitsa unayenera kuperekedwa ku mpingo.

Anthu amene adzakhale ndi moyo pa nthawi imene ntchito yakutetezera ya Khristu idzatsekedwe m'kachisi Kumwamba, adzaima ndi kuyang'anizana ndi Mulungu mwachindunji popanda mtetezi. Choncho miinjiro yao idzayenera kudzakhala yopanda banga, ndipo makhalidwe ao adzayenera kudzakhala oyeretsedwa powazidwa ndi mwazi.

Padzakhala ntchito yapadera yakuyeretsa, ya kufufuta machimo. Podzatsirizika ntchito imeneyi, anthu onse omtsatira Khristu adzakhala atakonzekera kotheratu za kubwera kwake.

Ntchito ya chiweruzo chakufufuza ndi kufufuta machimo idzatsirizika patsogolo pa kubwera kwachiwiri kwa Ambuye. Tsono popeza akufa adzaweruzidwa kudzera m'zolembedwa m'mabukhu, ndi kosatheka kuti machimo adzachotsedwe kufikira mlandu wa munthu aliyense udzakhale utaunikidwa.

Mu utumiki wa m'kachisi wa dziko lapansi, mkuru wansembe, akatha kupereka nsembe ya chitetezero m'malo mwa Aisrayeli, amaturuka ndi kudalitsa mpingo wonse. Khristunso, ku mapeto a ntchito yake ya kukhala nkhoswe, adzaonekera "wopanda chirema kuloza kuchipulumutso" kudzadalitsa anthu ake amene adzakhale akumyembekezera powapatsa moyo wosatha.

Pa nthawi yomwe inaikidwa kukhala ya chiweruzo – yomwenso inali kutsekedwa kwa masiku 2300, m'chaka cha 1844 – ndipo panayamba ntchito ya chiweruzo chakufufuza komanso kufufuta machimo. Anthu onse amene akudzitcha kuti ali otsatira enieni a Khristu ayenera kudzera pa chipata chakufufuzidwa mwakuyachi.

"Ndinapenyerera," anatero mneneri Danieli, "mpaka anaikapo mipando yachifumu, nikhalapo Nkhalamba ya kale lomwe. ... "woweruza mlandu anakhalapo, ndi mabuku anatsegulidwa." *Danieli 7:9, 10.* Umu ndimo mneneriyu anaonetsedwera m'masomphenya za tsiku lalikuru ndi loopsya pamene makhalidwe ndiponso ntchito za munthu wina aliyense zidzaikidwe poyera pamaso pa Woweruza wa dziko lonse lapansi, kuti munthu ali yense adzalandire mphotho "monga mwa ntchito zake."

Nkhalamba ya kale lomwe ndi Mulungu Atate. Ndi Iye amene ali magwero a umulungu wonse, ndiponso maziko a malamulo ake onse; ndipo ndi Iye amene adzapereka chiweruzo. "Taonani, anadza wina ndi mitambo ya kumwamba wina ngati mwana wa munthu, nafika kwa Nkhalamba ya kale lomwe; ndipo anamyandikizitsa pamaso pake." Kudza kwa Khristu komwe kukufotokozedwa apa sikubwera kwake kwachiwiri pa dziko lapansi. Uku ndi kudza komwe kunanenedwa mu ulosi kuti kudzachitika kumapeto kwa masiku 2300, m' chaka cha 1844. Kudza uku kunali kwakuti Wansembewamkuru wathuyu amalowa malo opatulikitsa, ndipo kumeneko anaonekera ali pamaso pa Mulungu Atate, kupitiriza kuichita ntchito yake yotumikira mtundu wa anthu kotsiriza, - kunali kukaiyamba ntchito yake ya chiweruzo chakufufuza ndiponso ya chitetezero cha iwo amene ali oyenera kupindula ndi utumiko wake.

Umu ndimo zidzachitikire pa tsiku lalikuru ndi lotsiriza la kuyeretsa ndi la chiweruzo chakufufuza, anthu amene adzapindure ndi ntchito'yi adzakhala okha'wo omwe ali ana enieni a Mulungu. Chiweruzo chotsiriza cha anthu oipa chomwe ndi chosiyana ndi ichi, chidzachitika pambuyo pa ichi.

Mabukhu a umboni Kumwamba, momwe munalembedwa maina ndi ntchito za anthu, ndiwo akugwiritsidwa ntchito pa chiweruzo chakufufuza'chi. Chiweruzo'chi chikuchitika pano m'kachisi wa kumwamba. Kwa zaka zoposa makumi anai tsopano chiweruzo'chi chiri mkati kuchitika. Posachedwa – palibe yemwe akudziwa kuti ndi liti – chiweruzochi chidzayamba kuchitika pa anthu a moyo. [Bukhu la Great Controversy likumasulidwa'li linalembedwa m' 1844. Mwa chifundo cha Mulungu nthawi yapatsidwabe chifukwa cha inu ndi ine]. Pamene ntchito ya chiweruzo chakufufuza idzafika pamapeto, mbali ya munthu ali yense idzakhala itadziwika kaya ya ku moyo wosatha kapena kuimfa. Nthawi ya chitetezero idzatha patatsala pang'ono kuti Ambuye aonekere m'mitambo ya kumwamba. "Chifukwa chake dikirani ... kuti angabwere balamanthu, nakupezani muli m'tulo." Marko 13: 35-36.

## *13. Lamulo la Mulungu Losasinthika*

"Ndipo anatsegulidwa Kachisi wa Mulungu amene ali m'Mwamba; ndipo linaoneka likasa la chipangano chake." Chibvumbulutso 11:19. Likasa la malamulo a Mulungu liri m'chipinda chopatulikitsa chomwenso ndi chachiwiri cha Kachisi wakumwamba. M'kachisi wa dziko lapansi, chipinda ichi chimatsegulidwa pa tsiku lalikuru la kutsekedwa kwa chitetezero, kuti kachisi ayeretsedwe. Choncho mau akuti kachisi anatsegulidwa m'Mwamba, ndipo likasa la chipangano chake linaonekera, akutanthauza kutsegulidwa kwa kachisi wakumwamba komwe kunachitika ' 1844. Anthu amene mwa chikhulupiriro anamtsatira Mkuruwansembe wao pomwe amaiyamba ntchito yake ya m'chipinda chopatulikitsa'yo, akutha kumvetsetsa bwino za likasa la umboni wake.




Likasa limene linali m'kachisi wa dziko lapansi mumakhalamo magome awiri a miyala, pomwe panalembedwa malamulo khumi a Mulungu. Choncho malamulo a Mulungu m'kachisi wa kumwamba ali khalidwe lenileni la Mulungu kuchokera komwe malamulo'wo anatengedwa. Anthu onse amene afikira pa chidzalo cha chiphunzitso chopambanachi ndi okha'wo angamvetsetse za chiyero, ndi kusatheka kwakuti chikhalidwe cha lamulo la Mulungu chingasinthike. Lamulo la Mulungu, pokhala bvumbulutso la chifuniro chake, komanso chikhalidwe chake chenicheni, ndi la myaya.

Pakati penipeni pa lamulo limene'li kuyambira kale Mulungu anati, "Uzikumbukira tsiku la Sabata, likhale lopatulika ... tsiku la chisanu ndi chiwiri ndilo Sabata la Yehova Mulungu wako." *Eksodo 20:8-11.* Chitsimikizo chinafikira anthu onse amene analiphunzira Bukhu Lopatulika m'zaka za m'ma 1844, kuti mosadziwa iwo anali kuswa malamulo a Mulungu posasunga tsiku lakupumula la Mlengi. Pamene anaturukira ichi, mitima yao inadzazidwa ndi chisoni, ndipo anatsimikizika mtima kuti sadzaswanso malamulo a Mulungu'wo nayamba iwo kusunganso Sabata lake kukhala lopatulika.

Palibe munthu angalephere kumvetsetsa kuti ngati kachisi wa dziko lapansi anali chifanizo cha kachisi wa kumwamba, ndiye kuti malamulo omwe anasungidwa m'likasa la pa dziko lapansi ndi omwewo ali chikhalidwe cha Mulungu m'likasa la Kumwamba; ndiponso kuti kuchibvomereza choonadi cha kachisi wakumwamba kukuphatikizanso kubvomereza zonse zimene malamulo a Mulungu akunena za udindo wa munthu wakusunga Sabata la lamulo lachinai la malamulo khumi. Apa chikuonetsedwa chinsinsi chachikuru. Khristu anatsegula chitseko, kapena kuti utumiki, wa m'chipinda chopatulikitsa, ndipo kuwala kochokera pa khomo la kachisi m'Mwamba kunaonekera; ndipo lamulo la chinai linaonetsedwa kuti liri chikhalire limodzi la malamulo khumi omwe ali chikhalire angwiro m'kachisi wa Kumwamba.

Anthu amene anakulandira kuwala kwa chiphunzitso chakuti pano Khristu akugwira ntchito yotetezera munthu, ndiponso chakuti lamulo la Mulungu ndi la kunthawi zonse,

kunapatsidwanso kwa iwo kumvetsetsa za choonadi chomwe chiri pa Chibvumbulutso 14:6-12. Kwa iwo mau akuti, "Pakuti yafika nthawi ya chiweruzo chake," akutanthauza za kutsekedwa kwa ntchito ya utumiki wa Khristu ya chipulumutso cha anthu.

Ntchito ya chiweruzo chakufufuza, imene inayamba m' 1844, iyenera kupitirira kufikira mlandu wa munthu aliyense utaweruzidwa, wa magulu onse awiri a anthu a moyo ndi akufa; ndipo idzapitirira mpaka nthawi yakutsekedwa kwa chitetezero cha mtundu wa anthu.

Tsono pakufuna kukonzekera za chiweruzo'chi, nkofunikira kuti anthu adzisunga malamulo a Mulungu. Malamulo amenewa'tu ndiwo adzakhale muyeso wa munthu aliyense pa chiweruzo. Chikhulupiriro ndi chofunikanso ngati munthu akufuna kusunga malamulo a Mulungu moyenera.

Mu uthenga wa mngelo woyamba, anthu akuuzidwa, *"Opani Mulungu, mpatseni ulemelero,"* ndi kumlambira Iye monga Mlengi wa za m'mwamba ndi dziko lapansi. Kuti anthu'wo achite ichi mwangwiro, ayenera choyamba kusunga malamulo a Mulungu. Popanda kusunga malamulo ake, palibe kupembedza kungakhale kokondweretsa Mulungu. Chompembedzera Mulungu ndi chakuti Iye ali Mlengi, ndipo kudzera mwa Iye zinthu zonse zinakhala. Angelo oyera a Kumwamba akupereka chifukwa chimene amamlambirira Mulungu pakunena, "Muyenera Inu, Ambuye wathu, ndi Mulungu wathu, kulandira ulemelero ndi ulemu ndi mphamvu; chifukwa mudalenga zonse." *Chibv. 4:11.*

Limodzi la malamulo khumi limanena mwa chindunji kuti Mulungu ndi Mlengi. Lamulo lachinai'li likuti, "Tsiku lachisanu ndi chiwiri ndilo Sabata la Yehova Mulungu wako." *Eksodo 20:10.* Ndipo popitiriza kufotokoza za Sabata'lo Ambuye akuti, "ndipo (masabata) adzakhala chizindikiro pakati pa Ine ndi inu, kuti mudziwe kuti Ine ndine Yehova Mulungu wanu." *Ezekieli 20:20.*

Kufunikira kwa Sabata monga chikumbutso cha chilengedwe ndi kwakuti limapatsa tanthauzo lenieni la chifukwa chimene Mulungu amayenera kupembedzedwera. Kunali kufuna kuti choonadi ichi chidzikhala m'mitima mwa anthu nthawi zonse kuti Mulungu analipereka tsiku'li m'Edeni; ndipo pozindikira kuti Mulungu ali chikhalire Mlengi wathu, ife tipitirize kumlambira Iye, ndipo ili lidzapitirira kukhala chikumbutso ndi chizindikilo ku nthawi zonse. Kusunga Sabata kulinso chizindikilo cha kum'zindikira ndi kupereka ulemu kwa Mulungu woona.

Pakufuna kulekanitsa iwo amene akusunga malamulo a Mulungu ndi chikhulupiriro cha Yesu, mngelo wachitatu akufotokoza za gulu lina la anthu omwe akuwachenjeza mwa mphamvu za kusayeruzika kwao m'mau akuti, *"Ngati wina alambira chirombocho, ndi fano lake, nalandira lemba pamphumi pake, kapena pa dzanja lake, iyenso adzamwako ku vinyo wa mkwiyo wa Mulungu." Chibv. 14:9-10.* Kodi mau akuti **chirombo, fano, lemba** amaimira chiyani? Mau amenewa akuyendera limodzi ndi mau a ulosi wa pa Chibvunbulutso 12 onena za chinjoka chomwe chanafuna kumupha Khristu pa nthawi ya kubadwa kwake. Pamene liu chinjoka kwenikweni likutanthauza Satana, komanso likuimiranso ulamuliro wa Aroma wa chikunja. Pa mutu 13 chikufotokozedwa chirombo china chomwe, "chinafanana ndi nyalugwe," chizindikilo chomwe a mipingo yambiri ya Mpanduko anati chikutanthauza mchitidwe wa upapa. "Ndipo chinatsegula pakamwa pake kukanena za mwano pa Mulungu, kuchitira mwano dzina lake. Ndipo anachipatsa icho kuchita nkhondo pa oyera mtima." *Chibvumbulutso 13:6-7.* Chirombo chafotokozedwa m'ulosi uwu ndi chomwenso chikutchedwa **kanyanga kakang'ono** pa Danieli 7. Nthawi ya miyezi makumi anai mphambu iwiri ndi yokhayokhayo yomwe ikudziwikanso ndi "nthawi imodzi ndi nthawi zina ndi nthawi ya nusu," kuimira zaka zitatu ndi theka, kapena masiku 1260 za pa Danieli 7 – nthawi imene ulamuliro wa upapa unazunza ndi kupondereza anthu a Mulungu.

Pa nthawi yokhayokhayo chizindikiro china chinaonetsedwa, "Ndipo ndinaona chirombo china chiri kururuka pansi; ndipo chinali nazo nyanga ziwiri ngati za mwana wa nkhosa, ndipo chinalankhula ngati chinjoka." *Chibv. 12:11.* Mneneri Danieli anawafotokoza maulamuliro amene anakhalako kale pa dziko lapansi kuti anali zirombo zoononga zomwe zinauka pambuyo pa, "mphepo zinai za mumlengalenga zinabuka pa nyanja yaikuru." Dan. 7:2. Madzi amaimira, "anthu pamene mphepo zikuimira kulimbana." Chirombo "chiri kuturuka pansi," chinayenera kuchokera m'dziko limene silinakhalidwe ndi anthu ndi kale lonse, ndipo chinakula pang'onopang'ono ndi mwakachetechete.

Monga linaukadi pfuko m'Dziko Latsopano m'chaka cha 1798 lomwe linakhala ndi likukula pang'onopang'ono mu mphamvu, ndi likhala ndi chiyembekezo ndiponso chipambano, zomwe zinakopa chidwi cha dziko lonse lapansi? – Dziko la Amerika wa Mgwirizano (USA), lomwe nyanga ziwiri mu ulamulirowu zinaimira utsopano, ubwino ndi kufatsa. Akhristu oyambirira pothawa chizunzo ku Ulaya anafika ku Amerika, anakhazikitsa boma limene maziko ake anali ufulu wakulekanitsa kotheratu kwa ntchito za boma ndi za chipembedzo. "Ndipo chinalankhula ngati chinjoka." "Nyanga zokhala ngati nkhosa" ndi "mau okhala ngati a chinjoka" akuimira ndi kufotokoza motsutsana pakunena za makhalidwe ndiponso maonekedwe a pfuko limene lanenedwa'li. Ulosi wakuti pfuko'li lidzalankhula "ngati chinjoka," ndi kuchita "ulamuliro wonse wa chirombo choyamba," unali kulosera za kuzunza, ndiponso kupondereza choonadi. Pfuko limeneli lidzakhazikitsa malamulo oumiriza anthu kuchita zofuna za mchitidwe wa upapa. "Ndikunena kwa iwo akukhala padziko, kuti apange fano la chirombocho." *Chibv. 13:14.*

Fano la chirombo lipangidwa ndi chirombo cha nyanga ziwiri. Kuti timvetsetse za chimene fano liri, ndiponso momwe lidzapangidwire, tiyenera kuwerenga za makhalidwe a chirombo cheni chake, - Mchitidwe wa Upapa. Pamene mpingo wa pa chiyambi unasokonekera pochoka m'choonadi chosabvuta kuchimvetsetsa cha Uthenga Wabwino, unafuna chithandizo cha ulamuliro wa dziko. Chotsatira chake chinakhala ulamuliro wa upapa momwe mpingo unayamba kulamulira za ndale, ndi kugwiritsa ntchito mphamvu za boma kukwaniritsa zofuna za mpingo'wo, makamaka pofuna kukhaulitsa anthu "otsutsana nawo." Pamene mpingo unakwaniritsa kulamulira boma unagwiritsa ntchito mphamvu za boma'lo kuzunza anthu amene anatsutsana ndi ziphunzitso zake.

Pamene mipingo ikuruikuru ya dziko la America wa Mgwirizano, idzagwirizana kutsatira ziphunzitso zomwe ndi zofanana pakati pao, idzakakamiza Boma kupanga malamulo oitchinjiriza kuti isagawanike, kudzangochita ichi kudzakwaniritsidwa kuti Amerika wa Mpatuko wathandizira kupanga fano la mchitidwe a Mpingo wa Aroma. Chirombo cha nyanga ziwiri, "chichita (chilamulira) kuti onse, ang'ono ndi akuru, achuma ndi osauka, ndi mfulu ndi akapolo, alandire chilembo." *Chibv. 13:16.*

Chenjezo la mngelo wachitatu ndi lakuti, "Ngati wina alambira chirombo ndi fano lake, nalandira lemba pamphumi pake, kapena pa dzanja lake, iyenso adzamwako ku vinyo wa mkwiyo wa Mulungu." Chirombo chimene chatchulidwa mu uthenga uwu, chomwe anthu adzachipembedza pokakamizidwa ndi chirombo cha nyanga ziwiri, ndi choyamba chija, kapena kuti chija chinafanana ndi nyalugwe m'maonekedwe ake cha pa Chibvumbulutso 13:1-8 – chomwe ndi mchitidwe wa upapa. *"Fano la chirombo"* likuimira machitidwe opandukira Mulungu a mipingo ya Mpanduko omwe adzachitika pamene mipingo ya Mpanduko'yo idzafuna chithandizo cha boma chokakamiza anthu kuchita za ku mtima kwao.

Anthu amene akusunga malamulo a Mulungu, adzasiyanitsika ndi iwo amene akulambira chirombo ndi fano lake ndi kulandira chilembo chake. Kusunga ndi kuswa malamulo a Mulungu kudzatsimikizika pakati pa anthu opembedza Mulungu ndi iwo opembedza chirombo.

Makhalidwe apadera a chirombo ndiponso a fano lake, ndiwo kuswa malamulo a Mulungu. Ndi pakusintha malamulo a Mulungu pomwe mchitidwe wa upapa unayamba kudzitamandira kuti mphamvu zake ndi zoposa za Mulungu. Choncho kumvera ndi kuchita malamulo okhazikitsidwa ndi mchitidwe umenewu ndiko kulandira chilembo ndi kumkweza papa m'malo mwa Mulungu. Lamulo la chinai linasinthidwa kukhala pa Sunday, tsiku loyamba la pa sabata m'malo mwa Saturday, Sabata la tsiku lachisanu ndi chiwiri. Iye "*adzayesetsa* kusintha nthawizo ndi chilamulo." Kusinthidwa kwa lamulo la chinai la malamulo khumi kukukwaniritsa ulosi uwu..



Anthu opembedza chirombo adzadziwika ndi machitidwe ao osasamala za chikumbutso cha chilengedwe cha Mlengi, nadzakweza malamulo a mpingo wa Aroma. Bukhu Lopatulika likufotokoza bwino za tsiku lachisanu ndi chiwiri kuti ndilo tsiku la Ambuye osati tsiku loyamba la pa sabata. Ichi ndi chinthu chimene ngakhale a mipingo ya Mpanduko akuchibvomereza kuti palibe pamene Mau a Mulungu akutiuza za kusinthidwa kwa tsiku la Sabata. Choncho pakusunga Sunday mokhulupirika a mipingo ya Mpanduko'wo akubvomereza ulamuliro wa mpingo osati wa Mulungu. Mpaka pano mpingo wa Aroma sukubvomereza ndi kulapa ngakhale pang'ono zakudzinamiza kwake kuti uli ndi mphamvu kuposa Mulungu. Pakutsatira maphunzitso olakwika'wa, a mipingo ya Mpanduko akukana kuchita molingana ndi malangizo amene akanawathandiza kudzilekanitsa ndi mpingo wa Aroma, - omwe ndi "Bukhu Lopatulika, ndi Bukhu Lopatulika lokha, lomwe ndi maziko a chipembedzo chao." "Pakusunga Sunday akhristu a Mpanduko akupereka ulemu ku ulamuliro wa mpingo [Katolika], chinthu chomwe sanayenera kutero" *(Plain Talk about Protestantism," p. 213).*

Kukakamizidwa kwakuti anthu adzisunga Sunday m'dziko la Amerika wa Mgwirizano kudzakhalanso komweko kukakamiza kuti anthu adzilambira chirombo ndi fano lake. Pamene lamulo la Sunday lidzakakamizidwa mwa lamulo, ndi pomwe anthu a dziko lapansi adzayambe kumvetsetsa za kufunikira kwa kusunga Sabata loona, ndipo ali yense amene adzasankhe kuphwanya malamulo a Mulungu, ndi kupitiriza kusunga malamulo amene si Mulungu amene anawapereka koma Mpingo wa Aroma, pakutero adzakhala akupatsa ulemu mchitidwe wa upapa osati Mulungu. Woteroyo adzalandira chizindikiro chakuti ali pansi pa ulamuliro wa Aroma – womwe ndi "lemba la chirombo."

Uthenga wochititsa mantha kwambiri umene sunayambe walalikidwa kwa munthu ali yense ndi uja wopezeka m'mau a mngelo wachitatu. Ulosi'wu ukufotokoza kuti mngelo woyamba adzalalikira ku "mtundu uli wonse ndi pfuko, ndi manenedwe ndi anthu." Koma mau akuchenjeza a mngelo wachitatu omwe alinso mbali ya uthenga wa angelo atatu, unakhuzana ndi chenjezo lopita kwa munthu ali yense pa yekha. Ndipo pa mkangano uwu chipembedzo cha Chikhristu pa dziko lonse lapansi chidzagawika magulu akulu awiri, - gulu la iwo akusunga malamulo a Mulungu ndi chikhulupiriro cha Yesu, ndi gulu la iwo akupembedza chirombo ndi fano lake

nalandira lemba lake. Anthu a Mulungu adzakanitsitsa kulandira lemba. A mipingo ya Mpanduko panopa akuonetsa chidwi ndi kuyandikira kwambiri ku chipembedzo cha Aroma kuposa momwe zinthu zakhala zikuchitikira m'zaka za m'mbuyomu. Iwo akumadzinamiza m'maganizo ao pakunena kuti, "ndiponso, sitikusiyana kwenikweni pa ziphunzitso zina ndi zina zomwe ndi zofunikira kwambiri, ndipo kuti kufewetsa ziphunzitso kwathu ndi kugwirizana ndi mpingo wa Aroma, kudzaupanga mpingowu kutimvetsetsa ndi kusinthika." Kodi anthu amene akuganiza chomwechi'wa akukumbukira kuti chimodzi cha ziphunzitso za mpingo wa Aroma'wu kwa zaka mazana asanu ndi anai tsopano chakhala chiri chakuti mpingowu ndi utsogoleri wake samachimwa? Nanga zingakhale zotheka bwanji kwa mpingo'wu kuwamvetsetsa a mipingo ya Mpanduko ndi kusintha machitidwe ake omwe akhala ali maziko ake kwa zaka zonse za m'mbuyomu?

Talekani malamulo oyendetsera maboma adziko lapansi asinthe, ndipo mpingo wa Aroma upatsidwenso mphamvu monga unali nazo pa chiyambi, mwamsangamsanga udzayambanso machitidwe ake a upandu ndi ozunza, opondereza anthu onse otsutsana nawo. "Sitidzasunga chikhulupiriro ndi malonjezano pokakamizidwa ndi anthu oukira." Mpingo'wu umatero. Inde pakhala pali kukonzanso mu mpingo wa Aroma; koma kusintha kumeneku sikukukhuza mchitidwe wa upapa ai. Ngakhale mpingo'wu umanyadira kuti uli m'kuunika, koma sumafuna konse kukhala m'chidziwitso cha Mau ndiponso mphamvu za Mulungu. *Chinthu chimene atsogoleri ake ndi anthu owatsatira akuchilakalaka kwambiri nthawi zonse ndicho kupeza njira zimene zingawapangitse anthu kuiwala Mulungu, koma m'maonekedwe ndi machitidwe ake zidzikhala ngati zomkumbukirira Iye.* Machitidwe a upapa akhazikika ndi kufunitsitsa atakwaniritsa kuipa uku konse.

Pano iwo ali mkati mwakuyesetsa kuti aipeze njira youtenga ulamuliro wa dziko la Amerika womwe ndi wa mipingo ya Mpanduko umene mpingo wa Aromawo unautaya m'dziko lapansi la kale. Ndipo chomwe chipangitse kuti zonse zitheke chidzakhala kukakamizidwa kwa lamulo la kusunga Sunday monga tsiku lakupembedza, - limene mpingo wa Aroma unalikhazikitsa, ndiponso umadzitamandira kuti liri chizindikilo cha ulamuliro wake. Mpingo wa Aroma umakanitsitsa mwatchutchutchu kuti sudzasintha machitidwe ake ku nthawi zonse. Talekani malamulo a dziko la Amerika wa Mgwirizano asinthidwe ndi kubvomereza kuti mpingo ukhale ndi mphamvu zakulamulira Boma; ndiponso kuti malamulo a dziko ayambe kulamulira za kayendetsedwe ka ntchito za chipembedzo muone.

## *14. Kuyambanso Kusunga Tsiku la Mpumulo wa Mulungu*

Ntchito yakukonzanso kasungidwe ka Sabata moyenera idzatsirizika m'masiku otsiriza. "Wodala munthu amene achita ichi, ndi mwana wa munthu amene agwira zolimba ichi, amene asunga Sabata osaliipitsa, nasunga dzanja lake osachita nalo choipa chiri chonse. Yense amene asunga Sabata osaliipitsa, nagwira zolimba chipangano changa. Naonso ndidzanka nao ku phiri langa lopatuilka." *Yesaya 56:2, 6, 7.* "Manga umboni, mata chizindikilo pachilamulo mwa aphunzi anga." *Yesaya 8:16.*

Chizindikilo cha lamulo la Mulungu chikupezeka mu lamulo lachinai. Ili ndi lamulo lokhalo la malamulo khumi momwe mukupezeka dzina ndi udindo za Iye amene anapereka lamulo'lo. Palibenso lamulo lina lomwe likufotokoza kuti lamulo linaperekedwa ndi Mulungu kuposa ili. Pamene Sabata linasinthidwa ndi ulamuliro wa Papa, chizindikilo chinachotsedwa pa chilamulo. Lamulo la Mulungu ndi la ngwiro ndipo kudzera mwa ili malingaliro, ziphunzitso ndi mau ena ali onse zimaweruzidwa.

"Udzautsa maziko a mibadwo yambiri; udzatchedwa Wokonza pogumuka, Wakubwezera njira zakukhalamo. Ukaletsa phazi lako pa Sabata, ndi kusiya kuchita kukondwerera kwako tsiku langa lopatulika, ndi kuyesa Sabata tsiku lokondwa." Mau awa anaperekedwa mu lamulo lamphamvu lomwe kudalitsika kwake kunaonekera pamene Mlengi anapumulanso, ndi kulidalitsa, ndipo Sabata linasungidwanso ndi Adamu. Kuyambira tsiku limene linaperekedwa mpaka lero lino, chidziwitso cha lamulo la Mulungu chakhala chiripo, ndipo Sabata la lamulo lachinai la malamulo khumi lakhala likusungidwa. Sabata ndi masungidwe ake zakhala ziri zamyaya ndiponso za ponseponse, *ndipo ndi zakale monga dziko lapansi.* Ichi nchifukwa chake lamulo ili liyenera kusungidwa ndi kulemekezedwa. Ilo silinakhazikitsidwa ndi chifuniro cha munthu, ndipo siliri monga mwa miyambo ya umunthu. Linalengedwa ndi Nkhalamba yakaleyo ndi kulamulidwa m'Mau ake kuti lidzisungidwa ku nthawi zonse.

## *15. Machenjerero a Chinyengo*

Kuyambira pachiyambi mu mbiri yakulengedwa kwa munthu, Satana wakhala akuchita machenjerero osiyanasiyana ndi cholinga chofunitsitsa kusokeretsa mtundu wathu. "Mkaziyo ndipo anati kwa njoka, Zipatso za mitengo ya m'mundamu tidye. Koma zipatso za mtengo umene uli m'kati mwa munda, Mulungu anati, Musadye umenewo, musakhuze umenewo, mungadzafe. Njokayo ndipo inati kwa mkaziyo, Kufa simudzafai." *Genesis 3:2-4.* Pamene Adamu anachimwa, anadzilekanitsa mwini yekha ndi chipatso cha mtengo wamoyo, ndi kudzitengera imfa. Moyo wosatha umene unalonjezedwa kwa munthu kudzera pakumvera, unataika mwa kusayeruzika.

Ndi kudzera mwa Khristu kokha komwe tingapeze nako moyo wosatha. Onse "amene afunafuna ulemelero ndi ulemu ndi chisaonongeko," adzalandira moyo wosatha *(Aroma 2:7).* Ndi wosokeretsa wa mkuru yemweyu amene anamlonjeza Adamu kuti adzakhala ndi moyo wosatha ngakhale atakhala chikhalire mu uchimo. Iye anati kwa Hava m'munda wa Edeni, "kufa simudzafai," – ndi mau okha'wo omwe akupezeka m'Bukhu lonse Lopatulika akulonjeza za umyaya wa moyo kwa anthu ochimwa. Chiweruzo cha Mulungu ku moyo wochimwa uli wonse ndi chakuti, "Moyo wochimwawo ndiwo udzafa" mau omwe Satana motsutsana ndi Mulungu anawatembenuza kuti moyo wochimwa sudzafa, koma udzakhala ku nthawi zonse. Munthu atangochimwa palibe mwana wa Adamu ndi m'modzi yemwe amene analoledwa kudyanso chipatso cha moyo. Chifukwa cha ichi palibe munthu ndi m'modzi amene sadzafa.

Satana analamulira angelo ake kuti ayesetse kuchisokoneza chikhulupiriro cha munthu kuti sadzafa koma adzakhala moyo wakuzunzika myaya. Monga zingathekedi, ngakhale kuti patakhala chikondi kaya chisoni cha mtundu wanji, komanso ngakhale kungoganiza mwa chilungamo, za chiphunzitso ichi chakuti akufa ochimwa adzakhala akuzunzika m'ng'anjo ya moto moyo wao wonse? Iyi inangokhala njira ya Satana yofuna kusokeretsa gulu lalikuru la anthu omwe akukhulupirira m'chiphunzitso cholakwikachi. Iwo akamva choncho amati popeza mtundu wonse wa anthu udzakhala ukuzunzika, Mulungu amene ali wachifundo chosaneneka adzauchitira chisoni ndi kuupulumutsa uli chikhalire mu uchimo. Koma Mulungu sakutero, Iye akutsimikizitsa m'Mau ake m'maumboni ochuruka kuti adzalanga onse olakwira lamulo lake. Imfa ya Mwana wake wopanda banga la uchimo ikutsimikizira kuti "mphotho yake ya uchimo ndi imfa."

Choncho ngati ife tikufuna kudzalandira moyo wosatha, tiyenera kuligonjetsa tchimo. Odala iwo amene akuchita malamulo ake (atsuka miinjiro yao), kuti adzakhale nao ulamuliro pa mtengo wa moyo, kuti adzalowe mu mzinda pa zipata. Ngati Mulungu akuonetsa chilungamo ndi chifundo chake kwa ochimwa, akutero kukupindula kwa chilengedwe chonse, komanso kukupindula kwa iwo amene chiweruzo chake chidzachitika pa iwo. Iwo amene asankha Satana kukhala mtsogoleri wao, ndipo akukhutitsidwa kukhala pansi pa ulamuliro wake, sangadzathe kukhala pamaso pa Mulungu. Monga oterewa angadzathe kukhala limodzi ndi anthu amene anawanyoza ndi kuwazunza pa dziko lapansi? Choncho monga moyo wosatha idzakhala mphotho ya olungamo chomwecho imfa idzakhala cholowa cha anthu osalungama.



Ndi "imfa yachiwiri" yomwe apa ikuyerekezedwa ndi moyo wosatha. "Kudzakhala kuuka kwa olungama ndi osalungama," *Machitidwe 24:15.* Magulu awiri akufotokozedwa m'mau awa. Iwo amene adzatchedwa "oyenera kulandira" mdzukiro wa ku moyo akutchedwa " odala ndi oyera mtima." Pa iwowa imfa yachiwiri iribe ulamuliro." *Chibv. 20:6.* [Gulu linalo] adzalangidwa m'miyeso yosiyanasiyana, "aliyense molingana ndi ntchito zake," omwe mapeto ao adzakhale imfa yachiwiri. "Katsala kanthawi ndipo oipa adzatha psiti. Inde udzayang'anira mbuto yake, nudzapeza palibe." *Mas. 37:10; Obad. 16.* Umu ndimo lidzathetsedwere tchimo, ndi zowawitsa zake zonse.

Chiri chonse cha zolengedwa za m'Mwamba ndi dziko lapansi chidzamveka chikupereka ulemu ndi ulemelero kwa Mulungu. Sikudzakhalanso moyo ndi umodzi umene udzachitiranso Mulungu mwano. Pa chiphunzitso cholakwika chakuti munthu sadzafai pabadwapo chija chakuti munthu wakufa amatha akuona zonse zomwe zikuchitika monga amachitira ali moyo. Kodi Bukhu Lopatulika likuti chiyani za zimenezi? Munthu akafa, "Mpweya wake uchoka abwerera kunka ku nthaka yake. Tsiku lomwelo zotsimikizika mtima zake zitayika." *Mas. 146:4.* "Pakuti amoyo adziwa kuti adzafa, koma akufa sadziwa kanthu bi." *Mlal. 9:5.* "Pakuti muimfa m'mosakumbukira Inu. M'mandamo adzakuyamikani ndani?" "Akufa salemekeza Yehova, kapena ali yense wakutsikira kuli chete." *Mas. 6:5; 115:17.*

Chiyembekezo chakuti munthu sadzafai ndipo kumwalira ndi mdalitso ndi chiyambi cha moyo watsopano chatsogolera anthu ambiri kunyalanyaza choonadi cha Bukhu Lopatulika chonena za m'dzukilo. Yesu anati, "Ndipo ngati ndipita kukakonzera inu malo, ndidzabweranso, ndipo ndidzalandira inu kwa Ine ndekha." "Pakuti Ambuye adzatsika Kumwamba mwini yekha ndi mpfuu, ndi mau a mngelo wamkuru, ndi lipenga la Mulungu; ndipo akufa mwa Ambuye adzayamba kuuka. Ndipo potero tidzakhala ndi Ambuye nthawi zonse." *Yoh. 14:3; 1 Ates. 4:16-18.* Apatu Paulo akunena za mtsogolo, za kubwera kwa Ambuye.

Munthu aliyense asanalandiridwe kwao kwa opulumutsidwa, mlandu wake uyenera kufufuzidwa, ndipo makhalidwe ake ndi ntchito zake ziyenera kuonetsedwa pamaso pa Mulungu. "Chifukwa anapangira tsiku limene adzaweruza dziko lokhalamo anthu m'chilungamo, ndi munthu amene anamuikiratu." *Mach. 17:31.* M'mau awa pa nthawiyo, mtumwiyu amafotokoza mombveka bwino, za mtsogolo, kuti Mulungu anaika nthawi yapadera, ya chiweruzo. Nanga kukanakhala kuti akufa olungama panopa akusangalala kumwamba ndiponso osalungama akukukuta malilime ao m'ng'anjo yotentha moto ndi sulfure, pakanakhala tanthauzo lanji lakuikira chiweruzo chomwe chidzachitika mtsogolo muno? Palibe munthu ndi m'modzi yemwe amati akangofa amapita kumwamba, koma onse ali chigonere mpfumbi kuyembekezera

mdzukilo. *(1 Ates. 4:14; Yobu 14:10-12).* Mu imfa maganizo onse a munthu amasiya kugwira ntchito. Akufa amene aikidwa m'manda amangokhala chete. Amakhala chigonere; iwo adzaukitsidwa pa kulira kwa lipenga la Mulungu ndi kulandira moyo wosatha ngati anali olungama. Pamene iwo adzaukitsidwa ku tulo tao tatikuruto, adzayambanso kuganiza kuyambira pamene analekezera pa nthawi yomwe imfa imawapeza. Chosangalatsa kwambiri ndi chakuti pakudzangouka m'manda, iwo adzapfuula mwa chipambano, Imfawe, mbola yako iri kuti?" *1 Akor. 15:55.*

Chiphunzitso chakuti munthu akamwalira amaona zinthu monga momwe anali moyo, komanso kuti mizimu ya iwo anafa kale imabweranso kudzatumikira anthu a moyo, chiri maziko enieni a chipembedzo cha mizimu ya anthu akufa komanso ya ziwanda lero lino. Angelo akugwa amene amatumikira Satana ndiwo amadzetsa machitidwe awa kuchokera ku dziko la mdima. Ndi Satana amene mwa machenjerero ake amadzetsa machitidwe osokeretsa'wa. Iye amagwiritsa mphamvu zake kubweretsa maonekedwe ngati a anthu kapena bwenzi amene anafa kale kwa abale ao omwe ali moyo. Iye amadzetsa ngakhale maonekedwe a anthu amene anamwalira ali osalungama. Ndipo anthu ongoyerekezedwa'wo amafotokoza kuti akusangalala Kumwamba ndipo palibe kusiyana pakati pa olungama ndi osalungama, pakutero nkumawalimbikitsa anthu a moyo kupitiriza kukhulupirira kuti palibe bvuto ndi m'mene amakhalira m'moyo uno kaya udyo kaya molungama chifukwa onse amalandiridwa kumwamba. Pakutero anthu amachilandira chiphunzitso cholakwikachi komanso kuchiphunzitsa. Anthu akakopeka mtima ndi chiphunzitso chakechi, Satana amalumikizako ziphunzitso zina zomwe cholinga chake chimakhala kufuna kuchotsa chikhulupiriro cha anthu m'Bukhu Lopatulika. Anthu ambiri akhala akupusitsidwa kuti chipembedzo cha mizimu ndi ziwanda ndi machitidwe a umunthu chabe chikhalirecho chiri machitidwe a zozizwa zochitidwa ndi Satana. Satana akusokeretsa anthu monga momwe anachitira ndi Hava m'Edeni, pogwiritsa ntchito machitidwe ndi mau oyamikira, chilakolako chofunitsitsa kukhala ndi chidziwitso choletsedwa, ndiponso pakukweza mtima wakudzimva ndi wakudzikweza. Choncho ndi kofunikira kuti tisamalitse kuti tisasokeretsedwe ndi bodza la dziwanda'li. Mulungu wapereka ku dziko lapansi kuunika kokwanira kowatsogolera anthu kutha kuturukira machitidwe a mizimu yosokeretsawa.

Mulungu mosatopa wakhala akuletsa machitidwe ali onse akulumikizana ndi mizimu ya anthu akufa. Machitidwe ali onse a mtundu uwu ndi onyansitsitsa pamaso pa Ambuye, ndipo akuletsedwa ndi kuti yense wowachita adziphedwa. Machitidwe akupembedza mizimu ya anthu akufa ali chinyengo chachikuru chomwe chikutsogoleranso anthu kubwerezanso za chinyengo chomwe chinachitika kale, koma lero ndiponso ngati kuunika kwatsopano, machitidwe a anyanga ndi ufiti zomwe zinakhala zikuletsedwa m'nthawi zakale zikubweranso mwa mphamvu. Mizimu yoipayi sizikusiyanitsa pakati pa chilungamo ndi chisalungamo ndipo ziwirizi zakuyendetsedwera limodzi. Ndi anthu owerengeka amene angamvetsetse za chinyengo cha Chipembedzo cha Mizimu'chi ndiponso kuopsya kwakukhala pansi pa machitidwe ake. Anthu ena amalowa ichi pongofuna kukwaniritsa umunthu wao. Koma kutero kumakhala kusewera pa msampha pomwe angathe kutaya miyoyo yao mosabvuta, ndi pakutero pomwe mdaniyu amatengerepo mwai wakuononga chikumbumtima chao. "Ndipo pamene iwo adzati kwa iwe, Funa kwa olaula, ndi obwebweta, amene alira pyepye, nang'ung'uza; kodi anthu sadzafuna kwa Mulungu wao? Kuchilamulo ndi kuumboni! Ngati iwo sanena malinga ndi mau awa, ndiye kuti mwa iwo mulibe choonadi."

Anthu ambiri atseka maso ao kukuunika ndi kuyenda mofulumira kulowera ku mdima ponyalanyaza machenjezo omwe akuperekedwa – ndipo Satana nayenso watchera misampha kuwazungulira iwo. Ena adzakhulupirira ndi kulumikizana ndi mizimu ya abwenzi ndi abale ao omwe anafa kale osadziwa kuti ndi ziwanda zomwe zimaonekera kwa iwo osati akufa'wo ndipo ndi izi zomwe zakhala zikufotokoza zinthu zazikuru zokhala ngati za ufumu wakumwamba chikhalirecho ziri ziphunzitso za bodza. Onse amene chikhulupiriro chao ndi chosazikika pa Mau a Mulungu adzasokeretsedwa ndi kugonjetsedwa. Machitidwe akusokeretsa a Satana adzakhala akukulirakulira. Mneneri Yesaya akufotokoza momveka bwino kwambiri za kuopysa kwa chinyengo chimene chidzafika pa osalungama ndi kulandiridwa ndi osokeretsedwa'wa. " Ife tapangana pangano ndi imfa, tabvomerezana ndi kunsi kwa manda." *Yes. 28:15.* Kwa nthawi yaitali Satana wakhala akukonzekera za chinyengo chake chachikuru chofuna kulisokeretsa dziko lonse lapansi – m'Edeni, iye anati, "Simudzafai, mudzakhala ngati milungu."

Monyengerera, iye wakhala akukonzekera za chinyengo chake chachikuru'chi pakukhazikitsa chipembedzo cha mizimu ndi ziwanda. Ndi okhawo amene adzalimbika kukhala mu mphamvu ya Mau a Mulungu mwa chikhulupiriro omwe adzagonjetsa, koma dziko lonse lapansi lidzatengeka kulowa m'chinyengo ichi. "Ndipo pangano lanu ndi imfa lidzathedwa, ndi kubvomerezana kwanu ndi kunsi kwa manda kudzalephereka; popita mliri woopsya udzakuponderezani pansi." Yes. 28:17-18.

## *16. Kulowa M'chisautso Chotsiriza*

Kuyambira pamene mkangano waukuru'wu unayamba Kumwamba, chakhala chiri cholinga cha Satana kulithetsa lamulo la Mulungu. Kunali kufuna kukwaniritsa ichi kuti iye anaukira Mlengi; ndipo ngakhale wanathamangitsidwa Kumwamba, iye wakhala akuipitiriza nkhondo yake pa dziko lapansi pano. Ndipo pofuna kusokoneza lamulo la Mulungu, iye akupitirizabe kukhotetsa ziphunzitso za Bukhu Lopatulika. Mkangano waukuru wotsiriza pakati pa choonadi ndi chisalungamo, udzakhuzanso kulimbana kwa nthawi yaitali komwe kwakhala kukuchitika pa lamulo la Mulungu. Tikulowa tsopano mu nkhondoyo.

Palibe chiphunzitso choipitsitsa mu nthawi ino kuposa ichi chonena kuti lamulo la Mulungu silikugwiranso ntchito pa anthu. Pfuko liri lonse la anthu liri ndi malamulo ake, omwe amayenera kulemekezedwa ndi kutsatidwa; palibe boma lingakhale lolimba ngati liribe malamulo. Umakhala mlandu waukuru munthu akapanda kusamala malamulo a Dziko ndi a mafuko lake, nanga koposa bwanji



kupondereza malamulo a Mulungu omwe ali maziko a maboma onse a dziko lapansi? Malamulo a maboma adziko lapansi amasinthasintha ndipo si a myaya; amalora anthu kuchita zinthu monga akufunira, koposa chotani m'mene Wolamulira wa chilengedwe chonse angachitire ndi lamulo lake, lomwe ndi losasinthika ndipo liri muyeso wakudzudzulira anthu osalungama ndi kuwabwezera iwo kukhala akumvera.

Pamene lamulo la chilungamo cha Mulungu lasiyidwa pambali, njira imatsegulidwa yoti kalonga wa uchimo akhazikitse ulamuliro wake pa dziko lapansi. Pena pali ponse pamene malamulo a Mulungu akukanidwa uchimo umasiya kukhala chinthu choipa kapena chilungamo kukhala chinthu chokhoza. Choncho pamene anthu osalungama azachitira chipongwe olungama amene akusunga malamulo a Mulungu, unyinji wa anthu achipongwewo mwakusankha kwao adzakhala akudziitanira pa iwo eni machenjerero a Satana. Talekani malamulo amene pakali pano akuletsa kuipa kwa anthu ataidwiretu kunja, pomwepo malamulo a umunthu adzakhaliratu osamveredwa. Ngati panopa lamulo la Mulungu linasiya kugwira ntchito pa anthu, nanga ndi chifukwa ninji anthuwo akuopa uchimo?

Ndipo zaonekera kale kuti chiphunzitso chakuti malamulo a Mulungu ndi osafunikira pa anthu, chadzetsa chifooko pa chikhalidwe chabwino ndi kutsegula zitseko za kusayeruzika pa dziko lapansi. Mchitidwe ndi malamulo onse a za chipembedzo omwe akhala ali maziko akukhalirana bwino kwa anthu, asokonekera ndi kukhala opanda pake, ndipo kwangokhala kuti ataidwe osawayang'ana nkomwe. "Kuchilamulo ndi ku umboni! Ngati iwo sanena malinga ndi mau awa, ndiye kuti mwa iwo mulibe choonadi." *Yes. 8:20.* Ndi chinthu chofunikira kuti anthu adzikhala ndi choonadi cha Bukhu Lopatulika; chifukwa ziphunzitso zake zimaonetsera poyera za chinyengo cha Satana.

Mwa umunthu palibe angasiyanitse ziphunzitso za Satana zomwe iye wayesetsa kuzifananitsa ndi za m'Bukhu Lopatulika pokhapokhapo pogwiritsa ntchito Mau Oyerawo. Onse amene angayesetse kusunga malamulo a Mulungu adzasekedwa ndi kunyozedwa. Osunga malamulo'wo angaime nji m'chikhulupiriro chao pokhapokhapo atakhala mwa Mulungu. Ndi okhawo amene akhazikitsa moyo wao pa choonadi cha m'Bukhu Lopatulika omwe angadzaime pa chitsautso chachikuru chomwe chiri nkudza. Kodi ife ndife okonzeka kudzaima ndi kutchinjiriza malamulo a Mulungu ndi chikhulupiriro cha Yesu? Chisanafike chiweruzo chotsiriza pa dziko lapansi, padzakhala, pakati pa anthu a Mulungu, chitsitsimutso chomwe sichinachitikepo ndiponso chinachitika nthawi ya atumwi. Mu nthawi imeneyi anthu ambiri adzadzilekanitsa ndi mipingo imene chikondi cha za dziko chatenga malo a chikondi cha Mulungu ndi Mau ake. Mdani wa miyoyo akufunitsitsa ataitsekereza ntchito imeneyi; ndipo nthawi ya utumiki wofunikira'wu itangotsala pang'ono, iye adzayesetsa kuitsekereza pobweretsa machitidwe ngati a chitsitsimutso chiri nkudza'cho. Ku mipingo imene angathe kuiyika pansi pa ulamuliro wake mwa chinyengo chake, iye adzayesetsa kuchita zinthu zoonetsa ngati muli madalitso ndi mphamvu zapadera kuchokera kwa Mulungu. M'matumiki ambiri a zitsitsimutso omwe achitika zaka theka la zana limodzi zapitazi, mphamvu ya chinyengoyi yakhala ikugwiritsidwa ntchito moonjezera, ndi cholinga chofuna kusokoneza chitsitsimutso choona chomwe chiri nkudza ndi utumiki wodzozedwa ndi Mulungu mtsogolomu.

Chikhalidwe ndi kufunikira kwa chilamulo cha Mulungu, zachokeratu m'mitima mwa anthu. Tsopano ndi nthawi yabwino yakufunika kwa mphamvu ya Mzimu wa Mulungu kuti adzetse chitsitsimutso m'nthawi yathu ino. Koma podzachitika ichi Satana wadzawanamizira anthu a Mulungu kuti ndiwo akubweretsa miliri ndi zoipa zonse zomwe zidzakhala zikuchitikira mbali yake. Uyu ndi uja Kumwamba anati amafuna kukhazikitsa boma la mtendere la Mulungu, koma pansi pa mtima akufuna kulanda ulamuliro. Iye anati akuchita zonse monga woimira wa Kumwamba chikhalirecho akungofuna kudzikweza ndi kukhala pamwamba, ndiponso kusintha lamulo la Mulungu. Mulungu samakakamiza chifuniro kapena chisankho cha munthu, - koma Satana pofuna kulamulira iwo amene sangathe kuwasokeretsa – amakakamiza ndi kugwiritsa ntchito nkhanza.

Anthu amene akulilemekeza Sabata la m'Bukhu Lopatulika adzanyozedwa kuti ali adani a lamulo ndi mtendere, kuti ndiwo akusokoneza ndi kudzetsa kusasunga malamulo pakati pa mtundu wa anthu. Chifukwa chakuti a mipingo ya Mpanduko

achikana choonadi chomwe chikanawathandiza pa kutchinjiriza lamulo la Mulungu, adzafunitsitsa ataletsanso anthu onse amene maziko a chikhulupiriro chao ndi Bukhu Lopatulika. Akuluakulu a mipingo ndi aboma adzagwirizana pakuyesetsa kunyengerera, kuumiriza, kapena kukakamiza anthu a mitundu yonse kulilemekeza Sunday. Kusoweka kwa umboni wa mau a Mulungu kuti tsiku'li si la sabata loona kudzapangitsa kuti iwo akhazikitse malamulo ozunza. Ngakhale m'dziko la ufulu la America, anthu olamulira ndi opanga malamulo, pofuna kuti akope chikoka cha anthu onse, adzagonjera kuzofuna za anthu ndi kukhazikitsa lamulo lokakamiza kusunga Sunday.

Mpingo wa Aroma, ndi mabungwe ake onse pa dziko lonse lapansi, udzapanga mgwirizano umodzi waukuru pansi pa ulamuliro, ndiponso ndi cholinga chokwaniritsa, zofuna za utsogoleri wake. Ziwalo za mpingo'wu zonse mosawerengera kuti zachokera ku pfuko liti kaya boma liti, adzapereka mtima wao wonse kumvera ulamuliro wa mpingo wao kuposa kumvera wina ali yense. Magulu onse a za chipembedzo adzakhala atakana Mau a choonadi a Mulungu omwe pa nthawiyo adzakhale asakusamalidwa. Pakukakamira pa ziphunzitso zolakwika zakuti wochimwa sadzafai komanso kuti munthu akafa amaonabe zinthu monga momwe anali moyo, iwo adzakhala atachikana chitchinjirizo chokhacho chomwe chikanawapulumutsa kuchinyengo cha Chipembedzo cha mizimu ya ziwanda.

Monga njira yokhayo yodzipeputsa kuti asachite ichi chomwe anakhala akutsutsana nacho, adzalamulira aphunzitsi ao otchuka kuti adzinka akuphunzitsa kuti lamulo la Mulungu linatha ntchito, choncho palibe chifukwa choligwiritsira ntchito ndi kusunga Sabata. Pamene ntchito yakukonzanso ndi ya chitsitsimutso cha kusunga malamulo ndi la Sabata loona idzanka ikukulirakulira, kukana kwa lamulo la Mulungu pofuna kuthana nalo lamulo lachinai kudzafalikira pa dziko lonse. Kudzera m'ziphunzitso zoipitsitsa zikuruzikuru ziwiri zomwe ndi zakuti munthu wochimwa sadzafai ndi kupatulika kwa Sunday, Satana adzaika anthu pansi pa chinyengo chake. Pamene chiphunzitso choyamba chidzayala maziko a Chipembedzo cha Mizimu, chachiwirichi chidzagwirizanitsa zipembedzo zonse ndi mpingo wa Aroma.

Aphunzitsi ambiri a za chipembedzo amati mwa imfa yake Khristu anathetsa malamulo, choncho anthu sayeneranso kumvera, kusunga ndi kuchita zomwe malamulo'wo akunena. Koma umu si momwe anazionera zinthu aneneri ndi atumwi pakunena za chiyero cha lamulo la Mulungu. Zaka theka la zana limodzi kuchokera pomwe anapachikidwa Khristu, Yohane anapereka madalitso kwa iwo "akusunga malamulo a Mulungu ndi chikhulupiriro cha Yesu, kuti akakhale nao ulamuliro pa mtengo wa moyo, ndi kuti akalowe m'mzinda pazipata." *Chibv. 22:14.* Kukanakhala kuti kunali kotheka kuti lamulo lidzisinthasintha kapena kuliika pambali nthawi zina, Khristu sakanadza kudzamfera munthu ndi kumpulumutsa kuchilango chakuliswa lamulo'lo. Choncho imfa ya Khristu, kuonjezera pakuti sinali kudzathetsa lamulo, iri umboni kuti lamulo'lo silidzasintha ndi pang'ono pomwe, ndi la myaya.

Khwerero loyamba munthu akafuna kuyanjanitsidwanso ndi Mulungu limakhala kutsutsika ku tchimo. "Tchimo ndilo kulakwira lamulo." Ndipo "uchimo udziwika ndi lamulo." *1 Yohane 3:4; Aroma 3:20.* Lamulo limamuonetsa munthu za tchimo lake, koma silimapulumutsa. Ndi uthenga wa Khristu wokha womwe ungathe kumpulumutsa munthu kuchilango ndi chibvundi cha tchimo. Iye ayenera kulapa pamaso pa Mulungu, amene ndi mwini lamulo lomwe munthuyo amaliswa ndipo Khristu ndiye nsembe yakutsuka tchimo. Ndi momwe zanenedwera za lamulo'mu, kodi munthu ali ndi ufulu wakumangoliswa? "Potero kodi lamulo tiyesa chabe mwa chikhulupiriro? Musatero ai; koma tikhazikitsa lamulo." "Pakuti ichi ndi chikondi cha Mulungu, kuti tisunge malamulo ake." *Aroma 3:31; 1 Yohane 5:3.* Tsono popeza Chipembedzo cha Satana chikuyesetsa kutsanzira machitidwe a Chikhristu chofooka a lero, chiri ndi mphamvu yaikuru yoti nkunyenga ndi kusokeretsa anthu osawerengeka. Kudzera mu Chipembedzo cha Satana'chi, zozizwa zidzachitika, odwala adzachiritsidwa, ndipo zozizwa zooneka ndi maso zidzachitidwa. Kudzera m'Chipembedzo cha Ziwanda chomwecho, Satana akudzizimbaitsa ngati mthandizi wa anthu opsyinjika, pamene pa nthawi yokhayokhayo akuwasokoneza iwo.

"Ndipo umodzi wa mitu yake unakhala ngati walasidwa kufikira imfa; ndipo bala lake la kuimfa lidapola." *Chibv. 13:3.* Kukhala ndi bala la kuimfa kukuimira kuthetsedwa kwa ulamuliro wa upapa m'chaka cha 1798. Paulo akufotokoza momveka bwino kuti munthu wa kusayeruzikayu adzakhalako kufikira kudza kwachiwiri kwa Ambuye (2 Ates. 2:8). Pafupifupi penipeni pa mathedwe a nthawi, iye adzayambanso ntchito yake yakusokeretsa. M'maiko onse awiri, Dziko Lakale ndi Dziko Latsopano, upapa udzalemekezedwanso kudzera pakulilemekeza Sunday. "Zitatha izi ndinaona mngelo wina wakutsika m'Mwamba wakukhala nao ulamuliro waukuru; ndipo dziko linaunikidwa ndi ulemelero wake. Ndipo anapfuula ndi mau olimba ... Turukani m'menemo, anthu anga; kuti mungayanjane ndi machimo ake, ndi kuti mungalandireko ya miliri yake." *Chibv. 18:4.* Chipembedzo chonyansitsitsa cha dziko lapansi chikufotokozedwa m'mau awa. Pakukanitsitsa choonadi maganizo a anthu adzaipa kwambiri, mitima yao idzakakala kufikira pakuti sangathenso kubwerera m'mbuyo. Pamene ziphunzitso za ziwanda zidzakhala zikubvomerezedwa ndi mipingo yonse, kudziletsa kudzauchokera mtima wa munthu. Kukhulupirira machitidwe a ziwanda kudzatsegula chitseko cha ziphunzitso za mizimu ya udierekezi. Za Babulo (Chisokonekero) Bukhu Lopatulika likuti, "Machimo ake anaunjikizana kufikira m'Mwamba, ndipo Mulungu anakumbuka zosalungama zake." *Chibv. 18:5.*

Mulungu ali ndi anthu ake m'Chisokonekero chimenechi; koma chiweruzo chake chisanachitike, okhulupirira oona mtima'wa ayenera kukhala ataitanidwa kuturuka m'menemo. Kuitanidwa kumeneku kuphatikiza kwa uthenga wa mngelo wachitatu, kuli chenjezo lotsiriza lomwe liperekedwe kwa anthu onse okhala pa dziko lapansi. Mphamvu za dziko lapansi, pogwirizana kuchita nkhondo molimbana ndi malamulo a Mulungu, zidzalamulira kuti onse, "ang'ono ndi akuru, achuma ndi osauka, ndi mfulu ndi akapolo," *Chibv. 13:16,* abvomereze miyambo ya mpingo pakulemekeza Sunday, sabata la bodza. Monga momwe chiphunzitsochi chikumvekera bwino'mu, munthu ali yense amene angapitirize kuswa malamulo a Mulungu, ndi kulemekeza malamulo opangidwa ndi munthu, ndiye kuti akuchitira dala, ndipo woteroyo akulandira lemba la chirombo. Pamene chiyeso chotsiriza chidzafika pa anthu onse, pomwepo padzakhala kulekanitsa pakati pa iwo akutumikira Mulungu ndi osamtumikira Iye. Pamene gulu limodzi, lidzabvomereza kumvera ulamuliro wa dziko lapansi lidzalandira lemba la chirombo, gulu lina, posankha kumvera ulamuliro wa Mulungu,lidzalandira chizindikilo cha Mulungu.

## 17. Kusankha Khristu ndi Moyo Wosatha

Pamene uthenga wa mngelo wachitatu udzatsekedwa, sipadzakhalanso mwai wakupembedzera anthu ochimwa a dziko lapansi. Anthu a Mulungu adzakhala atatsiriza ntchito yao. *Danieli 12:1.* Mngelo pakubwerako kuchokera ku dziko lapansi adzapfuula kuti ntchito yake yachitika, apo chiyeso chotsiriza cha dziko lapansi chidzakhala chitachitika, ndipo onse amene anatsimikizika kusunga malamulo a Mulungu atalandira, "chizindikilo cha Mulungu wamoyo."

Pomwepo Yesu adzasiya ntchito yake yakutetezera m'kachisi wakumwamba. Iye adzakweza manja ake, ndipo ndi mau akupfuula adzanena. "Chachitika." *Chibv. 22:11.* Mlandu wa munthu ali yense udzakhala utaweruzidwa kuloza ku moyo kapena ku imfa. Yesu adzakhala atachita ntchito yakutetezera anthu ake, ndi kufufuta machimo ao. Chiwerengero cha anthu ake chidzakhala chitatsimikizika.

Pamene Iye adzaturuka m'kachisi, mdima udzakutira anthu okhala pa dziko. Mu nthawi yoopsyetsetsayi olungama adzakhala pamaso pa Mulungu opanda wowapembedzera.

Kudziletsa komwe oipa anali nako kudzachokeratu, ndipo Satana adzadzitengera ulamuliro wonse m'manja mwake. Machimo a osalungama adzasefukira. Pomwepo Satana adzawasonkhanitsa onse okhala pa dziko ndi kulowa nao m'chisautso chachikuru chomwe chidzakhalanso chotsiriza. Dziko lonse lapansi lidzakhuzidwa ndi chiononngeko choopsya choposa chija chinachitikira Yerusalemu wa kale.



Ndipo Sabata loona lidzakhala chinthu chomwe akhristu onse adzakhala akukanganira, ndipo akuluakulu a chipembedzo ndi a dziko adzalumikizana ndi kukakamiza kulilemekeza Sunday, koma kagulu kochepa kadzakanitsitsa kudetsa chikhulupiriro chao posalemekeza Sunday'lo, ndipo kadzadedwa ndi onse.

Pamene Khristu adzatsiriza ntchito yake yakutetezera mu kachisi wa Kumwamba, mkwiyo wosasakaniza wa mkwiyo wa Mulungu udzaonekera motsutsana ndi anthu akupembedza chirombo ndi fano ndi kulandira lemba, ndipo udzatsanulidwa pa iwo. Iyi idzakhala miliri yomwe sidzakhuza dziko lonse lapansi, kapena kuti anthu onse okhala pa nkhope ya dziko. Komabe idzakhala chinthu chowawitsitsa chimene sichinayambe chachitikapo pa mtundu wa anthu chilengedwere cha dziko lapansi. *Chibv. 14:9, 10.*

Pamene chitchinjirizo cha malamulo a dziko chidzachotsedwa pa anthu osunga lamulo la Mulungu, padzakhala, mgwirizano womwe cholinga chake chidzakhale chakuononga olungama m'maiko osiyanasiyana. Pamene nthawi yakukwaniritsidwa kwa lamulo loperekedwa'lo idzangotsala pang'ono kufika pa mapeto, usiku umenewo anthu oipa adzagwirizana kupha ndi kukachotseratu kagulu kodedwako.

Nthawi yomweyo padzaonekera kum'mawa kamtambo kakang'ono kakuda, kukula kwake ngati dzanja la munthu. Uwu ndi mtambo umene udzamzungulira Mpulumutsi. Anthu a Mulungu adzauzindikira kuti uli chizindikilo cha Mwana wa munthu. Modekha mtima komwe sanachitikepo, adzauyang'anitsitsa ukutsika kuyandikira dziko lapansi, pofika pafupi udzawala ndi ulemelero waukuru. Ndipo angelo oyera, ochurukitsa, osawerengeka ngati mchenga, akumtumikira m'njira yake adzaimba nyimbo mwa luso. Mlengalenga udzadzazidwa ndi kuwala kwa maonekedwe ngati utawaleza *Chibv. 19:11, 14.*

Pamene mtambo udzidzayandikira pa dziko, diso liri lonse lidzamuona Kalonga wa Moyo. Pamutu pake padzakhala palibe korona wa minga woipitsa nkhope yake, koma nduwira ya ulemelero yofikira pa zikope za nkhope yake yonyezimira. *Chibv. 19:16.* Pamaso pake "nkhope za anthu onse zidzaoneka zotumbuluka," ndipo mantha akuru ndi kukhumudwa zidzakhala pa anthu amene anachikana chifundo cha Mulungu. *Yeremiya 30:6; Nahum 2:10.* Ndipo

olungama adzapfuula mwa mantha, "Akhoza kuima ndani?" Pomwepo mau a Yesu adzamveka, "Chisomo changa chikukwanira."

Dziko liri mkudzandima, mphenzi zikung'anima, mabingu akugunda, mau a Mwana wa Mulungu adzaitana oyera anagona mpfumbi. Kuyambira mulitari ndi mulifupi la dziko lapansi, akufa adzamva mau'wo; ndipo iwo adzauka. *1 Akorinto 15:55.* Ndipo oyera a moyo ndi olungama oukitsidwa pamodzi adzakweza mau ao kuimba nyimbo yaitali, yachisangalalo ndi yachigonjetso.

Olungama anafa'wo adzauka ndi matupi a thanzi okhala ngati achinyamata. Olungama a moyo adzasinthika, "m'kutwanima kwa diso." Pakumvera mau a Mulungu analandira chiyembekezo cha ulemelero, koma tsopano alandira moyo wosatha, ndipo pamodzi ndi oyera oukitsidwa adzakwatulidwa kukomana ndi Ambuye wao mu mlengalenga. Ana ang'ono adzanyamulidwa ndi angelo oyera ndi kuperekedwa m'manja mwa amai ao. Abwenzi amene analekana chifukwa cha imfa adzalumikizananso.

Chinsinsi cha kulora imfa ya pa mtanda chidzaika poyera zinsinsi zonse zobisika. Ndi kuunika kochokera ku Gologotha, machitidwe a Mulungu omwe adzatidzadza ndi mantha ndi kuthedwa nzeru adzaoneka kukhala okoma, ochititsa chidwi ndi opatsa chiyembekezo. Chifundo, kukoma mtima ndi chikondi cha umulungu zidzaonetsedwa zomangika pamodzi m'chiyero, chilungamo ndi mphamvu.

Apatu zidzatsimikizika kotheratu kuti Iye amene ndi Wodzala ndi luntha sanapatsa ndondomeko ina ya chipulumutso koma nsembe ya Mwana Wake. Ndipo cholinga cha nsembe imeneyi chinali chimwemwe chakudzalidzadza dziko lapansi ndi anthu opulumutsidwa, oyera, okondwa omwe sadzafanso. Uwu ndiwo mtengo wake wa moyo wathu umene Mulungu amakhutitsidwa nao, umene Iye anaupereka kukhala dipo; ndipo Khristu mwini wake, adzaona zipatso za nsembe yake yaikuru, nakhutitsidwanso.

Abusa ndi anthu owatsatira adzaturukira za kutaika ndi m'chiyanjano kwao ndi Mulungu. Adzaturukira kuti anaukira motsutsana ndi Iye amene ali chiyambi cha chilungamo ndiponso lamulo loyera. Palibe mau omwe angathe kufotokoza za kuwawa komwe anthu osalungama ndi osayanjanitsika adzakumve pa chimene anachitaya kwa myaya, - moyo wosatha. Akulingirira za chomwe anachitayacho chifukwa cha kusayeruzika kwao, adzadza nadzigwetsa pa mapazi amene anawanyoza ndi kupondereza chikhupiliriro chao, ndikubvomereza kuti Mulungu anawakonda anthu akewo.

Anthu adzaturukira kuti anasokeretsedwa. Adzalozana chala wina ndi mnzake kuti anatsogolerana kuchitaiko; kenaka onse adzagwirizana chimodzi adzakuika kuwawidwa mtima kwao pa abusa ao. Malupanga amene amati aphere anthu a Mulungu adzagwiritsidwa ntchito kuphera atsogoleri anawasokeretsawo. Kukhetsa mwazi kwakukuru kudzachitika pa dziko lonse.

Kwa zaka zikwi zisanu ndi chimodzi mkangano waukuru wakhala ukuchitika; Mwana wa Mulungu ndi atumiki ake wakhala akulimbana ndi mphamvu ya woipayo ndi atumiki ake, pakuchenjeza, kuunikira ndi kupulumutsa ana a anthu. Ndipo pano munthu ali yense ayenera kupanga chisankho chake. Nthawi yakwana yakuti Mulungu aonetse chilungamo cha mphamvu ya lamulo lake lomwe lakhala likuponderezedwa. Pa nthawiyi mkangano sudzakhala ndi Satana yekha, komanso ndi anthu ake. Mkati mwakuzunguzidwa mitu ndi chilakolako chao chosaletseka pa zoipa, ndi kudzatsanulidwa kwa mkwiyo wa Mulungu wopanda chifundo, adzaphedwa anthu oipa a dziko lapansi. *Yeremiya 25:33.*

Pakubwera kwa Khristu oipa adzathawa kuchoka pa nkhope ya dziko lonse lapansi – adzathedwa ndi mzimu wa pakamwa pake, ndikuonongedwa ndi maonekedwe akuwala kwa ulemelero wake. Khristu adzawatenga anthu ake kulowa nao mu mzinda wa Mulungu, ndipo dziko lidzakhala lopanda okhalamo ake. Dziko lonse lidzakhala ngati chipululu chopanda kanthu.

Yohane ananenera za kuponyedwa kwa Satana m'ndende yake, yomwe idzakhala iri makhalidwe ndi maonekedwe osokonekera ndi a chipululu a dziko lapansi pa nthawiyo; omwe akufotokozedwa kuti adzakhala kwa zaka chikwi chimodzi. Dziko lotere, logumukagumuka ndi loonongeka, ndilo lidzakhala kwao kwa Satana ndi angelo ake kwa zaka chikwi. Womangidwa ku ndende ya dziko lapansi, sadzatha iye kukhala ndi mwai wakuyendera maiko ena, kuti akayesenso kunyenga iwo amene sanachimwepo. Ichi ndi chomwe mau akuti adzamangidwa m'ndende yake akutanthauza; palibe wa moyo wina ali yense amene iye angadzayeserepo mphamvu zake. Sadzatha iye kuwanyenga ngakhale osalungama, adzakhala iwonso atafa, nakhala ku malo komwe mphamvu yake singadzathe kuwafikira. *Chibv. 20:1-3.*

Kwa zaka chikwi chimodzi, Satana adzakhala akuyendayenda uku ndi uku m'chipululu chopanda munthu ali yense cha dziko lapansi, kunka akuona zotsatira za kuukira lamulo la Mulungu komwe wanakuchita. Mu nthawi imeneyi adzakhala wakubvutika kosaneneka. Koma kwa anthu a Mulungu undende wa Satana udzadzetsa chimwemwe ndi kukondwera.

Mkati mwa nthawi ya zaka chikwi, - pakati pa mdzukiro woyamba ndi mdzukiro wachiwiri, chiweruzo cha osalungama chidzachitika. Pa nthawi imeneyi olungama adzachita ufumu monga mafumu ndi ansembe a Mulungu. Satana pamodzi ndi angelo ake adzaweruzidwa ndi Khristu ndi anthu ake. *1 Akor. 4:5; Dan. 7:22; 1 Akor. 6:3; Chibv. 20:4-6.* Podzatsekedwa kwa zaka chikwi, Khristu adzabweranso ku dziko lapansi. Iye adzadza ndi khamu la opulumutsidwa, ndi gulu lalikuru la angelo. Ndipo pamene adzidzabwera kachiwirika adzatero ali mu ulemelero waukuru, pomwepo adzaitana osalungama anafawo kuti auke kudzalandira chilango chao. Iwo adzaukadi, gulu lalikuru, ndi osawerengeka ngati mchenga wa mbali mwa nyanja. Diso liri lonse la m'gulu limene'li lidzatembenuka ndi kuuona ulemelero wa Mwana wa Mulungu. Iwo sadzapatsidwanso mwai wina wa chitetezero kuti akonzetserenso zolakwa zimene anazichita pamene anali moyo. Adzakhala alibenso chiyembekezo china chiri chonse.

Khristu adzatsika naponda pa phiri la Azitona, pomwenso pambuyo pakuuka kwake anakwerera pakupita Kumwamba. "Ndi mapazi ake adzaponda tsiku lomwelo pa phiri la Azitona, liri pandunji pa Yerusalemu kum'mawa, ndi phiri la Azitona lidzang'ambika ... ndipo padzakhala chigwa chachikuru ..." *Zakariya 14:4.* Pamenepo Yerusalemu Watsopano, m'kunyezimira kwa ulemelero wake, adzatsika pansi kuchokera Kumwamba, adzafikira pa malo oyeretsedwa ndi okonzedwa bwino kumlandira iye, pomwepo Khristu ndi anthu ndiponso angelo adzalowa mu mzinda woyerawo.

Pa nthawi imeneyi Satana adzakhala akukonzekera kudzamenya nkhondo yotsiriza kuti adzalande ulamuliro. Anthu osalungama akadzangooukitsidwa adzakhala ali pansi pa ukapolo wake. Pomkana Khristu iwo analora ulamuliro wa mtsogoleri woukirayu. Iwo adzamvera malingaliro ake ndi kuchita za ku mtima kwake. Monga mwa chikhalidwe ndi machenjerero ake, mpaka pano mdierekezi sakubvomereza kuti ali Satana. Pa nthawi iyonso adzachita zozizwa zoyesetsa kutsimikizira kuti sali mdierekezi. Adzagwiritsa ntchito mzimu wa mphamvu za kuukira kwake, nalimbikitsa ofooka, ndi kupatsanso chiyembekezo kwa ena onse. Pakati pa makamu a anthu oukitsidwawo padzakhala unyinji wa anthu amene anakhala moyo chisanachitike chigumula; amuna a atali misinkhu ndi a nzeru zochuruka. Padzakhalanso mafumu ndi ngwazi za nkhondo amene anagonjetsa amitundu, akatswiri omwe sanayambe agonjetsedwapo ku nkhondo.

Pamene iwo adzauka m'manda, adzayambanso kuganiza kuyambira pamene unalekezera moyo wao. Iwo adzakhalanso ndi chilakolako monga anali nacho pachiyambi chakufuna kumenyana ndi kugonjetsa iwo amene anawalamulira asanafe. Satana adzakambirana ndi angelo ake, ndiponso ndi mafumu ndi anthu ogonjetsa, ndi amuna a akuru awa. Iwo adzagwirizana zakuti akalande ndi kutenga chuma ndi ulumelero wa Yerusalemu Watsopano. Nthawi yomweyo onse adzanyamuka kukachita nkhondo. Kenaka Satana adzalamulira awa kuti apite chitsogolo, ndipo khamu losawerengeka'lo lidzaterodi, - gulu la a nkhondo limene silinayambe lakhalako ndi kutsogoleredwa ndi ngwazi zogonjetsa za dziko lapansi. Adzanka akuguba, anthu a maudindo osiyanasiyana'wa, adzayenda pa nkhope yokumbikakumbika ya dziko lapansi kupita ku Mzinda wa Mulungu. Koma molamulidwa ndi Yesu, zitseko za zipata za Yerusalemu zidzatsekedwa, ndipo asilikari a Satana adzauzungulira mzindawo, ndi kukonzekera kuulanda.

Kachiwiri tsopano, Khristu adzaonekeranso pamaso pa adani ake. Chapatali pamwamba pa maziko a golide woyengeka, padzakhala mpando wachifumu, uli pamwamba ndi wotukuridwira m'mwamba. Kuwala kwa maonekedwe ake kuzaudzadza mzinda wa Mulungu, ndi kufalikira kudutsa zitseko za linga, kufikira kudziko lonse lapansi. Pafupi penipeni ndi mpando wachifumu padzakhala iwo amene modzazidwa ndi choonadi analimbana ndi machenjerero a Satana. Pamenepo opulumutsidwa adzakweza mau kuimba nyimbo ya matamando yomwe idzamveka kumabwalo onse akumwamba ndipo angelo ndi aserafi naonso adzaimba nao limodzi m'mau akuyamika. Pagulu loyera'lo padzakhala palibe munthu ndi m'modzi yemwe wodzitamandira kuti anadzipulumutsa yekha. *Chibv. 7:9.*

Pamaso pa makamu onse okhala pa dziko lapansi ndi Kumwamba Mwana wa Mulungu adzabvekedwa ufumu kotsiriza. Pamenepo Iye adzapatsidwa ulemu ndi ulemelero ndi ukuru, zakukhala, Ambuye wa ambuye ndi Mfumu ya mafumu, kutsimikizira za chilungamo cha chiweruzo cha Mulungu pa onse amene anamuukira Iye. *Chibv. 20:11, 12.*

"Ndipo ndinaona akufa a ang'ono ndi akuru alinkuima ku mpando wachifumu; ndipo mabuku anatsegulidwa; ndipo bukhu lina linatsegulidwa, ndilo la moyo; ndipo akufa anaweruzidwa mwa zolembedwa m'mabuku, monga mwa ntchito zao." Pamene mabuku a zolembedwa adzatsegulidwa, diso la Yesu lidzayang'ana maina a osalungama, ndipo osalungama eni ake naonso adzakumbukira tchimo liri lonse limene analichita. Adzakumbukira pamene mapazi ao anapambukira kusiya njira ya chiyero ndi ya chilungamo, ndipo monga zimachitikira pa kanema wa zithunzi kuyesedwa ndi kuchimwa kwa Adamu kudzaonetsedwa, kenaka tsatanetsatane wa ndondomeko yaikuru ya chipulumutso chamunthu.

Ndipo ku gulu looneka lotangwanika'lo (osalungama) kudzaonetsedwa zochitika zotsiriza – kudzaonetsedwanso za kuzunzika mwakachetechete kwa Iye amene anayenda pa njira ya ku Gologotha; Kalonga wa Kumwamba atapachikidwa pa mtanda. Chinthu chonyansitsitsa chomwe chinatika monga momwe chinayenerera. Satana, angelo, ndi anthu ake adzakhala alibe mwai woti nkuchibwezera m'mbuyo choipa anachichitacho, izi zidzakhala chitsimikizo cha ntchito yao yoipa. Khumu lonse la anthu osalungama lidzaima pa muyeso wakuweruza wa Mulungu, pa mlandu wao wakuukira boma la Kumwamba. Apa ndipo zidzatsimikizike tsono kwa onse kuti



*Kulumikizananso Kwa Banja Kumwamba*

# DZIKO LOGARUKIRA MULUNGU

mphotho yake ya tchimo sikukhala moyo wodzilamulira kapena moyo wosatha monga Satana ankanamira, koma ukapolo, kuonongeka ndi imfa. Osalungama adzauyang'ana ulemelero umene anautaya, nadzadzimvera chisoni chachikuru.

Onse adzatsimikizira kuti kusalandirika kwao Kumwamba ndi chinthu chowayenera. Ngati kutulo, osalungama adzachitira umboni kukhazikitsidwa Mfumu kwa Mwana wa Mulungu. Adzaona m'manja mwake magome a miyala ya malamulo, ndiponso maweruzo amene anawanyoza ndi kuwakana. Adzachitira umboni za kuimba, chisangalalo, ndi chilemekezo zochokera kwa opulumutsidwa. Satana adzaoneka wa manyazi ndi wozizidwa thupi pakuona ulemelero ndi ukuru wa Khristu. Iye amene anakhalapo kerubi wakuphimba adzakumbukira pomwe wanagwera. M'maganizo mwake adzakumbukira malo amene anakhalapo kwao m'nthawi yomwe anali woyera ndi wangwiro, ndiponso mtendere ndi chimwemwe zomwe zinali zake kufikira pa nthawi imene munapezeka mu mtima mwake khalidwe la kung'ung'uza motsutsana ndi Mulungu ndi lomchitira nsanje Khristu. Adzakumbukiranso upandu wake umene anauchita pa ntchito ya Khristu, ndi kuulowetseralowetsera kwake pansi mtundu wa anthu. Iye adzatsimikiza kuti machitidwe ake a usatana anali opanda mphamvu yakuwaononga anthu amene chikhulupiriro chao chinali mwa Yesu. Cholinga cha mngelo woukira wamkuruyu chakhala chiri kudziyenereza, ndi kudzitamandira za kuti ndi iyedi amene anayambitsa kuukira boma la Kumwamba.

Iwo amene analumikizana naye adzatsimikizira za kulephera kwa Satana ndi za kuipa komwe anakuyambitsa. Anthu omtsatira Khristu ndi angelo omvera adzatsimikizira za chomwe chinali cholinga chenicheni cha Satana pakuukira boma la Mulungu. Pa nthawiyo Satana wadzakhala atasandulikadi choopsya kuti onse amuone. Ndipo iye adzatsimikiza kuti kuukira kwake kochita kukupanga mofunako kwampangitsa kusayenera kukhala nzika ya Kumwamba. Ndipo pomwepo Satana adzapinda maondo ake kugwada pansi, ndi kubvomereza chilungamo chomwe chidzaperekedwa pa chiweruzo chake. Funso liri lonse lokhuza choonadi ndi kusayeruzika komwe kwakhala kukuchitika kwa nthawi yaitali m'mkanganowu lidzayankhidwa mombveka bwino. Zotsatira za kuukira, zipatso za kunyalanyaza maweruzo a Mulungu, zidzaikidwa poyera kwa olengedwa onse kuti aone. *Mas. 145:10.*

Mbiri ya tchimo idzakhala umboni wakuti kukhala m'malamulo ndi mau a Mulungu muli chimwemwe cha onse omwe Iye anawalenga ku nthawi zonse. Ndipo uchokera maumboni onse a Mkangano awaukuru'wu, chilengedwe chonse kuphatikiza anthu olungama ndi ochimwa, ndi mtima umodzi chidzanena, "Njira zanu nzolungama ndi zoona Mfumu Inu ya oyera mtima." Ora lafika pamene Khristu ayenera kukhala pa mpando womuyenera Iye, ndi kulemekezedwa kuposa maukuru ndi maulamuliro ndi mphamvu ndiponso dzina liri lonse lingatchulidwe'lo.

Ndipo ndi mau akupfuula Iye adzalankhula kwa magulu a misonkhano ya aunyinji ya onse'wo, olungama ndi osalungama, "Taonani, iwo ogulidwa ndi mwazi wanga! Chifukwa cha awa ndinazunzidwa; chifukwa cha awa ndinaphedwa; kuti iwo athe kukhala pamaso panga ku nthawi zonse."

Likudza tsiku, lotentha ngati ng'anjo. Za m'mwamba zidzakanganuka ndi kutentha kwakukuru, ndipo dziko ndi ntchito ziri momwemo zidzatenthedwa. Pakuti liri tsiku lakubwezera la Yehova, chaka cha kubwezera chilango. Nkhope ya dziko lapansi ikhala ngati nyanja ya thope losungunuka – idzakhala ngati nyanja yaikuru yotentha moto. Iyi idzakhala nthawi ya chiweruzo ndi chilango cha anthu osaopa Mulungu. Ena adzaonongedwa m'kanthawi kochepa, pamene ena adzabvutika kwa masiku ochuruka. Ali yense adzalangidwa "monga mwa ntchito zake." *Malaki 4:1; 2 pet. 3:10; Yes. 34:8; Miy. 11:31.*

Machimo a olungama ataikidwa pa Satana, iye adzabvutika osati chifukwa cha kuukira kwake kokha, koma chifukwa cha machimo onse amene anawapangitsa anthu a Mulungu kuwachita. Potsirizira osalungama onse adzaonongedwa pakuponyedwa m'nyanja ya malawi a moto, kuyambira ndi muzu kufikira nthambi, - Satana ndiye muzu, omtsatira ake nthambi. Pamene dziko lapansi lidzakhala litakutilidwa m'moto wakuononga, olungama adzakhala mokondwa mu mzinda woyera. Pa onse amene adzadzuka nao pa mdzukilo woyamba, imfa ya chiwiri iribe ulamuliro pa iwo. *Chibv. 20:6' Mas. 84:11.*

"Ndipo ndinaona m'mwamba mwatsopano ndi dziko latsopano; pakuti m'mwamba moyamba ndi dziko loyamba zidachoka. *Chibv. 21:1.* Moto umene udzanyeketsa osalungama udzayeretsa dziko lapansi. Pachiyambi dziko lapansi linapatsidwa kwa munthu kukhala mochitiramo ufumu wake, koma munthuyo analipereka ili m'manja mwa Satana, ndipo ngakhale pano liri mochitiramo ufumu wa mdaniyu, linayanjanitsidwanso ndi Mulungu mwa nzeru yaikuru ya chipulumutso. *Yes. 45:18.* Cholinga cha Mulungu polilenga dziko chinali chakuti likhale cholowa cha myaya kwa opulumutsidwa. *Mas. 37:29.* Pakupewa kufotokoza momveka bwino kuti dziko liri nkudza ndi lenileni monga liri la lero'li zatsogolera anthu ambiri kuliona ilo ngati ndi la uzimu komwe kuli kutsutsana ndi choonadi za kwathu'ko. *1 Akor. 2:9.*

Chilankhulo cha umunthu nchosakwanira kuifotokoza momveka bwino mphotho ya olungama. Idzadziwika bwino kwa omwe adzailandire. *Ahebri 11:14-16.* Kumeneko kuli mitsinje yosaphwa, ya madzi oyera ngati mwala wa krustulo, m'mbali mwa mitsinjeyo muli mitengo yomwe nthambi zake zidzachitira mthunzi m'njira zomwe olungama a Ambuye adzidzayendamo. M'zigwa za see muli zitunda zokongola, ndipo nsonga za mapiri a Mulungu zizaonekera pamwamba. Pa zigwa zokongola zimenezi, m'mbali mwa mtsinje wa moyo, anthu a Mulungu, amene adzakhala ngati anthu akuyendera maulendo atari a za chipembedzo, adzapumulirako, ndipo dziko'lo lidzakhala kwao. *Yes. 32:18; 60:18; 65:21,22.*

Sikudzakhala chowawitsa chiri chonse m'dziko latsopano. Sikudzakhalanso kulira maliro. *Chibv. 21:4,11,24,3; Yes. 11:6,9; 33:24; 62:3; 65:19.*

Yerusalemu Watsopano, mzinda wa dziko latsopano wodzala ndi ulemelero udzatsika. "Sipadzafunika dzuwa" Palibe munthu adzakulakalaka kuwala kwa dzuwa m'mzinda wa Mulungu'wu. Sipadzakhala kutopa pakuchita chifuniro cha Mulungu ndi kuyamika dzina lake. Tidzakondwera m'kukoma ndi m'mtendere za m'dziko'lo, ndipo sitidzatopa kukhala m'menemo ku nthawi zonse. Chibv. 22:5; 21:22.

Anthu a Mulungu adzakondwera kukhala pamodzi ndi Atate ndiponso Mwana. Adzakondwera kukhala mu msonkhano wa oyera ndi olungama onse, kusakanikira limodzi ndi angelo ndiponso okhulupirira a mibadwo yonse. Aefeso 3:15. M'maganizo mwao adzalingirira ndi kukondwera za mphamvu yosalephera ya kulenga, ndi za chikondi cha kupulumutsa. Kumeneko zolakalaka za mtima zidzakwanitsidwa, chiri chonse chomwe munthu adzachita adzapindula nacho, ndipo zofuna za moyo zidzafitsidwa; kudzakhala kuphunzira zinthu zatsopano ndi kuchita chidwi ndi zomwe moyo sunazionepo.

Chuma ndi ulemelero wa chilengedwe chonse zidzaperekedwa kuchidziwitso cha opulumutsidwa a Mulungu kuti azindikiremo m'menemo. Pokhala ndi matupi aulemelero, iwo sadzatopa kuuluka kuchoka ndiponso kupita ku maiko apafupi ndi akutali. Ndi maso ao osadetsedwa ndi tchimo iwo adzauona ulemelero wa chilengedwe, madzuwa angapo, nyenyezi ndi mayendedwe ao, zikuyenda m'njira zao mozungulira mpando wachifumu wa Mulungu monga mwa chilongosoko cha makhazikitsidwe ao.

Ndipo pamene zaka zakukhala kwao myaya kumeneko zidzidzanka zikupitirira, olungama adzakhala akuturukira mabvumbulutso ambiri a ukuru ndi ulemelero wa Mulungu ndi wa Khristu. Pamene chidziwitso chao chidzanka chikukulirakulira, chikondi ndi chilemekezo chao zidzakhala zikuonjezekeraonjezekera, ndiponso chimwemwe chao kunka chichurukirachurukira. *Chibv. 5:13.* Mkangano waukuru'wu ufika pakutha. Tchimo ndi ochimwa onse sadzapezekanso. Chilengedwe chonse chidzakhala changwiro ndi choyera. Chikondi ndi umodzi zidzakhala pa chilengedwe chonse. Kwa Iye amene analenga zinthu zonse kudzachokera moyo ndi kuunika ndi chimwemwe, zomwe zidzafalikira kumiyamba yonse kuphaitikiza ya za m'mwamba. Kuchokera ku kanthu kochepetsetsa kosaoneka ndi maso kufikira ku dziko lalikuru'li, *zinthu zonse za moyo ndi zopanda moyo mu kukongola ndi ungwiro wao wodzala ndi chimwemwe zidzaonetsera kuti Mulungu ndiye chikondi.*


**MUKAFUNA KUMVA NDI KUDZIWA ZAMBIRI LEMBERANI KU:**

**Loud Cry and Family Life Ministries**
**P.O. Box 2850,**
**Blantyre,**
**Malawi. Central Africa.**

**Restoration Seventhday Adventist Ministries**
**P. O. Box 510751,**
**Chipata,**
**Zambia. Central Africa.**

**Advent Prophecy Update**
**P.O. Box 70516,**
**Ndola,**
**Zambia, Central Africa.**